
Ufumu wake unaimitsidwa.
Koma akudzautenganso.

# Mfumu ya Ulemelero



Kuchokera
Mumalembo Oyera
Yofotokozedwa ndi
P.D. Bramsen

Ojambula zithunzi
Arminda San Martín

ROCK International

**Mfumu ya Ulemelero**
Mlembi: P. D. Bramsen
Mkozi wa zithunzi: Arminda San Martín
KING of GLORY translated in chiChewa
Copyright © 2017 ROCK International. All rights reserved.

ISBN 978-99908-86-12-2

Losindikizidwa ROCK International
- **Chithandizo, Mwayi ndi chisamaliro cha ana**
- **Zothandizira zodziwa zoyenera**

P.O. Box 4766, Greenville, SC 29608
www.rockintl.org resources@rockintl.org
www.king-of-glory.com

Pomasulira buku ili tagwiritsanso Baibulo la Chichewa 'BUKU LOPATULIKA'.

Nkonzi wa mutu wa buku Dave Bramsen

Lotanthauziridwa ndi Mthenga Wabwino, PO Box 3151 Blantyre, Malawi

Chithunzi cha kanema Zarief Mina
Chithunzi cha pa tsamba176, chojambulidwa ndi Cole Phail, mukanema wa "Mfumu Ya Ulemerero"

**Zina zokhudza mlembi:** anabadwira ku California. Iye ndimkazi wake analera ana awo ku Senegal, Kumadzulo kwa Africa—dziko lodzala ndi asilamu ambiri m'musi mwa chipululu cha Sahara. Bramsen amalemba zowerenga anthu amaiko onse, Kukonza zipangizo zonena khani ndi kufotokoza uthenga wa aneneri a m'Baibulo. Analembanso buku mutu wake "*The Way of Righteousness*" (Mumagawo100 ofotokozera pa wailesi, linalembedwa mu chilakhulo cha chi Wolof ku Senegal, tsopano muzilakhulo zoposera 100), "*One God One Message*" (Buku lolembedwa ndicholinga chofuna kuthandiza anthu okayikira ofuna kumvetsa choonadi cha Baibulo.Buku ndi kanema wa Mfumu ya Ulemelero (yamphindi 222-yochititsa chidwi ndikufotokozera bwino ulendo wa mu malemba a aneneri) Lemberani: **pdbramsen@rockintl.org**


**Zokhudza wojambula zithunzi:** Arminda San Martín wa ku Argentina analemba: "Ndikakumbukira bwino ndinayamba kujambula zithunzi kale. Kenaka ndinalekeza nditakwatiwa komanso kumasamalira ana anga, ndinayambiranso ntchito yanga polandira degree ya ukadaulo wojambula zithunzi.
Ndinagwira ntchito molimbika, kufufuza machitidwe osiyanasiyana mu dziko la kwathu komanso ku New York, Kumene ndinakhala zaka zochepa.Nditabwelera ku Argentina ndinali ndi mwayi wokuza ntchito yanga yojambula zithunzi mu ma buku ambiri, Zogwirizana kwambiri ndi chilengedwe komanso uzimu. Maluso anga onse opatsidwa ndi Mulungu agwiritsidwa ntchito pojambula zithunzi mu khani ya Mfumu ya Ulemelero. .Kwa ine, uku ndi kukwaniritsidwa kwa maloto, mwayi wa kamodzi pa chaka. Ndikuthokoza Mulungu kwambiri chifukwa cha mwayi uwu. Ndikuthokozanso Paul Bramsen,Amene ndi mlembi wa luso ndi dongosolo. mkonzi. Ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha nzeru zake komanso kutsogolera kwake pondithandiza kukwaniritsa ntchito iyi." Arminda tsopano amagwira ntchito yofotokozera zithunzi kwa alembi ambiri.
Mupezeni: **armisanmartin@yahoo.com.ar**

*Printed in China*





# Kwa Mfumu ya Ulemelero ndi Dalitso la Ana a Misinkhu Yonse









*"chitetezo? Ananena zokhudza chitetezo ndani?'Palibe chitetezo. Koma alibwino. Ndi Mfumu, Ndikuuzani inu."*

— Kuchokera *The Lion, the Witch, and the Wardrobe* by C.S. Lewis







# Gawo la sewero


**Kuseli kwa zochitika musewero** ........................................................ 8

**Mawu oyamba**........................................................................ 11

1 • Mfumu ndi dziko lake la Ufumu

2 • Mfumu ndi Aneneri Ake

3 • Mfumu ndi Dziko Lake

**Part 1 – Mfumu lyankhula dongosolo Lake la za tsogolo** ........................ 19

| | |
|---|---|
| 4 • Tsiku Loyamba | Genesis 1 |
| 5 • Dziko Lolungama | Genesis 1-2 |
| 6 • Mwamuna Oyamba | Genesis 1-2 |
| 7 • Malo Okhala Abwino | Genesis 2 |
| 8 • Lamulo la Uchimo ndi Imfa | Genesis 2 |
| 9 • Mkazi Oyamba | Genesis 2 |
| 10 • Ufumu Wa Chiyero | Chibvumbulutso 4-5 |
| 11 • Dziko La Mdima | Yesaya 14; Ezekieli 28 |
| 12 • Njoka | Genesis 3 |
| 13 • Chisankho | Genesis 3 |
| 14 • Tchimo ndi Manyazi | Genesis 3 |
| 15 • Kufa mu Uzimu | Genesis 3 |
| 16 • Thembelelo | Genesis 3 |
| 17 • Lonjezo | Genesis 3 |
| 18 • Nsembe Yoyamba | Genesis 3 |
| 19 • Kuchotsedwa | Genesis 3 |
| 20 • Ana Oyambirira | Genesis 4 |
| 21 • Chipembezo cha Ochimwa | Genesis 4 |
| 22 • Lamulo la Nsembe ya Tchimo | Genesis 4 |
| 23 • Kuvomerezedwa ndi Kukanidwa | Genesis 4 |
| 24 • Kupha Koyambirira | Genesis 4-5 |

25 • Kuleza Mtima ndi Chigamulo — Genesis 6-7
26 • Kuyamba kwa Tsopano — Genesis 8-9
27 • Nsanje ya Kudzitama — Genesis 11
28 • Mulungu Ayitana Abrahamu — Genesis 12
29 • Osunga Lonjezo — Genesis 15
30 • Yesero Lalikulu — Genesis 22
31 • Mwana Woyenera Imfa — Genesis 22
32 • Zinthunzi ndi Uneneri — Genesis 22
33 • Mulungu Okhulupirika ndi Oyera — Eksodo 19-20
34 • Malamulo Khumi — Eksodo 20
35 • Zithunzi Zowonjezera — Eksodo 20, 24
36 • Ulosi Owonjezera — Masalmos & Mneneris

**Part 2 – Mfumu ikwaniritsa chikonzero chake**.............................................. 87

37 • Nkhani Ya Mfumu Ipitirira — Mateyu 1
38 • Nkhani ya Mariya — Luka 1
39 • Nkhani Ya Yosefe — Mateyu 1
40 • Kufika — Luka 2
41 • Nkhani ya Abusa — Luka 2
42 • Nkhani ya Anzeru Akum'mawa — Mateyu 2
43 • Mwana Wosalakwa (Wopambana) — Luka 2
44 • Mwana wa Nkhosa wa Mulungu — Yohane 1
45 • Mwana wa Bwana — Mateyu 3
46 • Munthu Wachiwiri — Mateyu 4
47 • Mesiya-Mfumu — Luka 4
48 • Ufumu pa Mizimu Yoyipa ndi Matenda — Luka 4
49 • Ufumu pa Mphepo ndi Mafunde — Marko 4
50 • Ufumu pa Tchimo — Marko 2
51 • Ufumu pa Imfa — Luka 7; Yohane 11
52 • Opereka — Yohane 6
53 • Mphunzitsi — Mateyu 5-7

54 • Wolemekezeka — Mateyu 17
55 • Cholinga Chake — Mateyu 16, 20
56 • Mfumu Ilowa mu Yerusalemu — Marko 11
57 • Mfumu Ikufunsidwa Mafunso — Luka 20
58 • Mfumu Yamangidwa — Marko 14
59 • Mfumu Yaukilidwa — Yohane 18
60 • Mfumu Yamangidwa — Mateyu 27
61 • Mfumu Yapachikidwa Pamtanda — Luka 23
62 • Mpulumutsi-Mfumu — Luka 23
63 • Kupereka Nsembe Komaliza — Mateyu 27
64 • Mfumu Yaikidwa M'manda — Mateyu 27
65 • M'manda Mopanda Kanthu — Mateyu 28
66 • Uthenga wa Aneneri — Luka 24
67 • Thupi Losandulika — Yohane 20
68 • Kunyamuka — Acts 1
69 • Chikondwelero Chopambana — Masalmo 24; Chibvumbulutso 5
70 • Mfumu Ikubweranso — Chibvumbulutso 19-22

**Mathero** ........ 157

• Kusangalala Kwamuyaya?

• Uthenga Oyipa

• Uthenga Wabwino

• Yankho kwa Mfumu

**Zowonjezera...** ........ 167

• Mafunso olondola sewero

• Zolemba zomaliza

• Kupita Mozama

# KUSELI KWA ZOCHITIKA MUSEWERO

*Alice anayamba kutopa ndikukhala pafupi ndi mkulu wake ,opanda chochita chenicheni; Pena amasuzumira pang'ono buku limene mkulu wake anali kuwerenga, koma linalibe zithunzi kapena kuonetsa kukambirana kwa khani, "ndiye kuti buku ili ntchito yake ndi chiyani," analingalira Alice, Lopanda zithunzi kapena kukambirana?"*

— ZOLEMBEDWA ZOYAMBA MU "*ALICE'S ADVENTURES IN WONDERLAND*" NDI LEWIS CAROLL, 1865

Buku limene mukuyandikira kuwerenga ladzala ndi zithunzi komanso zokambitsana, Koma mosiyana ndi khani yongosangalatsa ya 'Alice in Wonderland',[1] zithunzi ndizokambitsana za mu khani ya Mfumu YA ULEMELERO zinachitikadi.[2]

Chidwi chinandipangitsa kulemba buku la zithunzi kufotokozera khani yapamwamba kwambiri mwa khani zonse zonenedwa. Zaka zapitazo, Ndikukhala kumadzulo kwa Africa, ndinapanga maphunziro okhudza zoulutsa mawu pa wailesi.Tsiku loyamba aphunzitsi anafunsa, "Wailesi ndi yofunika mosiyana bwanji kuposa kanema?" Yakho lake linatidabwitsa

"Imapereka chithunzi chabwino."


Zoona.

Ngakhale kanema wapamwamba opangidwa ndi ndalama zochuka amavutika kulumikizitsa maganizo amunthu potathauzira mawu ang'ono pogwiritsa zithunzi zongoganizira.Malemba a neneri amaonetsera zithunzi za mu mawu ochuluka zimene kanema sangaonetse bwino, palibenso munthu wa luso amene angajambule bwinobwino.

Choncho ndikuvomereza. Palibe zojambula za luso zomwe zingafotokoze bwino khani yapamwamba thawi zonsezi.

Komabe, Ndizosangalatsa kuyesera.





Arminda San Martín, ojambula zithunzi mwa luso ochokera ku Argentina,

Wagwira ntchito ya Bwino potathauzira nkhani za Baibulo pogwiritsa ntchito kujambula zithunzi. Arminda anamaliza ntchito yofotokoza khani pogwiritsa zithunzi zojambula yekha kwa miyezi khumi ndi inayi.

Ndikhulupira kuti mukhala ndi chidwi ndi khani yake ngat ine.

Taganizirani izi.

Tikamawerenga buku la nkhani, timayambira pati? Pakati? ayi, Timawerenga tsamba loyamba. Choncho timamvetsa nkhani. Chimodzi modzi kuti timvetse malemba tiyenera kuwerenga poyambira, Ndi kutsatira nkhani mwa dongosolo mpaka pothera posangalatsa.

Zolemba za aneneri zili ndi nkhani zazifupi zochuluka zimene pamodzi zimapanga nkhani imodzi. Polemba nkhani ya Mfumu YA ULEMELERO,ndinamva ngati munthu wogwira ntchito yosamalira maluwa otumidwa mu munda wa ukulu. ndikukatenga maluwa ochepa kuwapanga mpukutu wa maluwa umene uonetsere kukongola kwa munda wonse. Kwa buku ili, ndasakha nkhani zochepa kuchokera mu Baibulo, ndikuzifotokozera mu magawo 70 a sewero kuonetsera ulemelero wa Mfumu yosatha imene yazionetsera yokha mu mbiri ya anthu.

Pemphero langa kwa Mulungu ndi lakuti kuonetsa ndi kufotokozera nkhani yoona iyi kubweretsa chidwi kwa onse omvera a zaka zosiyanasiyana kuwerenga zolemba za aneneri, kukhala muchikondi ndi Iye okambidwa muzolembazi, ndi kulowa mu ufumu wa chimwemwe umene sudzatha.

Mwa chithunzi chabwino,



# Mawu Oyamba

Mtima wanga usefukira nacho chinthu chokoma. Ndinena zopeka ine za Mfumu: Lilime langa ndilo cholembera chofulumiza kulemba.

Ndipo pindulani, m'ukulu wanu yendani, Kamba ka choonadi ndi Chifatso ndi chilungamo; Ndipo dzanja lanu lidzakuphunzitsani zoopsa.

— Kuchokera ku Mawu a Aneneri (Masalmo 45:1,4)

## Gawo la sewero 1
# Mfumu ndi Dziko lake la Ufumu

Kalekale dziko lisanakhaleko, kunali Mfumu, Mfumu ya ulemerero.

Mfumu imeneyi inali kumalo kumene wina aliyense sangafikireko. Mfumuyi inalipo yokha ndipo ufumu wake unali opanda malire. Iyoyo inali ndi nzeru zopambana, yachikondi, yachimwemwe komanso mtendere. Dzikoli silimafunikiranso dzuwa kapena nyenyezi, Chifukwa Mfumuyi inali kuwala.

Ngakhale dzikoli linalibe malire, koma chiwerengero cha okhalamo ake chinali chokhazikika. Ena amati Mfumuyi inalibe omutsatira ngakhale m'modzi.

Kapena anali nawo?

Chinsinsi choyamba cha Mfumu imeneyi chinali chakuti ngakhale inalipo yokha, koma sanakhalepo yekha.

Komabe, Iye amafuna kuyanjana ndi anthu ena anzeru.

Choncho Mfumu yabwino ndi yanzeruyi inapanga mzinda wakumwamba wodzala ndi zikwizikwi za angelo onyezimira ndi anzeru zakuya. Onsewa amawadziwa ndi maina awo ndipo Mfumuyi imafuna kuti nawonso ayidziwe. Moyo wokhala ndi Mfumuyi unali wochititsa chidwi nthawi zonse.

Koma Mfumuyi inkafuna zolengedwa zina zoposa angelo. Choncho analenga nthawi, dziko ndi zinthu zokhalamo – komanso malo okongola kwambiri amene anayikamo munthu.

Anthu analengedwa awiri okha, mwamuna ndi mkazi zomwe zili zosiyana ndi angelo. Mfumuyi inafunanso kukhala pachiyanjano ndi anthuwa monga mmene zinalili ndi angelo.

Kenaka chinachake chinachitika, chinali choyipa. Panali kuukira mu Ufumu wa kumwamba kenaka kunafalikira ku dziko lapansi.

Mngelo owukira analanda ulamuliro wa dziko lapansi posokoneza chikhalidwe cha anthu. Koma Mfumu siinadabwe.

Mfumu inali ndi njira yopulumutsira anthu yozama kwambiri

Yodabwitsa ndi yakuya, imene idzatenga zaka zambiri kuti ikwaniritsidwe.

Kodi ndi chiyaninso chimene mungayembekezere kwa Mfumu ya muyayayi?

Alibe chiyambi komanso mathero.





## Gawo la sewero 2
# Mfumu ndi Aneneri Ake

Kuti mudziwe za Mfumu ndi dongosolo lake, mukuyenera kudziwa Bukhu lake.

Kwa zaka chikwi chimodzi ndi mazana asanu, Mfumu inasankha anthu pafupifupi makumi anayi kuti alembe za Iyo ndi uthenga wake. Anthuwa amatchedwa aneneri. Mfumu inawapatsa anthuwa mawu ake, amene analembedwa kuti adzachulukitsidwe, kufalitsidwa komanso ndi kusungidwira mibadwo ya mtsogolo. Ngakhale aneneri ambiri samadziwana koma zolemba zawo zimafotokozera nkhani yofanana ndiponso uthenga umodzi.

Zolemba za aneneriwa zimatchedwa Mawu a Mulungu. Popanda Mawu a Mulunguwa sitikanadziwa kumene tinachokera, chifukwa chiyani tili pa dziko pano, ndipo tikupita kuti. Kuti tidziwe mayankho oyenera tikufunika Baibulo.

Pafupifupi zaka zikwi zitatu ndi mazana atatu apitao, Mfumu inauza mneneri wotchedwa Mose kuti alembe izi:

> Munthu sakhala wa moyo ndi mkate wokha, koma munthu akhala wa moyo ndi zonse zakutuluka mkamwa mwa Yehova. (Deuteronomo 8:3)

Lero mawu a Mfumuyi tilinawo m'Bukhu limodzi lotchedwa Buku Lopatulika. Kupatulika kumatanthauza *ungwiro* kapena *kukhala losiyana ndi ena onse*. Baibulo limatanthauza bukhu kapena *mabuku* osindikizidwa mu Bukhu limodzi. Baibulo ndi bukhu loyenda malonda kwambiri ndipo lamasuliridwa m'zinenero zambiri pa dziko lapansi. Uthenga olembedwa pa zikopa ndi zinthu zina zambiri umaonetsera kuti Baibulo linasungidwa bwino kuyambira kale.[3]

Baibulo lili ndi magawo awiri:

Gawo loyamba ndi Chipangano cha Kale (Mabuku asanu oyamba, Masalmo ndi ena otero.) M'menemo, Mfumu inalemba ndondomeko ya malingaliro ake.

Gawo lachiwiri ndi Chipangano chatsopano (Uthenga wabwino, Ntchito za Atumwi ndi mabuku ena otero.) M'menemo Mfumu ikukwaniritsa ndongosolo lake.

*Chipangano chimatanthauza mgwirizano kapena kuvomerezana*. Chipangano cha kale chimanena zimene Mulungu anakonzeratu kuti adzazichita. Chipangano Chatsopano chimanena za kukwaniritsidwa kwa zimene Mulungu anakonza. Ndi Mulungu yekha amene angalembe mbiri ya zinthu zisanachitike.

Kusiyana kwa Chipangano Chakale ndi Chatsopano zili ngati kusiyana pakati pa Mfumu yongotumiza makalata ndi zithunzi ndi Mfumu yokuyenderani.

Mawu a Mulungu anabwera ndikudziwika koyamba ku Middle East, Africa, Asia, ndi ku Ulaya, kenaka ku Amerika ndi kufikiranso maiko ena. Aneneri anachokera ku Middle East, koma nkhani ndi Uthenga umene analemba ndi wopita ku maiko onse, banja lililonse komanso munthu aliyense.

Kwa inu.





## Gawo la sewero 3

# Mfumu ndi Dziko Lake

Tikaona nthawi ya m'mbuyo Mulungu asanalenge anthu, dziko ndi nyenyezi timaona mphamvu ndi ulemelero wa mawu a Mulungu.

> Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. (Genesis 1:1)

Anthu ambiri lero amaganiza kuti dziko lapansi ndi zonse zodabwitsa zake zinangopezeka popanda Mlengi wa nzeru. Koma malingaliro awa samafotokoza momveka bwino luso limene linagwiritsidwa ntchito polengedwa dziko ndi zonse.

M'buku lake, Mfumu ikuti:

> Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; ndipo thambo limaonetsera ntchito ya manja ake.  (Masalmo 19:1)

Kunena za manja, yang'anani manja anu. Pindani zala zanu zazikulu. Yesani kugwira bukhu, tsache ndi nyundo opanda  zalazo. Taonani zala zanu ndi khungu lanu. Ganizirani zinthu zina zofunikira zimene mumachita ndi manja anu. Waluso wake ndi ndani amene anapanga zimenezi?

Kodi ndi nzeru ndi mphamvu zotani zingafunike kuti miyandamiyanda ya zinthu za mlengalenga zipangidwe? Kapena kulenga chinthu cha moyo chokhala ndi timagawo tating'onoting'ono tambirimbiri? Kapena kupanga ziwalo zosiyanasiyana zimene pamodzi zimapanga munthu kuti akhale munthu

Zaka zikwi zitatu zapitazo, mneneri komanso Mfumu yotchedwa Davide inati:

> Munandiumba ndisanabadwe ine. Ndikuyamikani chifukwa kuti chipangidwe changa ndi choopsa ndi chodabwitsa. (Masalmo 139:13-14)

Kodi mungafune kukumana ndi amene anakulengani? Kodi mungakonde kukhala naye amene analenga zam 'mwamba zonse kwa muyaya? Mungathe. Iye anadzionetsera Yekha. Akufuna inu mumdziwe. Akufuna banja lanu ndi anthu a m'dera lanu amudziwenso. Akufuna inu mudziwe zofuna zake, kumva chikondi chake, kuona ukulu Wake, kungonjera ulamuliro wake, ndi kukhala mu ulemelero Wake. Koma sadzakukakamizani kukhala wolamuliridwa ndi iye.

Chodziwikiratu ndi chakuti iyeyo si Mfumu wamba ayi. Iye ndi *Mfumu ya ulemerero.*


Nkhani yake ndi imeneyi.



# Gawo 1

## Mfumu Iyankhula Dongosolo Lake la za Tsogolo

— Chipangano Chakale —



## Gawo la sewero 4
# Tsiku loyamba

Mawu a Mulungu akuyamba ndi kulemekeza Mfumu. Iyo Ikutiuza zimene ikufuna kuti ife tizidziwe.

Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. (Genesis 1:1)

Chilichonse chimene timachiona ndi kuchigwira chili ndi chiyambi, koma Mlengi ndipo Mwini wake dziko alibe chiyambi ngakhalenso mathero. Iye ndi wosaoneka, ndi Mzimu wa muyaya amene amapezeka paliponse. Iye amaona ndipo amadziwa zonse.

Kodi mukudziwa dzina la Mfumuyi? Mulungu ali ndi maina ambiri, koma dzina lake lotchuka ndilo AMBUYE. Mu chiyankhulo choyamba cha Baibulo, akutchedwa Yahweh, kutanthauza kuti: IYE AMENE ALI, kapena INE NDINE.

Popitiriza nkhani ya chilengedwe Mfumu ikufotokozera m'mene dziko linalili pa chiyambi.

> Dziko lapansi ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa Nyanja; ndipo Mzimu wa Mulungu Unali kufungatira pamwamba pa madzi. (Genesis 1:2)

Nthawi yokonza dziko lokhalamo anthu inali itakwana.

> Ndipo anati Mulungu, kuyere; ndipo kunayera. Ndipo anaona Mulungu kuti kuyerako kunali kwabwino: ndipo Mulungu analekanitsa kuyera ndi mdima. Ndipo Mulungu anatcha kuyerako usana, ndi mdimawo anautcha usiku. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku loyamba. (Genesis 1:3-5)

Kodi Mulungu anachita chiyani pa tsiku loyamba la kulengedwa kwa zinthu? Iyeyo analamulira kuwala kuti kuchotse mdima. Kenaka dzuwa ndi limene linadzapereka kuwala pa dziko lapansi, komano sizinali choncho pa tsiku loyamba. Mulungu akufuna ife tidziwe kuti Iye ndiye kuwala.

> Mulungu ndiye kuunika; ndipo mwa Iye mulibe mdima. (1 Yohane 1:5)


Mulungu ndi woyera monga kuwala. Sangadetsedwe. Ngakhale pamene kuwala kuwunikira pa chinthu chodetsedwa, kuwalako sikusinthika. Mulungu ndi wangwiro. Mulungu ndi woyera.


Kodi mukudziwa amene anali ndi Mulungu pamene amalenga? Mzimu wake Woyera anali pompo, akuyenda pamwamba pa madzi. Mawu Ake anali pompo, akuyankhula.

> Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali kwa Mulungu, ndipo Mawu ndiye Mulungu. Awa anali pachiyambi ndi Mulungu. Zonse zinalengedwa ndi Iye… (Yohane 1:1-3)

Mzimu Woyera pamodzi ndi Mawu akhala ali ndi Mulungu Atate amene ali m'modzi ndi woona kwa nthawi zonse. Ndi chifukwa chake zikhoza kunenedwa za Mfumu kuti:

*Ngakhale pamene anali yekha, Iye sanakhalepo yekha .*





## Gawo la sewero 5
# Dziko labwino

Mu masiku asanu ndi limodzi, Mfumu inalenga dziko lokongola ndi lodabwitsa. Mulungu anangoyankhula, ndipo zinthu zokonzedwa bwino zinaoneka.

Tsiku 1 Mulungu anati: “Kuyele!’ ndipo kunayera.

Tsiku 2 Mulungu anapanga mlengalenga ndi thambo limene timaliona komanso mphweya umene timapuma. Mulungu anaika mlengalenga mpweya wofunikira ku moyo wa zinthu zolengedwa zonse.

Tsiku 3 Mulungu anati: “Kukhale mtunda! Ndipo udaoneka. Zimenezo ndi zimene zinachitika. Kenaka Mulungu anati: “nthaka ipatse zomera!” nthawi  yomweyo, udzu, zomera, maluwa ndi zipatso zinayamba kumera, chilichonse ndi mbeu yake.

Tsiku 4 Mulungu analamulira dzuwa ndi mwezi kuti ziwale. Iye anakhazikitsanso zaka, miyezi ndi masiku a pa dziko lapansi. Iye analenganso nyenyezi.

Tsiku 5 Mulungu anati, madzi adzale ndi nsomba ndi   za moyo zina! Mlengalenga mudzadze ndi mbalame za mitundu yosiyanasiyana!’ Ndipo izi ndi zimene zinachitikadi.

Tsiku 6 Mulungu anati: “Dziko lapansi likhale ndi mitundu yosiyanasiyana ya nyama – zoweta, zazing’onozing’ono komanso za kutchire!” Mulungu anapanga chilichonse cha moyo kutha kubereka ndikusamalira ana ake.

> Mulungu anaona kuti zinali bwino. (Genesis 1:25)


Panali mtendere pa dziko. Pachiyambi nyama zonse zinali pa ubale wabwino. Sizimaphana kapena kudyana. Chakudya chawo chimachokera ku zomera.

Panali dongosolo pa dziko. Dzuwa linali lotalikirana bwino ndi dziko lapansi. Mwezi umasintha pa kuyamba ndi kuoneka pang’ono kenako kuoneka wonse. Dziko lapansi limakonzanso mpweya, madzi komanso nyansi zake. Likadalamulidwa bwino dziko, ufumu wake sukadasowa chilichonse chabwino. Dziko likadakhala malo oyenera kukhalapo munthu.

Tsiku lililonse la chilengedwe limatipatsa chithunzithunzi cha m’mene Mulungu alili.[4]

> Tsiku 1 likutiwonetsa kuti Mulungu ndi woyera. Iye ndi wolungama ndi wangwiro ngati kuwala.
>
> Tsiku 2 likutisonyeza kuti Mulungu ndi wamphamvu zonse. Iye anapanga ndipo amasamalira mlengalenga.
>
> Tsiku 3 likutiphunzitsa kuti Mulungu ndi wabwino.  Iye  analenga zomera zochuluka komanso zakudya zathu.
>
> Tsiku 4 limafotokozera kuti Mulungu ndi wokhulupirika. Dzuwa ndi mwezi zinakhala m’malo awo oyenerera.
>
> Tsiku 5 likutitsimikizira kuti Mulungu ndi moyo. Anaika nsomba mu nyanja ndi mbalame mlengalenga.
>
> Tsiku 6 likunena kuti Mulungu ndi chikondi. Mulungu atalenga nyama, analenganso anthu kuti awaonetsere chikondi chake. Inali nthawi ya kupanga cholengedwa chapaderadera chakuti chionetsere chiyero, mphamvu, ubwino, kukhulupirika, moyo ndi chikondi chake.





## Gawo la sewero 6
# Mwamuna Oyamba

Pa tsiku lachisanu ndi chimodzi la kulenga, Mfumu inayankhula, (Mulungu Tate, Mzimu Oyera ndi Mawu) kuti:

> "Tipange munthu m'chifanizo chathu, m'amaonekedwe athu,[5] ndipo alamulire….pa dziko lonse lapansi…ndi pa zamoyo zonse…"
>
> Choncho Mulungu adamulenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo chake adamulenga Iye; adawalenga iwo mwamuna ndi mkazi. (Genesis 1:26-27)

Pamene Mawu akunena kuti Mulungu analenga anthu mu chifanizo Chake, sizitathauza kuti Mulungu ndiwofanana ndi Ife. Zikutiphunzitsa kuti tiyenera kuwonetsera moyo wake ndi chikhalidwe chake. M'mene ndalama ya a Roma inasindikiziridwira chithunzi cha mtsogoleri wawo, nchonchonso Mulungu anasindikiza chithunzi chake pa munthu. Mwamuna oyamba ndi mkazi oyamba analengedwa ndi kuthekera koganiza, kukonda ndi kuyankhula ngati Mlengi wawo kuti asangalale mu ubale wabwino ndi Iye. Anthu sanapangidwe kukhala akapolo a Mulungu, koma abwenzi ake.

Mulungu atalenga anthu m'chikhalidwe chake, anawapatsa ulamuliro. Anthu ankayenera kusamalira ndi kulamulira dziko lapansi m'malo mwa Iye, ndi kuzindikira zinsinsi ndi kugwiritsa ntchito mwanzeru. Choncho munthu ali ndi chikhalidwe chosiyana ndi nyama.

Mulungu anapereka magawo awiri kwa nyama amene ali thupi ndi moyo. Ndipo kwa Munthu anapereka magawo atatu amene ali thupi, moyo ndi mzimu.

> Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wa moyo mphuno mwake; munthuyo nakhala moyo. (Genesis 2:7)

Thupi linali nyumba chabe, m'mene Mulungu anauzira moyo ndi mzimu wa munthu.

Moyo unali nzeru za munthu, zokhumba zake ndi chifuniro chake, zimene zidapangitsa munthu kuganiza, kumva ndi kutha kupanga chisankho.


Munthu anayanjana ndi Mulungu chifukwa cha Mzimu. Pamene thupi linamuthandiza munthu kulumikizana ndi dziko, Mzimu anathandiza munthu kulumikizana ndi Mulungu osawoneka. Ambuye akufuna kuti anthu amudziwe.

Munthu anali chuma chapamwamba cha Mulungu. Popeza Mulungu anawalenga iwo, sanangokhala Mlengi wawo chabe, komanso anali Mwini wa iwo.

Ambuye Mulungu adapanga Adamu dzina lake limatanthauza kuti *ochokera kunthaka,* mwachidule *Munthu*. Kenako anapanga mkazi oyamba, koma asanatero panalinso zina zoti akonzekere kuti amupange.

Adamu amafunika pokhala ndi ntchito.





## Gawo la sewero 7

# Malo okhala abwino

Atapanga munthu woyamba kuchokera ku dothi[6] ndi kumupumira phweya wa moyo, Mulungu anadzala munda wa Edeni, cha ku Middle East.

Mtsinje wokongola umadutsa pakati pa mundapo.

> Ndipo Ambuye Mulungu analenga mitengo yamitundu yosiyana yokoma m'maso ndi yabwino kudya imere m'thaka; pakati pa mundapo panali mtengo wamoyo ndi mtengo wakudziwitsa chabwino ndi choyipa.
>
> Ambuye Mulungu anatenga munthu, ndikumuika m'munda wa Edeni kuti aulime ndikuusamalira. (Genesis 2:9,15)

Mulungu sanafunsire nzeru kwa Adamu pamene amalenga zinthu m'munda wa Edeni popeza iye sankadziwa zimene zinali zabwino kwa munthu.

M'munda wa Edeni munali zinthu zopatsa chidwi, zinthu zooneka modabwitsa, zonunkhira bwino, komanso zokoma kudya. Mitsinje yonyezimira, mbalame zoimba. Maluwa onukhira. Zolengedwa za bweya, zipatso za mmadzi, masamba odyeka. Zipatso zotsekemera, Nkhalango zodabwitsa, miyala yamitundumitundu, tizirombo topatsa chidwi. Ndipo miyandamiyanda ya zinthu zina zodabwitsa zachilendo.

Mulungu anamupanga Adamu kukhala kholo la mtundu wa anthu osati kungomuzindikira. Mulungu amafuna Adamu ndi banja lake kuti adzilamulira pamodzi ndi Iye nthawi zonse. Koma okhawo amene angadalirike ndi ntchito zazing'ono akhoza kupatsidwa ntchito zazikulu.

Choncho Mulungu anampatsa Adamu ntchito yoyamba: Kusamalira munda.

Mundawo udali malo abwino, opanda minga, tchire komanso tizirombo toyipa. Nyengo idali yoyenera, dothi lake lachonde, mvula sinali kugwa. M'malo mwake, chinyezi chimachokera pansi ndipo chimathirira thaka.

Mulungu anampatsanso Adamu ntchito yotchula zinyama maina.

Mulungu anamupatsa ufulu wopereka maina kwa zolengedwa zonse. Tangoganizirani m'mene zinalili. Zinyama ziwiriziwiri zokhala ndi msana wotambalala ndi miyendo ya mphamvu zinandanda. Adamu anaziona bwinobwino, anazimenya pa misana pawo, ndipo anazitcha a bulu. Pakuitana kwa Mlengi, chimbalame chachikulu cha mlomo wautali ndi mapiko aakulu chinatera, "Chiomba khanga!" anatero Adamu. Kenako, chirombo chofiira ndi mawanga akuda chinadutsa. Kodi mukuganiza kuti Adamu anachitcha chiyani?

> Ndipo mwamuna anatcha maina zinyama zonse, ndi mbalame za mlengalenga ndi nyama zonse za m'thengo: koma kwa Adamu sanapezedwe womuthangatira iye. (Genesis 2:20)

Munda wa Edeni anali malo abwino kwa munthu kuti adziwe Mlengi wake.

Inali nthawi yomupatsa Adamu yesero.





## Gawo la sewero 8

# Lamulo la Uchimo ndi Imfa

Kuyambira pa chiyambi, Mulungu ndi munthu anali pa ubwenzi, koma ubwenzi umenewo umafunika kuyesedwa. Mfumu siyimafuna kuti omutsatira adzikakamizidwa kuigonjera Iyo.

Mulungu anamukonda Adamu ndipo anali ndi malingaliro abwino pa Iye ndi banja lake lamtsogolo. Chifukwa Mulungu amafuna anthu osati zinthu chabe, Anampatsa Adamu lamulo lakuti alimvere.

> Ndipo Ambuye Mulungu analamulira, munthu, "Mitengo yonse ya m'munda udyeko; koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoyipa usadye; chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu." (Genesis 2:16-17)

Ili silinali lamulo lovuta. Adamu akanadya chipatso chilichonse m'munda kupatula chimodzi. Pakumvera lamulo lophwekali, Adamu akanawonetsa kuti amamukhulupirira Mlengi wake kuti amadziwa zimene zinali zabwino kwa iye.

Kodi Mulungu ananena kuti chidzamuchitikire ndi chiyani Adamu akaphwanya lamulo limeneli?

Kodi Mulungu anamuuza Adamu kuti akadya chipatso choletsedwa adzayambe kuchita zikhulupiriro za zipembedzo, kugwiritsa ntchito kolona, kusala kudya, kupereka zopereka, kupita kukachisi kapena kumzikiti, ndi kuyesa kuchita ntchito zabwino mokwanira kuti afafanize ntchito zoyipa? Kodi ndi zimene Mulungu ananena?

Ayi, izi sizimene Mulungu ananena.

Mulungu anamuuza Adamu kuti: "Ukadya *udzafa* ndithu""

Kusamvera malamulo a Mulungu kumatchedwa *tchimo*.Chilango chakuswa lamulo la Mulungu ndi *imfa*. M'bukhu lake, Mfumu akulitcha kuti "lamulo la uchimo ndi imfa." (Aroma 8:2)

Lamulo la Mfumu limati tchimo liyenera kulangidwa ndi imfa.

Imfa imatanthauza kulekana. Adamu akanapanda kumvera lamulo limodzi la Mulungu,

Iye akanakhala ngati nthambi imodzi yothyoka imene ikadanyala ndi kufa nthawi yomweyo, yalekana ndi magwero a moyo wake.

Adamu akanasankha kuchita zimene anafuna kuchita m'malo mwa zimene Mfumu ya Dziko inamuuza achite, mchitidwe umenewo ukanakhala kugalukira: likanakhala tchimo.

Uchimo ukanathetsa ubwenzi wa munthu ndi Mulungu.

Uchimo ukanapangitsa thupi la munthu kukalamba ndi kufa.

Uchimo ukanalekanitsa mzimu, moyo ndi thupi la munthu ndi Mulungu kwa muyaya.

Uchimo umapha.





## Gawo la sewero 9

# Mkazi Woyamba

Mulungu atampatsa mwamuna woyamba ntchito ndi lamulo loti alimvere,inali nthawi tsopano yopanga mkazi woyamba

> AMBUYE Mulungu anati: "Sikwabwino kuti mwamuna akhale yekha" Ndidzam'pangira womuthangatira womuyenera."
>
> Choncho AMBUYE Mulungu anam'pangitsa mwamuna kugona tulo tatikulu: ndipo iye ali chigonere, anatenga nthiti ya mwamuna ndipo anatseka pamene anachotsa nthitipo ndi m'nofu. Kenaka AMBUYE Mulungu anapanga mkazi kuchokera ku nthiti imene anatenga kuchokera kwa mwamuna, ndipo anamubweretsa iye kwa mwamuna.
>
> Ndipo mwamuna anati: "Uyu tsopano ndiye fupa la mafupa anga, ndi mnofu wa mnofu wanga; ndipo adzatchedwa mkazi chifukwa anamtenga mwa mwamuna." (Genesis 2:18,21-23)

Kodi mukuzindikira amene anapanga opaleshoni yoyamba-komanso amene anakonza ukwati woyamba? Inde, anali Mulungu.

Mawu akuti Mkazi mu chingerezi amatanthauza kuti otuluka mwa mwamuna.Kenaka, Adamu anamutcha mkazi wake Hava, kutanthauza kuti mayi wa onse. Pamene Mulungu anawapatsa ntchito zosiyana, Anapanga Mwamuna ndi mkazi kukhala ofunikira mofanana.Monga Adamu, Hava analengedwa m'chifanizo cha Mulungu. Iyenso anapangidwa kuti adziwe Mlengi wake, kuonetsera khalidwe lake, komanso kukhala mu ubale wabwino ndi Iye kwa muyaya.

> Mulungu anaona zonse zimene anapanga, ndipo zinali bwino kwambiri. Ndipo kunali madzulo, ndiponso kunali m'mawa – Ili ndilo tsiku lachisanu ndi chimodzi.
>
> Patsiku la chisanu ndi chiwiri Mulungu anamaliza ntchito yake yonse; choncho Iye anapuma ku ntchito yake yonse. (Genesis 1:31; 2:2)


Chifukwa chiyani Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri? Chifukwa ntchito yake inatha. Komanso, polenga dziko lathu masiku asanu ndi limodzi ndi kupuma tsiku lachisanu ndi chiwiri, Mulungu anakhazikitsa sabata la masiku asanu ndi awiri--- dongosolo lopumira pantchito limene likugwiritsidwa ntchito padziko lonse lapansi.


AMBUYE Mulungu, ngati bambo wanzeru ndi wachikondi anasamalira Adamu ndi Hava. Madzulo aliwonse, amabwera ku munda, kudzawayendera ndi kudzayankhula nawo.

> Mwamuna ndi mkazi wake anali amaliseche ndi omasuka pamaso pa Iye. Ndipo panalibe manyazi. (Genesis 2:25)

Tangoganizirani dziko labwino lokhalamo banja lokhulupirika lomwe lili mu ubwenzi wabwino ndi Mlengi wolungama. Ndi m'mene zinthu zinalili pachiyambi.

Nanga chinavuta nchiyani?





## Gawo la sewero 10

# Ufumu wa Kuwala

Tisanadziwe chimene chinalakwika pa dziko lapansi, tiyenera kumvetsa zinthu zina zokhudzana ndi kumwamba.

Dziko lotchedwa Paradizo, ndi malo owala kwambiri, a nyimbo zokoma, a zoyankhula zogwira mtima komanso a zinthu zosangalatsa.Zochititika zazing'ono za zakumwamba zimaposa zochitika zazikulu za dziko lapansi. Kumwamba ndi kosiyana ndi dziko lapansi.

Kumwamba ndi kwawo kwa Mfumu. Mfumu inapanga Paradizo kukhala malo osangalatsa. Kukongola kwa mzindawu kumaonetsera ukulu ndi ulemelero wa Mfumu.

> Ndipo mzindawo ndiwa golidi woyengeka, wofanana ndi mandala woyera.
> (Chibvumbulutso 21:18)

Nkhani ya Kumwamba inalembedwa mwatsatanetsatane mu buku la Chibvumbulutso. Mulungu anampatsa m'neneri Yohane mwayi owona kumwamba ndipo anamuuza kuti alembe zimene anaziona.

> Pambuyo pa inepo panali mpando wachifumu kumwamba ndipo wina wakukhalapo… Utawaleza umene unawala ngati malo okongola unazungulira mpando wachifumuwo… Kuchokera ku mpando wachifumu kunatuluka kung'anima kwa mphenzi, ndi kugunda ndi kulira kwa ziphaliwali…Kutsogolo kwa mpando wachifumu kunali chimene chimaoneka ngati Nyanja yaikulu ya galasi, yowala ngati Nyanja ya mandala Ndinapenya ndipo ndinamva mawu a angelo ambiri, ndipo mawerengedwe awo anali zikwi zikwi, komanso zikwi khumi kuchulukitsa ndi zikwi khumi. Anazungulira mpando wachifumu…sanasiye kunena kuti "Woyera, woyera, woyera Ambuye Mulungu Wamphamvu zonse, amene anali, amene ali, ndi amene alinkudza."
> (Chibvumbulutso 4:2-3,5-6; 5:11; 4:8)

Mngelo amatanthauza kuti *mtumiki kapena wotumidwa*. Angelo ndi mizimu ya Mulungu ya moyo. Ngati mlengi, angelo samaonekera kwa munthu, pokhapokha akatumidwa pantchito imene ayenera kuwonekera.


Mfumu ya kumwamba inapanga angelo isanapange anthu. Mawu a Mulungu amanena kuti: "angelo onse anafuula ndi chimwemwe" (Yobu 38:7) pamene amayang'anira Iye akulenga dziko lapansi.

Mulungu anapatsa angelo ake nzeru zomudziwa, zomumvera, zomuyamika ndiponso zomutumikira Iye kwamuyaya. Angelo sanali akapolo a Mulungu. Mulungu sanakakamize Angelo kumulambira Iye, chimodzimodzinso ndi mmene anachitira ndi anthu. Iye amafuna omutumikira akhale osangalala ndi okonzeka kumutumikira mwaufulu.

Baibulo limanena za mngelo m'modzi wapamwamba amene Mulungu anam'patsa nzeru zakuya, kukongola, ndi mphamvu.

Ngati mukudziwa nkhani ya mngelo ameneyu, ndiye kuti mukudziwa kumene tchimo linayambira.





# Gawo la sewero 11
## Dziko la Mdima

Lusifala anali m'modzi wa angelo a Mulungu ndipo dzina lake limatanthauza Wonyezimira.Mabuku a aneneri amamufotokoza Lusifala ngati "wokomera muyeso ndi chizindikiro, wodzala ndi nzeru wokongola wangwiro." (Ezekieli 28:12)[7]

Kenaka Lusifala anayamba kuziona yekha m'malo moyang'ana Mfumu ndi Mlengi. Kwa nthawi yoyamba, chinthu cholengedwa chinakhala chodzikweza! Ataphimbika m'maso ndi kukongola kwake komanso nzeru zake, ndi kuyiwala amene anamulenga, Lusifala ananena mu mtima mwake,

> "Ndidzakweza mpando
> wachifumu pamwamba pa
> nyenyezi za Mulungu...
> Ndizakwera pamwamba
> pa mitambo;
> Ndizafanana ndi
> Wam'mwambamwamba."
> (Yesaya 14:13-14)

Lusifala anafuna kukhala mfumu. Anafuna zofuna zake zichitike osati zofuna za Mulungu.

Tchimo linalowa mu dziko.

Lusifala anakopa gawo limodzi la angelo mu kuukira kwake, koma Mulungu, amene sangalolere tchimo, anamuponyera kunja kwa mzinda wake wakumwamba.

Dzina la Lusifala linasintha kukhala Satana, kutanthauza kuti wosokoneza. Iye amatchedwanso mdyerekezi, kutanthuza kuti wonama. Angelo oyipa amatchedwa ziwanda.

Mu malo a chinsinsi a mdima, Mulungu anakonza ndende ya mdyerekezi ndi ziwanda zake. Malo amenewo amatchedwa gahena komanso Nyanja ya Moto. Ndi malo olekanirana ndi Mulungu kwamuyaya, malo amene oukira sadzavutitsanso. Tsiku limodzi Satana ndi ziwanda zake zonse adzatsekeredwa kwamuyaya mu ndende imeneyo, koma onse sali kumeneko.

Ndiye kodi mizimu yoyipayi inapita kuti pamene Mulungu anaiponyera kunja?

Inalowerera mu mlengalenga wa dziko la pansi. M'menemo mdyerekezi anawagawa angelo ake m'maudido. Ngati sangalamulire kumwamba, adzalamulira dziko lapansi! Nchifukwa chake Malembo oyera amamutcha Satana "mkulu wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu, wakuchita tsopano mwa ana asakumvera." (Aefeso 2:2)

Mdierekezi ndi ziwanda zake samaonekera kwa ife, koma alikodi. M'mene sitidziwira m'mene amaonekera, sitidziwanso zolinga zawo zakuda ndi zoyipa. Adzagwiritsa ntchito njira zonse zonama kuti awakope anthu kuti alowe mu ufumu wawo wa mdima ndi wa imfa. Sadzakusiyani kufikira, atakuwonongani.

> Satana yemwe adzionetsera
> yekha ngati mngelo
> wakuunika. (2 Akorinto 11:14)

> Mdani wanu mdierekezi, monga
> mkango wobuma ayendayenda
> ndikufunafuna wina akamlikwire.
> (1 Peter 5:8)

Tsopano tiyeni tibwerere ku nkhani ya makolo athu oyamba.





## Gawo la sewero 12
# Njoka

Miyoyo ya Adamu ndi Hava inali yodzaza ndi kuchita zambiri ndi kukhala ndi zolinga.

Tsiku lililonse linali lodzaza ndi zodabwitsa pamene amatulukira zinthu zambiri m'munda, amasamalira zolengedwa ndi zomera, ndipo amasankhamo zakudya.

Madzulo aliwonse anali osangalatsa kwambiri chifukwa Mlengi-Wawo-Mwini anawapatsa ulemu powayendera yekha. Amakonda bwanji kuyenda ndi kuyankhula naye! Mwamuna uyu ndi mkazi wake anali osangalala m'munda mwao m'mene amakhala.

Koma Satana sanali osangalala. Amamuda Mulungu ndipo amawada olengedwa awiriwa amene amaonetsera chifanizo cha Mulungu.!

Choncho mdierekezi, amene analephera kulanda ufumu wa kumwamba, anakonza zotenga malo pa dziko lapansi. *Akanangomutenga Adamu, mkulu wa mtundu wa anthu, kusankha kuphwanya Lamulo la Mulungu. Koma sakanamuyesa adamu pamaso mpamaso…*

Tsiku lina Hava anamva mawu.

Sanali Adamu. Sanalinso Mulungu.

Inali njoka!

Kwa Hava, chokwawa choyankhula chinali chinthu china chimene anachitulukira. Analibe ganizo lakuti Mdani wa Mulungu amagwiritsa ntchito njoka. Komanso sanadziwe kuti Satana amkafuna kumugwiritsa ntchito iye kuti amuyese Adamu kuti aphwanye Lamulo la Mulungu.

Njoka inali itadikira modekha, maso ake amamuyang'ana mkaziyo. Kenaka, pamene mpata unapezeka, njoka inamulizira likweru,

> "Ea! Kodi anatitu Mulungu, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu'?" (Genesis 3:1)


Satana anafuna Hava awakaikire mawu a Mulungu. Anafunanso kuti iye aganize kuti Mulungu amawabisira china chake chabwino iye ndi mwamuna wake.

> cha mtengo wapakati pa munda, ndipo musaugwire, kapena mudzafa,"

> "Kufa simudzafai; chifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mudzadya umenewu, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati Mulungu wakudziwa zabwino ndi zoyipa." (Genesis 3:2-5)

Kodi Hava adzachita chiyani?





# Gawo la sewero 13
## Chisankho

Mulungu anamupatsa Adamu ndi Hava ufulu wosankha pakati pa kuchita chifuniro Chake kapena kuchita chifuniro chawo.

AMBUYE anadziwa chimene chinali chabwino kopambana kwa olengedwa apaderawa amene anawapanga m'chifanizo chake. Iye amafuna Adamu ndi Hava amukhulupirire Iye, ngakhale samamvetsa ulamuliro Wake.

Mulungu amaona zoopsa za kutsogolo, zotsatira za tchimo, nchifukwa chake anamuuza Adamu kuti:

> "Koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoyipa, usadye umenewo, chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu." (Genesis 2:16-17)

Koma tsopano njoka inamuuza Hava,

> "Kufa *si*mudzafayi." (Genesis 3:4)

Kodi Hava akhulupirire ndani - Mlengi wake kapena cholengedwa?

Izi ndi zimene zinachitika:


> Pamene mkazi anaona chipatsocho kuti chinali chabwino kudya, chokoma m'maso, cholakalakika komanso chopatsa nzeru, anatengapo ndipo anadya.
>
> Napatsanso mwamuna wake amene ali naye, nadya iyenso. (Genesis 3:6)

Mkazi anadya! Mwamuna anadya!

Hava anadya chipatso choletsedwacho chifukwa ananamizidwa ndi bodza la Satana. Adamu anadyanso potsatira maganizo ake mwa kusamvera Mulungu.

M'malo momvera Mlengi wawo woyera ndi wachikondi, munthu anadzipereka kwa mdani.

Makolo athu oyamba anachimwa.





## Gawo la sewero 14

# Tchimo ndi Manyazi

Adamu anali wamkulu wa mtundu wa anthu. Mulungu anapereka kwa iye lamulo lakuti asadye chipatso cha mtengo wa chidziwitso cha zabwino ndi zoyipa. Adamu ndi mkazi wake Hava atangodya chipatso choletsedwa ndi pamene anayamba kumva zotsatira zowawa za chisankho chao choyipa.

> Ndipo maso ao onse awiri anatseguka, ndipo anazindikira kuti anali maliseche, ndipo adasoka masamba a mkuyu, nadzipangira matewera. (Genesis 3:7)

Manyazi ndi nthumanzi zinagwira mitima yao ndipo Anamva kuti sanali oyera, mkati ndi kunja komwe.

Tchimo linabweretsa manyazi.

Adamu ndi Hava asanaphwanye lamulo la Mulungu, amadziwa Mulungu ndipo "analibe manyazi." (Genesis 2:25) Iwo ankamva bwino kukhala ndi Mlengi wawo, kuonetsera chifaniziro Chake, ndi kukhala abwenzi ake.

Koma pamene anadya kuchokera ku mtengo wa chidziwitso cha zabwino ndi zoyipa, anakhala ndi manyazi.

Mmalo mwa ulemu anakhala amanyazi.

Anayesera kuphimba manyazi awo ndi masamba a mkuyu, koma kuyesera kwawo sikukanakhoza kuthetsa mabvuto awo. Anayesera mu nzeru zawo pofuna kuchotsa tchimo limene linatenga malo m'miyoyo mwawo. Anasowa chochita kuti abwezeretse ulemu umene anautaya.


Anali masana.

Mlengi wawo oyera ndi wachikondi amabwera madzulo kudzawayendera madzulo. Maganizo omuona Iye amawapangitsa nthumanzi m'matupi mwawo.

Kodi adzanena chiyani kwa iwo?

Kodi iwo adzanena chiyani kwa Iye?





## Gawo la sewero 15

# Kufa mu Uzimu

Asanachite kusamvera pamaso pa Mulungu, Adamu ndi Hava amasangalala kumuona bwenzi lawo- Mlengi nthawi iliyonse imene amabwera kudzawayendera.

Tsopano anali ndi mantha.

> Ndipo anamva mawu a Yehova Mulungu ali nkuyendayenda m'munda nthawi yamadzulo: ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wake pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda. (Genesis 3:8)

Monga ana osamvera amene amabisalira makolo awo, Adamu ndi Hava anayesera kubisalira Mlengi wawo.

> Koma AMBUYE anamuitana Adamu, "Kodi uli kuti?"
>
> Iye anayankha, "Ndinakumvani m'munda ndipo ndinali ndi mantha chifukwa ndinali maliseche; ndipo ndinabisala."
>
> Ndipo Mulungu anati: "Anakuuza ndani kuti unali maliseche? Kodi wadya kuchokera mu mtengo umene ndinakulamula kuti udsadye?"
>
> Mwamuna anati: "Mkazi amene munamuika muno ndi ine—
>
> Anandipatsa chipatso chochokera mu mtengo, ndipo ndinachidya."
>
> Kenaka AMBUYE anati kwa mkazi, "Ndi chiyani ichi wapanga?"
>
> Mkazi anati: "Njoka inandinamiza, ndipo ndinadya" (Genesis 3:9-13)

Ndi chifukwa chiyani Adamu ndi Hava anafuna kubisalira Mulungu? Chifukwa anachimwa. Chifukwa chiyani amanamizira ena pa tchimo lawo? Chifukwa anali ndi manyazi.

Adamu ndi Hava sanaonetserenso chifanizo cha Mulungu choyera, m'malo mowonetsera Kuyera ndi chikondi cha Mlengi wawo, iwo tsopano anawonetsera kuukira kwa Satana ndi matama.

Banja loyamba linakhala ngati nthambi yothyoka ku mtengo wa moyo.

Tchimo lawo linathetsa ubwenzi wawo ndi mfumu ya dziko.


Mu uzimu, iwo anafa. Tchimo lawo linawalekanitsa ndi Gwero la moyo wosatha.

Mu umunthu, anali ndi moyo, koma ichi chinali chiyambi cha kukalamba. Mphamvu ya imfa inalowa m'matupi mwawo.

Ndipo kodi chinayambitsa imfa imeneyi ndi chimaliziro ndi chiyani?

Tchimo.





## Gawo la sewero 16

# Temberero

Pachiyambi cha mbiri ya anthu, Mulungu ndi munthu amakhala pamodzi.

Mtendere ndi chisangalalo zinalipo. Kenaka munthu anaphwanya lamulo la Mulungu.

Tsiku lomwelo Adamu ndi Hava anachimwa, Mulungu analengeza zina mwa zotsatira za mtsogolo za tchimo lawo.

Kwa mkazi Ananena:

> "Udzasauka pakubala, udzakhumba mwamuna wako, ndipo iye adzakulamulira iwe." (Genesis 3:16)

Tchimo lisanachite ufumu m'moyo wawo, Hava amakondwa mu chikondi ndi chisamaliro cha Mwamuna wake, koma tsopano chikhalidwe chawo chopakika ndi uchimo chidaonjezera mkwiyo ndi zowawa ku chimwemwe cha m' banja.

Kenaka, Mulungu anamuuza mwamuna,

> "Nthaka ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe; m'kusauka udzadyako masiku onse a moyo wako. Minga ndi mitula idzakubalira iwe; ...mthukuta la nkhope yako udzadya chakudya, kufikira kuti udzabwerera kunthaka, chifukwa kuti m'menemo unatengedwa: chifukwa kuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko udzabwerera. (Genesis 3:17-19)

Chifukwa cha tchimo lawo, Adamu ndi Hava, anataya ulamuliro wawo pa dziko lapansi. Dziko lawo lidzakhala ndi minga, zowawa, chisoni, matenda ndi imfa.

Ena mwa ife ndife ozolowera mazunzo oterewa, moti timangovomereza kuti zikhale choncho. Koma Kodi zinakonzeka choncho pachiyambi kuti thengo la maluwa onukhira lizikhala ndi minga zobaya? Kapena pakulandira mphatso pa kubereka udzikhalaponso ululu waukulu? Kapena kwa iwo olengedwa mu chifanizo cha Mulungu akalambe ndi kufa? Ayi. Mulungu sanakonze chiyambi cha chilengedwe chomenyana chokha. Zinali chifukwa cha tchimo la munthu kuti dziko lapansi likhale pansi pa themberero la Mulungu.

Munthu anachimwa ndipo munthu ayenera kufa. Lamulo la tchimo linafunikira imfa.


Imfa ndi kulekana. Tchimo limabweretsa zotsatira zowawa zitatu:

> 1. Imfa ya ku uzimu: Mzimu wa munthu umalekana ndi Mulungu.
> 2. Imfa ya ku thupi: Mzimu wa thupi ndi moyo umalekana ndi thupi. (komanso ndi okondedwa ake.)
> 3. Imfa yamuyaya: Mzimu wa moyo ndi thupi umasiyana ndi Mulungu kwamuyaya mu ng'anjo ya moto.[8]

Munthu alibe njira yodzipulumutsa yekha ku themberero la uchimo.

Kodi panali chiyembekezo?





## Gawo la sewero 17

# Lonjezo

Satana anaba chuma chapadera cha Mfumu, koma Mfumu inali ndi dongosolo la chinsinsi yochibwezeretsa. Chifukwa ndipo limemene mfumu inakonza kuti ilipire linali lochuluka kwambiri, ngakhale ziwanda kapena anthu sankamvetsa dongosolo lake mpaka litakwaniritsidwa.

Pa tsiku lomwelo Satana anagwira mtundu wa anthu, Mulungu ananena kwa njoka,

> "Chifukwa wachita ichi, ndiwe otembeleredwa opambana ndi zinyama zonse, ndi zamoyo zonse za m'thengo: Udzikwawa ndi pa mimba pako, ndipo udzadya fumbi masiku onse a moyo wako." (Genesis 3:14)

Nthawi imene Mulungu analenga njoka, zinali ndi miyendo. Chifukwa njoka inagwiritsidwa ntchito ndi Satana kuchimwitsa anthu, Mulungu anaitemberera kuti idzikwawa pansi. (Kodi mumadziwa kuti njoka zonse zinali zofanana ndi nsato zinali ndi timatudza pansi pa kungu lawo timene tinali timiyendo kalelo?) Popanga njoka kukhala zirombo zapansi kwambiri, Mulungu anapereka chikumbutso ku banja la munthu kuti tsiku lina adzapondereza Chinjoka Chokalambacho chotchedwa Mdierekezi kapena Satana." (Chibvumbulutso 12:9)

Kenaka Mulungu ananena kwa Satana, amene anagwiritsa ntchito njoka,

> "Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbewu yako ndi mbewu yake; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chitende chake." (Genesis 3:15)

Umodzi mwa uneneri oyamba mwa mauneneri amene Mulungu adzawawonetsera, pang'ono ndi pang'ono mu dongosolo lake lopulumutsira anthu kwa Satana, ku uchimo ndi ku imfa. Koma kubisira Satana ndi otsutsa dongosolo lake, mfumu inayika uneneri mu m'ndandanda wa malamulo.

Mulungu analonjeza kutumiza Mpulumutsi ku dziko lapansi- *mwana wobadwa kwa mkazi*.

Mpulumutsi adzakhala ndi amayi ake, koma sadzakhala ndi abambo ake.

Adzadziwika ngati Messiah, kutanthauza kuti wosankhidwa.

Satana adzamenya Chitendene cha Messiah, koma Messiah adzaphwanya mutu wa Satana.

Kodi zonsezi zimatanthauza chiyani? Patsogolo Mfumu idzalongosola zonse bwino, koma pamenepo Mulungu anapereka chiyembekezo kwa Adamu ndi Hava.


Patadutsa zaka zikwi zochuluka, m'modzi mwa aneneri adalemba,

> Anthu amene anayenda mu mdima aona kuwala kwakukulu …
>
> Namwali adzaima! Nadzabala mwana wam'muna
>
> nadzamutcha Immanuel— 'Mulungu ali nafe.' (Yesaya 9:2; 7:14)

Mfumu idzawombola[9] chuma chake chapadera.

Koma chidzakhala cha mtengo wotani?





# Gawo la sewero 18
## Nsembe Yoyamba

Kodi mukukumbukira zimene Adamu ndi Hava anachita atadya chipatso choletsedwa? Anapanga zofunda za masamba a mkuyu.

Kodi anamva bwino ndi zofundazo pamaso pa Mlengi- oweruza wawo? Ayi! Anachita manyazi ndipo anatsutsika. Analibe njira yodzikometsera pamaso pa Mulungu.

Choncho Mulungu anawachitira chinachake.

> Yehova Mulungu anapangira Adamu ndi mkazi wake Malaya azikopa nawaveka iwo. (Genesis 3:21)

Anapanga nsembe yoyambirira ndani? Mulungu anapanga.

AMBUYE anapha nyama zina, anapanga zovala za zikopa, ndipo anaveka Adamu ndi Hava. Pochita choncho, Mulungu amawaphunzitsa phunziro la chilungamo, chifundo ndi chisomo cha Mulungu.

Tiyeni tione mawu atatu ofunikirawa

> *Chilungamo*. Onani nyama zakufa. Chifukwa chiyani Mulungu anadzipereka nsembe? Anachita choncho kuti aonetse Adamu ndi Hava kuti lamulo la tchimo ndi imfa liyenera kugwiridwa. Tchimo lawo liyenera kulangidwa mwa imfa. Chimenecho ndi chilungamo.
>
> *Chifundo*. Yang'anani kwa Adamu ndi Hava. Kodi Mulungu anawapha? Ayi. Mulungu anapereka nyama kuti zife m'malo mwawo. Iyi inali njira ya Mulungu yolangira uchimo wawo posawalanga iwowo. Chimenecho ndi chifundo.
>
> *Chisomo*. Tsopano yang'anani ku zovala zokongola za Adamu ndi Hava. Kodi anthu awiriwa akaphwanya lamulo amayenera kulandira mphatso imeneyi? Ayi! koma Mulungu anawonetsa chifundo chake powaveka ndi zikopa za nyama zoperekedwa nsembe. Chimenechi ndi chisomo.

Chifukwa cha zimene AMBUYE anawachitira, Adamu ndi Hava anakhalanso osangalala ndi Mulungu!


Mwazi wa nyama unabisa Uchimo wawo. Adamu ndi Hava anayenera kufa pa tsiku limene lija, koma nyama zosalakwa zinafa m'malo mwa iwo.


Mikanjo ya zikopa za nyama inaphimba manyazi awo. Kachiwirinso, Adamu ndi Hava anamva bwino pa maso a Mulungu.

Patadutsa zaka zikwizikwi m'modzi mwa aneneri aMulungu adalemba,

> Ndidzakondwa kwambiri mwa Yehova, moyo wanga udzakondwelera mwa Mulungu wanga; pakuti iye wandiveka ine ndi zovala za chipulumutso ndikundifunda chofunda chachilungamo. (Yesaya 61:10)

Mulungu Yekha ali ndi njira yokonzeranso ochimwa kukhala abwino.





## Gawo la sewero 19

# Kuchotsedwa

Pamene Mulungu anachotsa angelo owukira kuchoka kumwamba, kuweruzidwa kwawo kunatsimikizika. Mizimu iyi ngakhale inali mukuwunikira inalibe chowiringula cha tchimo lawo. Koma tchimo- linawononga anthu, Ambuye anali ndi cholinga kuti awatengenso ngati akadamukhulupirira iye.

Komabe, tchimo lili ndi zotsatira zake. Ngati m'mene Mulungu anamuchotsera Satana ndi angelo ake oyipa ku paradizo wakumwamba, ndiye tsopano Mulungu waturutsa mwamuna ndi mkazi wake mu paradizo wa dziko lapansi.

> Ndipo anamuchotsa munthuyo; nakhazika Makerubi cha kum'mawa kwake kwa munda wa Edene, ndi lupanga lamoto lakuzungulira ponsepo, lakusunga njira yaku mtengo wa moyo. (Genesis 3:24)

Mtengo wapakati pa Munda unali wosiyana ndi mitengo ina. Okhawo omwe anali abwino anakatha kudya kuchokera kumtengowo. Adamu ndi Hava sanalinso wolungama. Anali atachimwa ndipo anayenera kukalamba ndi kufa.

Mlengi wathu wamkulu ndi woyera. Izi zikutanthauza kuti ndi woyeretsetsa, wangwiro, wabwino, ndi wolungama. Chifukwa cha chilengedwe chake ndi malamulo ake oyera, ayenera kulanga tchimo ndi imfa — kulekanitsidwa ndi wopereka Moyo.

Anthu ena amaganiza kuti Mulungu ndi wa "mphamvu" kuti akhoza kuphwanya malamulo ake omwe. Tangoganizani mu chipinda choweruziramo milandu pamene oweruza milandu akukana kukakamiza malamulo a zamalo. Kodi munganene kuti oweruza milandu wamtundu wotere ndi wopambana? Tangoganizani za masewero ampira wamiyendo pamene wankulu woyimbira masewero a kunyalanyaza malamulo a masewero. Kodi munganene woyimbira masewero kuti ndi wabwino kapena oyipa?

Satana amafuna Hava akhulupirire kuti mlengi wake sakanakakamiza malamulo ake, kuti sakanalanga ophwanya malamulo ndi imfa. Koma mfumu yolungama ndi yoweruza za kumwamba ndi zapadziko amasunga mawu ake nthawi zonse.

Mulungu ndi wamkulu. Mukhoza kumukhulupirira.

> Chilungamo ndi chiweruzo ndiwo maziko a mpando wachifumu wanu; Chifundo ndi choonadi zitsogolera pankhope panu. (Masalmo 89:14)


Wonani ngati mungathe kuyankha chilapi ichi: *Kodi ndi chiyani chomwe Satana ndi anthu amapanga chimene Ambuye Mulungu sangapange?*

Ili ndi yankho lamwini wake Mulungu:

> "Sindizaipsa chipangano changa; kapena kusintha mawu otuluka m'milomo mwanga …
> Ndinalumbira kamodzi m'chiyero changa." (Masalmo 89:34-35)

Mfumu ya zakumwamba ndi zapadziko singabwerere pa mawu ake.





# Gawo la sewero 20

## Ana oyamba

Kunja kwa munda, dziko linakhalabe malo okongola, koma linalinso ndi zinthu zoyipa ngati minga zobaya, tizilombo tosowetsa mtendere, matenda ndi zovuta zambiri. Panalibenso ubale pakati pa zinyama ndi munthu. Chakudya chinali chovuta kupeza. Adamu ndi Hava amayenera kugwira ntchito molimbika kuti adye.

Analinso ndi nthawi ya chimwemwe ndi chisangalalo.

> Ndipo mwamunayo anadziwa mkazi wake Hava: ndipo anatenga pakati: nabala Kaini, ndipo anati: ndalandira munthu kwa Yehova." (Genesis 4:1)

Hava anamutcha mwana woyamba wa dziko lapansi kuti Kaini, kutanthauza kuti Cholowa. Chuma chapamwamba chochokera kwa Mulungu! Mwina amaganiza kuti mwana wake akanakhala mpulumutsi wolonjezedwa, koma mosakhalitsa anadzindikira kuti mwana wake anali osamvera ndi wodzikonda—ngati makolo ake!

Patapita nthawi, pamene mwana wawo wamamuna wachiwiri anabadwa, Hava anamutcha iye Abele, kutanthauza kuti *kupepuka kapena chabe*, Adamu ndi Hava sakanatha kubereka mwana osachimwa amene akanapulumutsa anthu ku machimo awo.

M'malo molingalira kuyera kwa Mulungu, Ana a Adamu ndi Hava analingalira za chikhalidwe cha uchimo wa makolo awo.

> Adamu … anali ndi ana amuna ndi akazi … angati iye, m'chifaniziro chake. (Genesis 5:4,3)

Yang'anani chithunzi. Kodi mukuona Kaini akulanda m'bale wake chipatso? Akupanga zinthu ngati makolo ake, amene anadya chipatso chimene sichinali chawo. Ngati nthenda yopatsirana, Adamu ndi Hava adapatsira ana awo tchimo.

> Adamu atachimwa, uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa uchimo; kotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa. (Aroma 5:12)


Mwambi wa dziko la Africa umanena kuti *Khoswe amabereka ana amene amatha kukumba ngati iye*. Mwambi wa ChiArab umanena kuti *mwana wa Bakha amayandama*.

Makolo athu oyamba atachimwa, anakhala ngati nthambi yothyoka kuchoka pa mtengo. Monga momwe mtengo ndi tsamba pa nthambi yotchoka imakhudzidwira, aliyense ochoka mu banja la Adamu anakhudzikanso ndi tchimo lake

Adamu atafa, Mneneri mfumu Davide analemba,

> Onani ndinabadwa mphulupulu: ndipo mai wanga anandilandira m'zoyipa. (Masalmo 51:5)

Izi sizingatisangalatse, koma tikudziwa kuti ndi zoona.





## GAWO LA SEWERO 21
# KUPEMBEDZA KWA OCHIMWA

Adamu ndi Hava anali ndi ana ambiri, koma mawu a Mulungu amafotokoza kwambiri za ana aamuna awiri oyamba.

> Abele anali m'busa wa nkhosa, koma Kaini anali mlimi. (Genesis 4:2)

Kaini ndi Abele anali olimbikira ntchito.

Onse ankamudziwa Mlengi wawo.

Onse ankafuna Mulungu awalandire komanso.

kupembedza kwawo. Vuto la onse linali tchimo.

Sikuti anangobadwa ochimwa, koma amakhalanso monga ochimwa. Tsiku lililonse amaganiza, amayankhula, ndipo amachita zinthu mu njira zimene sizimaonetsera chiyero ndi chikondi cha Mulungu. Zimenezi Mfumu mu Buku lake imadzitcha kuti tchimo.

> Pakuti onse anachimwa, naperewera pa Ulemelero wa Mulungu. (Aroma 3:23)

Kodi panali njira imene Mulungu akanakhululukira Abele ndi Kaini kuwayesa olungama pamaso Pake? Inde, koma sizikanakhala zophweka.

> Ndipo opanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka. (Ahebri 9:22)

Lamulo losasweka lija la dziko-lamulo la tchimo ndi imfa- linayenera kuchitika. Tchimo likuyenera kulangidwa ndi imfa. Ndi chifukwa chake Njira ya chikhululukiro cha Mfumu inakwaniritsidwa ndi imfa. Pamene ochimwa amayenera kufa, Mulungu amalandira magazi a nyama za mitundu ina monga nkhosa.

Nkhosa simayenera kukhala yamawanga, yodwala kapena yachilema. Imayenera kukhala yathanzi ndi yonenera. Imayenera kukhala nkhosa yosadetsedwa.

Nkhosa imaphedwa ndi kuwotchedwa imafa m'malo mwa ochimwa. Nkhosa imatenga malo a ochimwa.

Tsiku lina onse awiri anabweretsa nsembe kwa Mulungu, koma m'modzi yekha anabweretsa nsembe yoyenera.

> Ndipo panali atapita masiku, Kaini anatenga zipatso kukapereka nsembe kwa Yehova.
>
> Ndiponso Abele anatenga iyenso mwana oyamba wa nkhosa zake ndi mafuta omwe. (Genesis 4:3-4)

Mukuganiza ndi nsembe iti imene Mulungu anailandira?





## Gawo la sewero 22
# Lamulo la Nsembe ya Tchimo

Onani anyamatawa. Onani zimene akufuna kupereka kwa Mulungu. Onani pa maguwa.

Guwa linali malo okwezedwa, kawirikawiri amapangidwa ndi miyala kapena dothi. Anali malo a imfa. Guwa limalumikiza zopereka za anthu a pansi ndi Mulungu kumwamba komanso pakati pa Mulungu ndi munthu. Chilichonse choperekedwa pa Guwa chimayenera kuwotchedwa ndi moto.

Mulungu amatsata chilungamo nthawi zonse koma amafuna kuwonetsa chifundo. Kodi akanachita bwanji zonse? Akanalanga bwanji tchimo opanda kulanga ochimwa? Patapita nthawi yaitali kuchokera pa Kaini ndi Abele Mulungu anamuuza Mneneri Mose:

> Pakuti moyo wa nyama umakhala m'mwazi; ndipo ndakupatsani uwu pa guwa la nsembe, uchite chotetezera moyo wanu; pakuti ochita chotetezera ndiwo mwazi, chifukwa cha moyo wake. (Levitiko 17:11)

> Ndipo ayike dzanja lake pa mutu pa nsembe yopsereza; ndipo idzalandiridwa m'malo mwake, imutetezere. (Levitiko 1:4)

Kodi *Chiyeretso chimatanthauza* chiyani? Zikutanthauza kulipira mtengo woyenera Chiombolo kuti machimo achotsedwe, ayeretsedwe, ndi kukhululukiridwa. Mu nthawi za chipangano chakale, Mulungu anawauza anthu kuti adzalandira mwazi wa ana ankhosa, nkhosa zazimuna, mbuzi, ng'ombe zazimuna, nkhunda ngati malipiro amachimo awo. Magazi amenewa adzapereka dipo—kutchinjiriza tchimo—koma kufikira patsiku limene Mulungu adapereka nsembe yoyenera kuti alipire mtengo woyenera ndi wovomerezeka ndi lamulo la tchimo ndi imfa.


Tsopano yang'anani Kaini ndi zimene akufuna kupereka kwa Mulungu. Kusankha kwabwino kwa zipatso ndi masamba! M'mene zinamuvutira kugwira ntchito kuti apeze choperekachi! Koma sizinakatchinjiriza machimo ake chifukwa zinalibe magazi, palibe malipiro a imfa.

Yang'anani kwa Abele ndi zopereka zake. Kuona komvetsa chisoni! Kamwana ka nkhosa kakuyembekezera kufa. Kodi mukumuona Abele akuyika dzanja lake pa mutu pa mwana wa nkhosa? Chifukwa Abele amakhulupirira dongosolo la Mulungu, Mulungu anatenga machimo onse a Abele ndi kuwayika mwa mwana wa nkhosa. Abele akumuyamikira AMBUYE kuti ngakhale iye, Abele, akuyenera chilango cha imfa, Mulungu avomera magazi a mwana wa nkhosa ngati chotchinjiriza ku tchimo.

Chilamulo cha Mulungu chimafuna kuti ochimwa onse alandire chilango cha imfa koma Mulungu mu chilungamo ndi chifundo analandira nsembe ya mwana wa nkhosa mmalo mwao: pa malo ophera nsembe yopsereza ndipo pophera nsembe yaochimwa pamaso pa Yehova; ndipo yopatulikitsa." (Levitiko 6:25)

Lamulo lopereka tchimo linamumasula Abele ku lamulo la tchimo ndi imfa.

Koma nanga bwanji Kaini?





## Gawo la sewero 23
# Kuvomerezedwa ndi Kukanidwa

Kodi mukuona guwa la Kaini? Kodi pali chiyani? Mbewu zofota. Tsopano yang'anani pa guwa la Abele. Kodi pali chiyani? Magazi ndi phulusa.

Kodi Mulungu amawaganizira chiyani awiriwa ndi kupembedza kwawo?

> Yehova ndipo anayang'anira Abele ndi nsembe yake, koma sanayang'anira Kaini ndi nsembe yake. (Genesis 4:4-5)

Sitinawuzidwe m'mene Mulungu anavomereza nsembe ya Abele ndi kukana nsembe ya Kaini.[10] Mawu a Mulungu amati:

> Ndi chikhulupiriro Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yoposa ija ya Kaini, m'mene anachitidwa umboni nayo kuti anali olungama nachitapo umboni Mulungu pa mitulo yake. (Ahebri 11:4)

Chifukwa anakhulupirira mwa AMBUYE ndi dongosolo lake, Abele anakhululukidwa ndi kuwerengedwa olungama. Iyi inali mphatso ya Mulungu kwa Abele.

Mulungu anali ataika machimo a Abele mwa mwana wa nkhosa. Mwana wa nkhosa anafa m'malo mwa Abele. Magazi a mwana wa nkhosa anakhetsedwa ndipo thupi lake linawotchedwa mpaka phulusa. Mkwiyo wa kulungama kwa Mulungu pamwamba pa tchimo unali utagwa pa mwana wa nkhosa m'malo mwa kugwa pa Abele. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anakhutitsidwa ndi nsembe yoperekedwa ndi Abele ya mwana wa nkhosa? Chifukwa inalozera za kubwera kwa mpulumutsi amene adzalipire ngongole ya machimo a dziko lapansi. Chifukwa chachikhulupiriro chake mu dongosolo la Malungu Abele anali mu ubale wabwino ndi Mulungu. Patapita nthawi, Abele atamwalira, m'malo mosiyana ndi Mulungu kwa Muyaya anakakhala ndi Mulungu ngati bwenzi lake. Lamulo la nsembe lidagonjetsa ndi lamulo la tchimo ndi imfa.

Kaini anamufikira Mulungu ndi mapemphero ake, koma ananyalanyaza lamulo la Mulungu lomwe limanena kuti tchimo liyenera kulangidwa ndi imfa. Kaini anali wa chipembedzo, koma sanali mu ubale wabwino ndi Mulungu. Lamulo la tchimo ndi imfa linamukakamira iye ngati mtambo wakuda. Akanapanda kukhulupirira Mulungu ndi dongosolo lake sakanamudziwa Mulungu ngati bwenzi lake. Akanamuona Mulungu ngati oweruza wake.

Anthu ena amayesa kumuteteza Kaini ponena kuti: "Kaini anali mlimi. Anabweretsa zomwe anali nazo." Koma Mulungu samafuna zomwe anali nazo. Kaini anakatha kugulitsa mbewu zina ndi kupeza mwana wa nkhosa m'modzi pa ana ankhosa a Abele, kapena anakayika dzanja lake pa mwana wa nkhosa wa Abele ndi kupembedza pa guwa la nsembe lomwelo.

Kodi Kaini akadachita chiyani?

Kodi akanalapa ndi kufika kwa Mulungu ndi chopereka choyenera?





## Gawo la sewero 24

# Kupha koyambirira

MULUNGU anakana chopereka cha Kaini. Komabe Mulungu amamukonda iye ndipo anamufunsa kuti alape.

Kodi kulapa kumatanthauza chiyani?

Mutakhala kuti mukufuna kuyenda ulendo wopita ku mzinda wina wake. Mutazindikira kuti mwakwera sitima yolakwika mutakwera kale. Kodi mungatani? Mukhoza kuvomereza kulakwitsa kwanu, kutsika mu sitima, ndi kukwera mu sitima yoyenerera. Izi ndi zomwe kulapa kumatanthauza.

Kulapa kumatanthauza ku sintha maganizo anu; kutembenuka kuchoka kuzomwe zili zabodza ndi kudzipereka ku zomwe zili zoona. Kulapa pa maso a Mulungu sikutanthauza kuti ndiyenera kudzilanga ndekha chifukwa cha machimo anga. Zimatanthauza kuti ndiyenera kuliona tchimo langa m'mene Mulungu amaliwonera.

Mulungu amafuna Kaini alape—kusiya kukhulupirira munjira yake ndi kukhulupirira ndi kutsatira njira ya Mulungu.

> Ndipo Kaini anakwiya kwambiri, ndipo nkhope yake inagwa.
>
> Ndipo Yehova anati kwa Kaini, ukwiiranji? Yagweranji nkhope Yako? Ukachita zabwino, sudzalandilidwa kodi? Ukaleka kuchita zabwino, uchimo ubwatama pa khomo: kwa iwe kudzakhala kulakalaka kwake, ndipo iwe udzamulamulira iye." (Genesis 4:5-7)

Kaini anali wodzikweza kwambiri kuti sakanatha kulapa. Anali *atachititsidwa manyazi ndi mchimwene wake*! *Amatha kuchotsa manyazi ndi kubwezeretsa ulemu munjira yake!*

> Tsopano Kaini anati kwa m`bale wake Abele, "Tiye tipite ku munda." Ndipo pamene anali m'mundamo, Kaini anamupanga chiwembu m`bale wake ndi kumupha.
>
> Kenako Ambuye anati kwa Kaini, "Kodi mchimwene wako Abele alikuti?"
>
> "Sindikudziwa," anayankha. "Kodi ndine osunga mchimwene wanga?"
>
> Ndipo anati: wachita chiyani? Mawu a mwazi wa mphwako andifuulira ine ku nthaka." (Genesis 4:8-10)

Moyo ndi mzimu wa Abele unali utapita kukakhala ndi AMBUYE, koma thupi lake linabwerera kufumbi kufikira tsiku la mtsogolo pamene Mulungu adzasandutse fumbiro kukhala thupi la mphamvu lolemekezeka kwa nthawi yosatha.

Ndipo kwa Kaini, Mulungu anamupatsa mwayi wina olapa, koma anakana.

> Ndipo Kaini anatuluka pa maso pa Yehova. (Genesis 4:16)

Mu mzimu wa kuukira ndi kudzikuza, Kaini anasuntha kupita kuvuma ndi kukamanga mzinda. Iye ndi mkazi wake anali ndi ana ambiri. Zidzukulu zawo zinapanga zida zachitsulo zoyambirira ndi zida zoyimbira. Mibadwo ya Kaini inali ya nzeru kwambiri, koma simadziwa AMBUYE.





## Gawo la sewero 25

## Kuleza mtima ndi chilango

Patadutsa mibadwo khumi kuchoka pamene Adamu adachimwa Mulungu anapereka uthenga womvetsa Chisoni kwa Mtundu wa anthu:

> Kuipa kwa munthu kunali kwakukulu pa dziko la pansi, ndiponso kuti lingaliro lonse lamaganizo a mitima yawo linali loyipabe lokhalokha. (Genesis 6:5)

Koma banja limodzi padziko lapansi limakhulupirirabe Mulungu.

> Nowa anapeza kukonderedwa pamaso pa AMBUYE.
>
> Ndipo Mulungu ananena kwa Nowa, "ndiika mathero kwa anthu onse, pakuti dziko lapansi ladzaza ndi chiwawa. Taonani ndidzaononga iwo pamodzi ndi dziko lapansi. Udzipangire wekha chingalawa cha mtengo wa njale; upangemo zipinda muchingalawamo, ndipo upake ndi utoto mkati ndi kunja. Kupanga kwake ndi kotere …" (Genesis 6:8,13-15)

Bwato la milingo itatu lalikulu, lalitali ngati bwalo losewererapo mpira ndi theka, lidali ndi zipinda zokwanira kusunga mtundu uliwonse wa nyama ziwiriziwiri ndi nyama magulu asanu ndi awiri anyama ziwiriziwiri operekera nsembe ya tchimo. Chombo chidakhala ndi malo opumira ndi chipata chimodzi chachikulu.

Kwa zaka zikwi, Nowa anamanga chombo, pamodzi ndi mkazi wake, ana ake aamuna atatu ndi akazi awo. Pamene amagwira ntchito, Nowa anachenjeza dziko za chilango cha Mulungu, koma anthu anamunyoza.

Pamapeto chombo chinapangidwa. Banja la Nowa linasungiramo zinthu. Mulungu anabweretsamo zinyama, zokwawa, tizirombo, ndi mbalame. Zinali zosangalatsa pamene zimalowamo, ndipo zinakhala mzipinda zake zochuruka.

Nowa ndi banja lake analowamonso. Kodi munalowanso wina kuti apezemo chitetezo? Ayi. Mulungu anatseka chitseko. Mitambo yambiri inakutila dziko, mphenzi inang'anima ndipo ziphaliwali zinalira.

> Tsiku limenelo akasupe onse akuya anatumphuka ndi zipata zakumwamba zinatseguka. Ndimvula inagwa pa dziko kwa masiku makumi anayi usana ndi usiku. Mwezi wachiwiri, tsiku la khumi ndi asanu ndi awiri la mwezi, tsiku lomwelo akasupe onse amadzi aakulu anasefuka, ndi mazenera akumwamba anatseguka. Ndipo mvula inali pa dziko lapansi masiku makumi anayi usana ndi usiku. (Genesis 7:11-12)

Inali ngozi yaikulu kwambiri mu mbiri. Kupatula miyoyo isanu ndi itatu mu chombo, anthu onse anafa.

Dziko la anthu odzikuza losakhulupirira linadziwa choona mochedwa.

Zofukulidwa za munthaka zimatsimikizira zolembedwa za Mawu a Mulungu. Kuchokera ku Sahara mpaka ku Himalaya, za pansi pa Nyanja, zikhoza kufukulidwa mu zipululu zazikulu za pa dziko lapansi ndi m'mapiri.

Mu chifundo chake Mulungu ndi wodekha, koma mu chilungamo Chake adzaweruza tchimo.





## Gawo la sewero 26
# Kuyamba kwa Tsopano

Choncho kodi ndi chiyani chimene chinachitika kwa Nowa ndi banja lake, ndi nyama zake mu chombo?

Iwo anapulumuka ku chilango cha Mulungu.

> Ndipo Mulungu anakumbukira Nowa ndi zamoyo zonse, ndi nyama zonse zimene zinali pamodzi naye m'chingalawamo; ndipo Mulungu anatumiza mphepo pa dziko lapansi, naphwa madzi. (Genesis 8:1)

Chombo chachikulu chinayandama, pamapeto chinakaima pa Ararat,

phiri lalikulu kwambiri lokhala ndi msonga ziwiri ku mvuma kwa Turkey.

Katatu Nowa anatumiza nkhunda kuti ikaone ngati ingakapeze malo ouma. Nthawi yoyamba nkhunda inangobwera. Nthawi yachiwiri nkhunda inabwerera kwa Nowa ndi tsamba la mtengo wa azitona ku kamwa kwake. Ulendo wachitatu nkhunda siinabwerere. Inapeza malo okhala! Nowa anadziwa kuti inali nthawi yoti atuLukamo mu chombo. Chaka chinadutsa chiyambireni chigumula.

Kodi mukudziwa chinthu choyamba chimene Nowa anachitira banja lake ndi nyama zake atatuluka mu chombo?

> Ndipo Nowa anamanga guwa la nsembe la Yehova, anatengapo nyama zodyedwa zonse ndi mbalame zodyedwa zonse napereka nsembe zopsereza pa guwapo.  Ndipo Yehova anamva chonunkhira chakukondweretsa …(Genesis 8:20-21)

Chilungamo cha Mulungu ndi chifundo chake sichinasinthe. Tchimo linafunikabe malipiro a imfa. Ndi chifukwa chake Nowa anakhetsa mwazi wa nyama zosalakwa ndi kuziwotcha matupi awo pa guwa, zitapachikidwa pakati pa kumwamba ndi dziko lapansi, pakati pa Mulungu ndi Munthu. Nsembe zoterezi zimaloza kwa Mesiya wosachimwa amene adzabwera tsiku lina kudziko lapansi kudzapereka malipiro enieni a tchimo.

Kenaka, Mulungu anamulamula Nowa ndi banja lake:

> "Mubalane, muchulukane, mudzadze dziko la pansi." (Genesis 9:1)


AMBUYE anapanganso pangano ndi Dziko Lapansi:

> "Ndiyika utawaleza wanga mtambomo, ndipo udzakhala chizindikiro chapangano lopangana ndi ine ndi dziko la pansi… Ndipo madzi sadzakhalanso konse chigumula chakuononga za moyo zonse." (Genesis 9:13,15)

Ngati chizindikiro cha pangano, Mulungu anatulutsa utawaleza wa ulemerero oyenda mumlengalenga mwa mtambo. Mulungu analonjeza kuti sadzatumizanso chigumula pa dziko lonse lapansi. Utawaleza umatikumbutsa kuti, kaya kulanga kapena kuteteza,

Mulungu adzasunga malonjezo Ake nthawi zonse.





## Gawo la sewero 27

# Nsanja ya kudzitama

Ngakhale pamene anadalitsidwa ndi chiyambi cha tsopano, patapita mibadwo yochepa anthu ambiri anatembenukira Mulungu ndikuyenda njira zawo.

Mwa chitsanso. Mulungu anawauza anthu kuti amwazikane pa dziko.” (Genesis 1:28; 9:1) Kodi munthu anachita chiyani?

Malembo amanena kuti:

> Apa dziko linali ndi chiyankhulo chimodzi,
>
> Pamene anthu anayamba kupita cha kumvuma, anapeza chigwa cha Sinala (pano dziko la Iraq) ndipo anakhala pamenepa, ananena pakati pawo “tiyeni tiwumbe njerwa ndikuziwotcha bwino”
>
> Anagwiritsa ntchito njerwa m’malo mwa miyala komanso phula m’malo mwa simenti ndi mchenga.
>
> Kenako anati “bwerani tiyeni tidzimangire mzinda ndi nsanja yofika kumwamba kuti tikathe kudzipangira tokha dzina ndi kusamwazika pa dziko lonse.” (Genesis 11:1-4)

Malo mokweza dzina la Mulungu anthu omangawa anafuna kuti anthu akweze iwo, monga Satana anagwidwa ndi mzimu wa kudzitama ndi kuwukira.

Pofuna kumanga nsanja yofika kumwamba anali ngati opemphera a lero amene amafuna kufika kumwamba ndi mphamvu zawo zokha. Monga Kaini anthuwa anali opemphera, koma anayiwala njira ya Mulungu ya kukhululuka ndi chilungamo, sanakhulupirire Mulungu ndi chikonzero chake.

Ndiye Ambuye Mulungu anati:

> “Bwerani tiyeni tipite pansi ndikuwapatsa  ziyankhulo zosiyana, apa sadzatha kumvesetsana wina ndi mzake.”
>
> Mu njira iyi Mulungu anawamwaza pa dziko lonse lapansi ndipo izi zinathetsa kumanga kwa mzindawo. Ichi ndi chifukwa chake mzindawu anawutcha Babele (malo achisokonezo), chifukwa ndi apa pamene Mulungu anawasokonezera anthu powapatsa ziyankhulo zambiri. Choncho kuwamwaza padziko lapansi. (Genesis 11:7-9)

Popereka chiyankhulo ku banja kapena mtundu uliwonse Mulungu anayimitsa ntchito yomanga mzindawo.Anthuwo analibe chisankho china koma kusiya Babele ndi kudzaza dziko lapansi, monga Mulungu analamulira.

Athuwo sanamalize nsanja yawo koma chikonzero cha Mulungu chinachitika mwa nthawi yake.





## Gawo la sewero 28

# Mulungu ayitana Abrahamu

Mibadwo inadutsa chichokereni nthawi ya mneneri Nowa. Satana anagwira mayiko mwamphamvu, zinawoneka choncho.

M'malo mokhulupirira Mulungu anthu anakhulupirira zipembedzo zawo. Mayiko ena analambira dzuwa m'malo mwa amene analenga dzuwalo. Ena analambira Mwezi.

Ichi chinali chaka cha 1925 asanabadwe Yesu.

Mudera la kumpoto chakumvuma kwa dziko la Arabia munali kukhala wachikulire wina dzina lake Abramu. Kenako Mulungu anasintha dzina lake kukhala Abrahamu, kutanthauza "Bambo wa makamu."

Abrahamu anali ndi zaka 75 ndipo Sara, mkazi wake anali ndi zaka 65 ndipo analibe mwana. makolo awo ndi anthu okhala nawo pafupi anali opembeza mafano. Kutamanda zinthu zolengedwa m'malo mwa olenga.

Tsiku lina Mulungu ananena kwa Abrahamu:

> "Siya dziko lako, anthu ako ndi banja la bambo ako ndipo upite komwe ndidzakuwonetsere,"
>
> "ndidzakupanga iwe kukhala mtundu opambana ndipo ndidzakudalitsa, ndidzapanga dzina lako kukhala lopambana ndipo udzakhala mdalitso ndidzadalitsa okudalitsa ndi aliyense okutemberera ndidzamutemberera ndipo anthu onse adziko lapansi adzadalitsidwa kudzera mwa iwe." (Genesis 12:1-3)

Mulungu ankafuna kupanga pangano ndi Abrahamu. Ngati atasiya banja la bambo ake ndi kupita malo osawadziwawa, Mulungu adzamuchitira iye zinthu ziwiri zopambana:

1. Mulungu adzamupanga Abrahamu kukhala tate wopambana
2. Kudzera mu mtundu umenewo Mulungu adzadalitsa anthu a mitundu yonse.

Ngati Abrahamu atatsatire ndi kukhulupirira Mulungu adzakhala tate wa mtundu umene adzachokera aneneri, malembo ndi mpulumutsi wa dziko lapansi.


Kodi Abrahamu anachita chiyani?

> Mwa chikhulupiriro atayitanidwa kupita ku malo amene analonjezedwa, anamvera ndi kupita, ngakhale sankadziwa komwe anali kupita. (Ahebri 11:8)

Sizinali zophweka kwa Abrahamu ndi mkazi wake kusiya abale awo ndi kutembenukira zipembedzo za mabanja awo. Koma anasankha kulandira chidzudzulo kuchoka kwa abale kuti iwo athe kutsatira Mulungu m'modzi oona.

Kukhulupirira ndi kumvera Mulungu sikophweka nthawi zonse koma ndi kwabwino koposa nthawi zonse.





## Gawo la sewero 29

# Osunga lonjezo

Abrahamu ndi mkazi wake anali atakalamba ndipo analibe ana. Ndipo Mulungu analonjeza Abrahamu kukhala tate wa mtundu waukulu.

Kodi Abrahamu anatani ndi lonjezo losathekali?

> Abrahamu anakhulupirira Mulungu ndipo anatchedwa olungama ndiponso bwenzi la Mulungu. (Yakobo 2:23; Genesis 15:6)

Monga obwera mbuyo mwa Adamu, Abrahamu anali ochimwa, koma monga Abelo ndi Nowa, Abrahamu amapereka nsembe za uchimo kwa Mulungu. Chifukwa anakhulupirira Mulungu ndi malonjezo ake Mulungu anamutcha olungama kumwamba. Ndipo anamupatsa mphoto ya moyo osatha. Sara anakhulupiriranso ndipo anayesedwa kulungama.

Koma ndikovuta kudikira.

Anakhala mudziko la Palestine kwa zaka khumi, kuyembekezera ndi kupemphera kuti Sara akhale ndi pakati ndipo anaganiza zomuthandiza Mulungu chikonzero chake. Potsatira mwambo wa nthawi imeneyi, Sara anapereka wa ntchito wake Hagara kwa Abrahamu. Abrahamu anagona naye ndipo anakhala ndi pakati ndi kubereka mwana wa mwamuna anamutcha Ismayeli.

Patadutsa pafupifupi zaka khumi ndi zitatu, Abrahamu anali ndi zaka 99 ndipo Sara anali ndi zaka 89. Mulungu anawaonekeranso iwo nawauza iwo kuti adzakhala ndi mwana amene adzamutcha Isake. Mulungu ananenanso kwa Abrahamu,

> Za Ismayeli… Ndamdalitsa iye, ndipo ndidzamchulukitsa… koma pangano langa ndidzalimbikitsa ndi Isake, amene Sara adzakubalira iwe nthawi omwe yino chaka cha mawa." (Genesis 17:20-21)

Patatha chaka Sara anabereka Isake, mwana wa lonjezo.


Onani chithunzichi, kodi mukuwona Abrahamu ndi mkazi wake akuyangana kumwamba? Akuthokoza Mulungu pa kukhulupirika kwake. Patapita nthawi Hagara ndi Ismayeli anatumizidwa kutali, koma Mulungu anali wabwino kwa iwo.

> Mulungu anali ndi nyamatayu pokula mu chipululu cha Parana. Anakhala katswiri wa uta ndipo mayi ake anakonza ukwati wa iye ndi mtsikana waku Aigupto. (Genesis 21:20-21)

Ismayeli anasanduka atate wa Aluya, amene Mulungu waadalitsa munjira zambiri.

Pa Isake, anatsala kwawo kusamalira ziweto za bambo ake. Nthawi zina Isake anathandiza bambo ake kusankha nkhosa yathanzi kuyipha ndikuyiwotcha nsembe pa guwa chifukwa cha machimo awo. Koma palibe pakati pawo, Isake ngakhale Abrahamu anali kudziwa nsembe imene Mulungu anali kufuna.





## Gawo la sewero 30

## Yesero lalikulu

Mulungu anakonza dongosolo lowombola anthu kumachimo ndi imfa pogwiritsa ntchito Abrahamu ndi mwana wake komanso aneneri ena powonetsera chithunzithunzi chake chowombola anthu. Mulungu anakonza zakuyesa chikhulupiriro cha Abrahamu kufika pa mathero a mlingo pomufunsa iye kuchita chinthu choopsa. Chinthu choti sichinapange tanthauzo mpaka pa mathero a yeseroli.

Pa nthawi imeneyi ya moyo wake Abrahamu anali ndi chikhulupiriro chosasunthika mwa Mulungu. Abrahamu anali kumudziwa Mulungu. Anali kudziwa kuti Mulungu ndi wabwino komanso wachilungamo. Koma, kodi Abrahamu akanatha kumukhulupirira ndi kumumvera ngakhale pamene Mulungu amamuuza zinthu zooneka zoipa?

Iyi ndi nkhani yochokera mu malembo:

> Patapita nthawi Mulungu anayesa Abrahamu.
>
> Anati kwa iye "Abrahamu!"
>
> Ndili pano! Anayankha.
>
> Kenako Mulungu anati "tenga mwana wako Isake, amene umamukonda ndipo upite ku chigawo cha Moriya, ndipo ukamupereke mwanayo ngati nsembe yopsereza pa limodzi mwa mapiri amene ndidzakuwuza."
>
> Mawa wa tsiku lotsatira lake, Abrahamu anadzuka ndikukonzekera bulu wake. Anatenga awiri mwa kapolo ake ndi mwana wake Isake. Atatha kupeza nkhuni zokwanira, nsembeyo ananyamuka kupita ku malo amene Mulungu anamuuza.
>
> Pa tsiku lachitatu Abrahamu anayang'ana kumwamba ndi kuona malo ena patali. Ananena kwa akapolo ake "khalani pompano ndi bulu pamene ine ndi nyamatayu tikupita uko., tikapembedza kenako tidzabwerera kwa inu."
>
> Abrahamu anatenga nkhuni za nsembezo ndi kuziyika pa mwana wake Isake ndipo iye ananyamula moto ndi mpeni.
>
> Pamene awiriwa anali kupitirira. Isake anayankhula ndi kunena kwa bambo ake Abrahamu. "Bambo?"
>
> "Inde mwana wanga?" Abrahamu anayankha
>
> Isake anati: "Moto ndi nkhuni tili nazo, koma nkhosa ya nsembeyo ili kuti?"
>
> Abrahamu anayankha "Mulungu yekha adzapereka nkhosa ya nsembe yopserezayi, mwana wanga"
>
> kenako awiriwa anapitiriza limodzi. (Genesis 22:1-8)





## Gawo la sewero 31

# Mwana wotaidwa

Kodi munamva zomwe Abrahamu anawauza a ntchito ake asanakwere phiri la nsembe?

> “Tikapembeza kenako tidzabwerera kwa inu.”

Kodi mwana wa Abrahamu anakabwerera bwanji ngati anali kukaphedwa ndi kuwotchedwa thupi? Malembo akuti:

> Abrahamu anali ndi maganizo a kuti Mulungu anali wakuthekera kudzutsa akufa. (Ahebri 11:19)

Mulungu analonjeza kuti Isake adzakhala tate wa fuko lopambana (Mtundu umene mpulumutsi adzachokere.) Mulungu sanganame. Izi zinali zokwanira kwa Abrahamu.

Panthawiyi kodi Isake anali kuganiza chani? Anali kudziwa kuti anali ochimwa ndipo anayenera kufa chifukwa cha machimo ake. Komanso anali kudziwa kuti Mulungu atha kulola mlowammalo. *Koma tsikuli anali kupita kumalo a nsembe opanda nkhosa. Sizinali ndi tanthauzo.* ndipo Isake anati kwa bambo ake:

> “Moto ndi nkhuni ndi izi koma nkhosa ya nsembe yopserezayo ili kuti?
>
> Abrahamu anati “Mulungu yekha adzapereka nkhosa ya nsembe yopserezayi, mwana wanga.”

Tsopano tiyeni tipitirize nkhaniyi.

> Atafika pa malo amene Mulungu anamuuza, Abrahamu anamanga guwa ndikusanja nkhuni pamwamba pake. Anamanga mwana wake Isake ndikumugoneka pa guwali pamwamba pa nkhuni.
>
> Anatambasula dzanja lake natenga mpeni kuti azinge mwana wake.
>
> Koma angelo wa Mulungu anayitana kuchoka kumwamba. “Abrahamu! Abrahamu!”
>
> “Ndili pano” anayankha.
>
> “Usayike dzanja lako pa nyamatayo” iye anati “Usachite chilichonse kwa iye, pano ndadziwa kuti umawopa Mulungu. Chifukwa sunakanize ine mwana wako. Mwana wako mmodzi yekhayo.” (Genesis 22:9-12)

Abrahamu ndi mwana wake anakondwera! koma nanga nsembe yofunikayo?

> Abrahamu anayang’ana mwamba ndipo mosachedwa anawona mwana wankhosa atakodwa m’malunje ndi nyanga zake. (Genesis 22:13)

Mwana wa Abrahamu wapulumutsidwa ku chilango cha imfa.

Mulungu wapereka mlowam’malo!





## Gawo la sewero 32
# Zithunzi ndi uneneri

Kodi Mulungu anapulumutsa bwanji mwana wa Abrahamu amene amayenera kufa? Anapereka nyama yosalakwa kuti ikafe m'malo mwa iye.

> Abrahamu anayang'ana mwamba ndikuona mwana wankhosa atakodwa m'malunje ndi nyanga zake. Anapita pompo ndikutenga nkhosayo ndikuyipereka ngati nsembe yopsereza malo mwa mwana wake. (Genesis 22:13)

Zochitika zonsezi zinapereka chithunzi cha chikonzereo chake chotumiza pa dziko lapansi mpulumutsi woyera amene adzakwaniritsa zoyenera za chilamulo cha tchimo ndi imfa. Ndi kupulumutsa ochimwa amitundu yonse ya dziko lapansi,

> Ndipo Abrahamu anawatcha malowa *"Mulungu adzapereka"* ndipo mpaka lero limatchedwa kuti "phiri la Mulungu adzapereka." (Genesis 22:14)

Ndi chifukwa chiyani anatchula dzina loti "Mulungu adzapereka" osati "Mulungu wapereka"

Kodi Mulungu anangopereka dipo lowombola chabe?

Potchula phirilo *"Mulungu adzapereka"*, mneneri Abrahamu adalosera tsiku limene pa phiri lomwelo, Mulungu mwini adzapereka nsembe ya mwazi wa mtengo wapatali ndipo Mulungu adzavomereza iyi kukhala kulipira kwa machimo onse a dziko lapansi. Kuti aliyense okhulupirira mu nsembe imeneyi sadzatayika koma kukhala ndi moyo wosatha.

Zaka 1900 zitadutsa Abrahamu chiperekereni nsembe ya nkhosa pa guwa, mpulumutsi wolonjezedwayo adzayang'ana m'mbuyo pa nthawi yosayiwalikayi ndi kunena kuti:

> "Tate anu Abrahamu anasangalala poganizira tsiku ili, analiwona ndipo anakondwera." (Yohane 8:56)

Pamene utsi wa nkhosayo unali kupita kumwamba. Mulungu anamupatsa Abrahamu masomphenya a nsembe yopsereza imene idzachitike pa phiri lomwelo. Modabwitsa yankho la Abrahamu ku funso la mwana wake "kodi nkhosa ili kuti?" linakhala ndi tanthauzo lakuya.

> "Mulungu mwini adzapereka *nkhosa ya nsembe* yopsereza, mwana wanga." (Genesis 22:8)

Kwa Abrahamu ndi mwana wake, Mulungu anali asanapereke Mwana Wa Nkhosa, anapereka nkhosa.

Kodi *Nkhosa* inali kuti?

Pa nthawi yoyenera Mulungu mwini adzapereka yankho.





## Gawo la sewero 33

# Mulungu wokhulupirika ndi woyera

Kodi mukukumbukira malonjezo awiri amene Mulungu anapanga kwa Abrahamu? Choyamba Mulungu anati:

> "Ndidzakupanga iwe kukhala mtundu opambana." (Genesis 12:2)

Mulungu anasunga mawu ake, Abrahamu anabala Isaki, Isaki anabala Yakobo ndipo Yakobo anali ndi ana amuna khumi ndi awiri. Ndipo awa anasanduka mitundu 12 ya Israyeli. Mulungu ananenanso kuti:

> "Anthu onse a dziko lapansi adzadalitsidwa kudzera mwa iwe." (Genesis 12:3)

Mulungu anasunganso mbali iyi ya lonjezo. Pogwira ntchito ndi mtundu wopatulikawu ndiponso wowukira, Mulungu anafuna kuwonetsa anthu onse a dziko lapansi chimene iye ali ndi momwe ochimwa angabwerere kwa iye. Nthawi zonse zimene Mulungu anateteza mtunduwu. Amateteza chikonzero chake chodalitsa inu ndi ine. Pakuti ananenera malembo oyera kuti, mpulumutsi olonjezedwa adzachoka ku mtundu uwu.

Chikonzero cha chinsinsi cha Mulungu chinali kupitirirabe.

Pafupifupi zaka 1500 Yesu asanabadwe Mulungu anayitana Mose wochokera ku mbadwo wa Abrahamu. Kuti akhale mneneri wake, Mose analemba mabuku asanu oyambirira mu Baibulo. Mulungu anagwiritsanso ntchito Mose kutsogolera mtundu wa Abrahamu zikwi zikwi kuchoka ku Aigupto. Komwe anali pa ukapolo kwa zaka zambiri, Mulungu yekha anawatsogolera kudutsa mu chipululu ndi mtambo kupereka mthunzi masana ndi moto kupereka kuwala usiku. Ndi dzanja lake la mphamvu, anatsegula njira yothawira kwa iwo pa Nyanja yofira, kuwapatsa mkate ochokera kumwamba ndi madzi kuchokera ku thanthwe. Ndikuwabweretsa pa phiri la Sinai.

Phiri ili lili pamunsi pa phiri limene Mulungu anawauza anthuwo kuti:

> "mudzakhala mu ufumu wanga... ndi mtundu oyera!" (Eksodo 19:6)

Mulungu anali kufuna kuti mtunduwu ukhale oyera. Opatulidwa kwa iye ndi osiyana ndi mitundu yozungulira. Koma anthuwo sanamvetse tanthauzo lakukhala oyera. Sanadziwone iwo ngati ochimwa opanda pake. Iwo anayesa adzakhala okonderedwa ndi Mulungu. Kuti awaphunzitse phunziro la mkwiyo wake pa tchimo, Mulungu anabwera pansi kudzera mu kugwedeza, kuyaka kwa moto wotentha ndi kulira kwa malipenga kwakukulu.

> Ndipo phiri la Sinai linafuka monsemo, popeza Yehova anatsikira m'moto pamenepo; ndi utsi wake unakwera ngati utsi wa mng'anjo, ndi phiri lonse linagwedezeka kwambiri. Ndipo pamene liu la lipenga linamveka linakulira-kulira, Mose ananena, ndi mulungu anamyankha ndi mawu." (Eksodo 19:18-19)

Mulungu anapereka kwa Adamu lamulo limodzi.

Nthawi inafika yopereka malamulo khumi kwa mtundu watsopano.





## Gawo la sewero 34
# Malamulo khumi

Anthu ambiri a mtunduwu ankaganiza kuti anali oyenera kukhala anthu a Mulungu, choncho Mulungu anawapatsa malamulo khumi. Koyamba mu mawu ogwedeza pa phiri la Sinai kenako pa miyala iwiri.

Tiyeni tiwerenge malamulo khumi. (kumanja kuchokera pa Eksodo 20)

Mulungu anamuuza Mose kuti onse atsate malamulo khumi.

> "Otembereredwa ndi munthu amene sasunga chilamulo ichi." (Deuteronomo 27:26)

Kodi mukuganizira kuti anthu anaganiza bwanji atamva malamulowa? Kodi mukuganiza anali kumvabe kukhala oyenera? Nanga bwanji inu? Kodi mukuganiza ndinu oyenera kukhala mu ufumu wopambana wa Mulungu?

Werenganinso lamulo loyamba. Kodi mumayika Mulungu patsogolo nthawi zonse? Ngati ayi, mwalephera kusunga lamuloli. Werengani lamulo lachisanu. Ngati simumvera makolo anu muli olakwa pa maso a Mulungu. Tsopano onani lamulo la chisanu ndi chitatu. Ngati munatengapo chinthu choti sichanu kapena kubera mayeso mwalakwira lamulo limeneli. Kodi munanenako bodza. Mwalakwira lamulo la chisanu ndi chinayi. Lamulo lomaliza limanena kuti ndi kulakwa kufuna katundu wa mwini. Mulungu amawona ngakhale tchimo la mu mtima mwathu.

Kodi ndi machimo angati anachititsa kuti ubale pakati pa Adamu ndi Hava uwonongeke ndi Mulungu? Tchimo limodzi! Lamulo la chiyero la Mulungu silinasinthe.

> Amene asunga chilamulo chonse koma kulephera lamulo limodzi waphwanya malamulo onse. (Yakobo 2:10)


Mulungu ndi oyera ndipo sangalekerere tchimo. Kodi mungafune kukhala m'chipinda chimodzi ndi nkhumba yokufa imene ili kuvunda? Umu ndi momwe tchimo lili kwa Mulungu monga kumwaza mafuta onunkhira sikungayeretse chipindachi, palibe mphamvu za chipembedzo zimene zingayeretse mitima yathu.

Monga kalilole amene amandiwonetsa kuda pa nkhope yanga, malamulo a Mulungu amandiwonetsa machimo a mumtima wanga, monga kalilole sangayeretse nkhope yanga, malamulo sangayeretse mtima wanga.

> Palibe amene adzatchedwa olungama pamaso pake posunga lamulo koma kudzera mu chilamulo tidzakhala ozindikira tchimo. (Aroma 3:20)

Ngati timadzitenga kuti ndife oyera, koma sitili oyenera kukhala ndi Mulungu kumwamba.

Tisowekera Mpulumutsi.


1. Usakhale nayo milungu ina koma ine ndekha.
2. Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chili chonse. Chifukwa Ine Ndine Mulungu wako.
3. Usatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe.
4. Udzikumbukira tsiku la sabata likhale lopatulika.
5. Uzilemekeza atate wako ndi amako.
6. Usaphe.
7. Usachite chigololo.
8. Usabe.
9. Usanamizire mnzako.
10. Usasirire nyumba yake ya mnzako, mkazi wa mnzako kapena chilichonse chimene si chili chako.



## Gawo la sewero 35
## Zithunzi zowonjezera

Malamulo khumi anapereka chilamulo chomveka bwino pa chabwino ndi choyipa. Ichi chinali chinthu chabwino. Koma chilamulo cha Mulungu chinabweretsanso nkhani zoyipa. Chilamulochi, chinawonetsa munthu kuti ali mu mavuto aakulu. Chifukwa cha machimo awo akuyenera kufa ndi kusiyana ndi Mulungu.

Nkhani yabwino inali yakuti Mulungu anali kulandilabe nsembe yamwazi wa nkhosa, ng'ombe, mbuzi ndi nkhunda kufufuta machimo awo. Choncho, tsiku lomwe Mulungu adamupatsa malamulo Mose, anamuuza kuti:

> "panga guwa ndikupereka nsembe yako yopsereza."
> (Eksodo 20:24)

Kodi mukuona Mose atayika dzanja lake pa mutu wa nkhosa? Kodi mukuona anthu amene akweza manja awo kuloza mwana wankhosayu? Chifukwa akukhulupirira Mulungu ndi njira yake ya chikhululukiro, machimo awo akuyikidwa pa mwana wa nkhosa wosalakwa. Nkhosayi idzaphedwa pa guwa. Mwazi umene udzakhetsedwa udzafufuta machimo a anthuwo. Kenako thupi la nyamayi lidzawotchedwa mpaka phulusa. Phulusali lidzaonetsa chimene Mulungu wachita ndi machimo awo. Akhululukidwa!

Koma chikhalidwe chopereka mwazi wa nyama kuti machimo akhululukidwe chinali chabe chithunzi cha zomwe Mulungu anali kufuna.

> Nsembe za nthawi ya chikhalidwechi zinali kubwerezedwa-bwerezedwa, chaka chilichonse. Koma nsembezi sizinakwanitse kupereka kuyera kwa anthu amene anali kubwera kudzapembedza.
>
> Zikanakwaniritsa kupereka kuyera, nsembezi bwenzi zitatha. Chifukwa opembedza anakakhala oyeretsedwa kwa muyaya. Ndipo mzimu wokumva kulakwa bwenzi utasoweratu.
>
> Koma zotsutsana ndi zomwe zinachitika. Nsembe za chaka chilichonse zinawakumbutsa za machimo awo chaka chilichonse. Chifukwa ndi kosatheka mwazi wa ng'ombe ndi mbuzi kuchotsa machimo. (Ahebri 10:1-4)


Zinyama sizinalengedwe mu chifanizo cha Mulungu.

Mtengo wa mwana wankhosa siwofanana ndi munthu. Monga simungatenge galimoto la dongo kupita kogulitsa magalimoto ndikuyipereka kulipira galimoto yeniyeni. Choncho mwazi wa nkhosa sungalipire mphoto ya chilamulo cha tchimo ndi imfa.

Nsembe yoyenera inali kufunika.

Pamene nsembe za nyama zimalephera kuchotsa machimo a dziko, zinawapatsa ochimwa chithunzi cha amene angathe kuchotsa machimowo.





# Gawo la sewero 36
## Ulosi owonjezera

Pamene nthawi ya kubwera kwa Yesu inali kuyandikira, Mulungu anauza aneneri ake kuti alembe maulosi ambiri a Mpulumutsi-Mfumuyo. Awa ndi ochepa mwa maulosi akalewo:

*Namwali adzakhala ndi pakati ndipo adzakhala ndi mwana wa mwamuna….*
*— Mneneri Yesaya 7:14*

*"Koma iwe Betelehemu... mwa iwe mudzatuluka amene adzakhala mfumu. Amene wachokera kunthawi za kale."*
*— Mneneri Micah 5:2*

*Pakuti kwa ife mwana wabadwa kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa, ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lake, ndipo adzamutcha dzina lake wodabwitsa, wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate wosatha, kalonga wa mtendere.*
*— Mneneri Yesaya 9:6*

*Mulungu wanu adzabwera kudzakupulumutsani kenako maso akhungu adzatseguka makutu a osamva adzatseguka ndipo olumala adzadumpha….*
*— Mneneri Yesaya 35:4-6*

*Iye anasendezedwa ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa…*
*— Mneneri Yesaya 53:7*

*"Alasa manja ndi mapazi anga."*
*— Mneneri David, Masalmo 22:16*

Mpulumutsi olonjezedwa ali kudza!
Koma abwera liti? Ndipo iye adzakhala ndani?
Kodi maulosi adzakwaniritsidwa bwanji?



# Gawo 2

## Mfumu ikwaniritsa chikonzero chake

— Chipangano chatsopano —



## Gawo la sewero 37

## Nkhani ya mfumu ipitirira

Kodi ndime yoyamba ya buku la Mfumuyi inakusangalatsani bwanji? kodi munaphunzira Chiyani mu chipangano cha kale?

Chipangano chimatanthauza *mgwirizano*. Mulungu asanapereke chipangano chatsopano anati:

> "nthawi ikubwera…imene ndidzapereka chipangano *cha tsopano*." (Yeremiya 31:31)

Mu chipangano choyamba ndi anthu ake, Mulungu anawapatsa malamulo ambiri kuwaonetsa kuyera kwake ndi kuchimwa kwawo, Anawapatsanso zithunzi ndi maulosi a mpulumutsi amene anali kubwera. Mu chipangano cha kale aneneri analosera za mtsogolo. Mesiya-Mfumu adzabwera. Koma mu chipangano cha tsopano tikuwerenga:

Mesiya-Mfumu yabwera!

Chipangano cha tsopano muli uthenga wabwino, mu chiluya uthengawu amawutcha Injil. Kutanthauza nthano yabwino. Uthengawu umayamba ndi mawu awa:

> Buku la kubadwa kwa Yesu Khristu, mwana wa Davide, Mwana wa Abrahamu. Abrahamu anabala Isake; ndi Isake anabala Yakobo; ndi Yakobo anabala... (Mateyu 1:1-2)

Potchula dzina la aliyense malembo akulemba ndandanda wa otsatira mbadwo wa Abrahamu kufikira pa Yesu. Mulungu adzasunga lonjezo lake lodalitsa anthu a mitundu yonse potumiza mpulumutsi kudzera mwa mtundu wa Abrahamu.

Chipangano cha tsopano muli mabuku anayi a uthenga wa bwino. Chifukwa chiyani anayi? Bwanji osangokhala limodzi? Mu chipangano cha kale Mulungu anamuuza Mose.,

> "Mfundo ya nkhaniyi idzakhazikitsidwa ndi umboni wa anthu awiri kapena atatu." (Deuteronomo 19:15)

Kuti atsimikize nkhani ndi uthenga wake. Mulungu anasankha osati anthu awiri kapena atatu, koma anthu anayi kuti alembe ma umboni osiyana a moyo wa Mesiyayu. Maina awo anali, Mateyu, Mariko, Luka ndi Yohane. Monga atolankhani anayi olemba nkhani imodzi. Onse akufotokoza nkhani imodzi. Koma kuchokera mu ngodya zosiyana.

Chipangano cha tsopano chili ndi mabuku 27. Buku la machitidwe, lolembedwa ndi Luka limatiuza zimene zinachitika Mesiya atamaliza ntchito yake. Mulungu anamulimbikitsa Paulo (amene anali chigawenga), Yakobo ndi Yuda (abale ake a Yesu), Petulo ndi Yohane (msodzi) kulemba mabuku otsala mu chipangano cha tsopano. Buku lililonse limationetsera zambiri za mfumuyo ndi zikonzero zake pa onse amene akonda iye.

Iyi ndi nkhani yotsatira.





## Gawo la sewero 38

# Nkhani ya Mariya

Nthawi inafika, patapita zaka zikwi-zikwi akukonzekera, Mulungu anali atatsala pang'ono kutumiza Mesiya-Mfumu pa dziko lapansi. Koma kodi iye adzakhala ndani? Ndipo kodi adzabwera bwanji?

> Mu nthawi ya Mfumu Herodi mfumu ya ku Yudeya… Mulungu anatuma mngelo Gabriyeli ku Nazareti mzinda wa mu Galileya, kwa namwali amene amayenera kukwatiwa ndi mwamuna otchedwa Yosefe. Wotsatira wa mtundu wa Davide. Dzina la namwaliyu linali Mariya.
>
> Mngeloyo ananena ndi iye "usaope, Mulungu wakukondera, udzakhala ndi pakati ndi kubereka mwana wa mwamuna" ndipo udzamutcha dzina lake Yesu, adzakhala opambana ndipo anthu adzamutcha mwana wa Mulungu wakumwamba. Ambuye Mulungu adzamupatsa mpando wa bambo ake Davide ndipo adzalamulira. Ufumu wake uzakhala opanda malire. (osatha)
>
> "Izi zizatheka bwanji?" Mariya anafunsa mngeloyo "pakuti sindidziwa mwamuna ayi?"
>
> Mngelo anayankha "Mzimu Woyera adzabwera kwa iwe ndipo oyerayu adzatchedwa mwana wa Mulungu."
> (Luka 1:5,26-27,30-35)

Kodi ndi chifukwa chiyani Gabriyeli anamutcha *"Yesu mwana wa Mulungu?"*

Ena amaganiza kuti Mulungu anatenga mkazi nakhala ndi mwana. Izi sizitanthauza choncho.

Ngati muli ochokera ku Africa ena atha kukutchulani mwana wa Africa. Kodi izi sikutanthauza kuti Africa anakwatira ndikukhla ndi mwana, ayi! Izi zikutanthauza kuti inu munachokera ku Africa.

Mesiya akutchedwa mwana wa Mulungu chifukwa anachokera kwa Mulungu. Anabwera mu banja lowonongeka ndi tchimo, la Adamu koma sanachokere kwa Adamu, iye ndi Mawu, Mzimu ndi Mwana wa Mulungu.


> Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali kwa Mulungu, ndipo Mawu ndiye Mulungu. Awa anali pachiyambi kwa Mulungu. Zonse zinalengedwa ndi iye; ndipo kopanda iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa. Ndipo Mawu anasandulika thupi nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi. (Yohane 1:1-3,14)

Kodi mukukumbukira lonjezo limene Mulungu anapanga tsiku limene Adamu anadya chipatso choletsedwa? Mulungu analengeza kuti *mwana wa mzimayi adzaphwanya mutu wa njoka.*

Mwana olonjezedwayu tsopano anali m'mimba mwa namwali.

Iye adzaphwanya mutu wa njoka imene iti idzaoneke.





## Gawo la sewero 39
# Nkhani ya Yosefe

Mariya, namwali, analonjezedwa ukwati ndi Yosefe. Mpala matabwa okhala ku Nazareti. Dera lakumalire akumpoto kwa dziko la Palestina.

Onse Mariya ndi Yosefe anali Ayuda ochokera ku mtundu wa Davide kupitirira mpaka kwa Abrahamu. Yosefe anayenera kukhala karonga koma dera lawo linali kulamuliridwa ndi Aroma. Asilikali AchiRoma ankalondera mizinda ndipo onse oganiziridwa kufuna kulanda boma amakhomedwa pa mtanda. Otolera msonkho amabera anthu. Moyo unali owawa.

Koma Yosefe anali osangalala, posachedwa adzatenga Mariya kukhala mkazi wake. Anagwira ntchito molimbika kukonza malo amene adzakhale limodzi akadzachita ukwati. Kenako tsiku lina anamva nkhani yodzidzimutsa. Mariya anali oyembekezera.

"kodi mukuganiza Yosefe anamva bwanji? Zinawoneka ngati Mariya sanali okhulupirika kwa iye.

Yosefe anasweka mtima, koma anafuna kuchita chinthu choyenera. Anayimitsa chinkhoswe mwa kachetechete chifukwa sanafuna kuchititsa Mariya manyazi.

> Ali kuganizira zimenezi. Iye anagona ndipo mngelo anamuonekera iye ku maloto.
>
> "Yosefe, mwana wa Davide", mngelo anati: "usaope kumutenga Mariya kukhala mkazi wako. Chifukwa mwana ali mwa iye ndi wa Mzimu woyera. Ndipo adzakhala ndi mwana wa mwamuna ndipo udzamutcha Yesu. Pakuti adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo."
>
> "Zonsezi zinakhala kuti zikachitidwe chonenedwa ndi Ambuye mwa mneneri, ndikuti: 'Onani! namwali adzaima ndadzabala mwana wa mwamuna, ndipo adzamutcha dzina lake Emanueli' (ndilo losandulika, Mulungu nafe.)"(Mateyu 1:20-23)

Kudandaula kwa Yosefe kunasandulika chimwemwe. *Ulemu waukulu!* Mariya adzakhala mayi wa *Mesiya olonjezedwa*, ndipo iye Yosefe adzakhala atate wake pa dzikoli.

Mesiya oyera adzakhala ndi mayi wa umunthu koma opanda bambo. Dzina lake lidzakhala Yesu kutanthauza *Mulungu amapulumutsa kapena kuti mpulumutsi*.

> Yosefe atadzuka, anachita zimene mngelo wa Mulungu analamula. Anakwatira Mariya koma anakhalabe namwali mpaka mwana wake atabadwa. Ndipo yosefe anamutcha Yesu. (Mateyu 1:24-25)

Dzanja la Mulungu linali mu zonsezi.





## Gawo la sewero 40

# Kufika

Zaka mazana asanu ndi awiri zadutsa, mneneri Mika ananenera kuti Mesiya Mfumu adzabadwa mu Betelehemu, mzinda wa kale wa Mfumu Davide.

Panali vuto, Mariya ndi Yosefe amakhala ku Nazareti, ulendo wa masiku atatu kupita kumpoto. Kodi malemba adzakwaniritsidwa bwanji?

Mulungu ali ndi zonse m'manja ake.

Pamene nthawi inafika kuti Mariya abereke mwana, mfumu ya Aroma Kayisala analamula kuti aliyense abwerere ku dera lakwawo kuti akalembetse kalembera wa msonkho. Choncho Yosefe ndi mkazi otsala pang'ono kuchirayu anachoka ku Nazareti napita ku Betelehemu.

> Ali kumeneko nthawi yoti mwana abadwe inafika ndipo anabala mwana wake oyamba wa mwamuna.
>
> Anamukutira mu zovala ndikumuyika modyetsera ngombe, chifukwa panalibe malo ku nyumba yosungira alendo. (Luka 2:6-7)

Ku Betelehemuko, mzinda odzaza ndi anthu apaulendo (mzinda wa kalembera wa msonkho) *mwana wolonjezedwa wa mzimayi wabadwa*. Uthenga wabwino ukulemba nthawi mwatchutchutchu:

> Anabereka mwana wake wa mwamuna oyamba. (Luka 2:6)

Ku mbali ya mayi wake, mwanayu anali wakhanda kwa Mariya. Koma kwa bambo ake, anali mwana wa muyaya wa Mulungu. Ndi Mawu amene analenga dzikoli, Mawu omwewo amene anagwedeza phiri la Sinai, Mawu omwewo anamveka mu kulira kwa mwanayu.

Kodi mwanayu anabadwira kuti?

Osati malo achifumu, kapena ku chipatala, kapena malo osungira alendo. Mfumu yochokera kumwamba inabadwira m'khola, momwe ana ankhosa amabadwira. Ndipo anagona modyetsera nkhosazo monga kama.


Ili linali dongosolo la Mulungu.

> Pakuti mudziwa chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti, chifukwa cha inu anakhala wosauka, angakhale anali olemera, kuti inu ndi kusauka kwake mukakhale olemera. (2 Akorinto 8:9)

Koma, kodi Mulungu sanakatha kukonzekera chisangalalo popereka ulemu pa kufika kwa mwana wake?

Iye anachita.





# Gawo la sewero 41
## Nkhani ya Abusa

TKodi Mulungu anadziwitsa ndani za kubwera kwa Mesiyayu pa dziko? Mafumu? Anthu otchuka ndi achuma? Atsogoleri a chipembedzo?

Ayi.

Anthu oyamba kulandira uthengawu anali abusa ankhosa. Amenewa anali oyang'anira nkhosa zoperekedwa nsembe pa guwa mu kachisi wa ku Yerusalemu.

> Awa anali abusa okhala kunja kuyang'anira nkhosa usiku. Mngelo anawaonekera iwo ndipo ulemelero wa Mulungu unawala pa iwo ndipo anadzazidwa ndi mantha.
>
> Koma mngelo ananena kwa iwo: "musaope ndabwera ndi nkhani yabwino ya chisangalalo chimene chidzakhala cha anthu onse lero mu mzinda wa Davide mpulumutsi wakubadwirani, Iye ndi Khristu Ambuye!" Ichi chidzakhala chidziwitso kwa inu, mudzapeza mwana atakutilidwa ndi zovala atagona modyetsera nkhosa.
>
> Mwadzidzidzi angelo akumwamba ena anatsika kulemekeza Mulungu ndi kunena: "Ulemelero ukhale ndi Mulungu wa mwamba ndi mtendere kwa munthu amene iye wamukondera."
>
> Pamene angelowo anabwerera kumwamba, abusawa ananena pakati pawo; tiyeni tipite ku Betelehemu tikaone zimene zachitika, zimene Mulungu watiuza ife.
>
> Choncho anafulumira ndi kukapeza Mariya ndi Yosefe ndi mwanayo amene anagona modyera nkhosa.
>
> Atamuona Mwanayu anafalitsa uthengawu wokhudzana ndi zimene anauzidwa za Mwanayu. Ndipo onse amene anamva anazizwa ndi zimene abusawo ananena. (Luka 2:8-18)

Abusa anali ndi nkhani yodabwitsa!

*Mpulumutsi wabadwa! Tamuona! Tamugwira! Mngelo watiuza kuti Iye ndi Khristu Ambuye. Gulu loyimba la angelo linadzaza mlengalenga. Usiku unali ngati masana! Mesiya wabwera, ali pano! ali pano!*

Anthu ena anakhulupirira uthenga wa abusawo koma ambiri sanakhulupirire. Koma kukhulupirira kapenanso kusakhulupirira, Mfumu imene kubadwa kwake kunagawa mbiri ya dziko pawiri,[14] inali yoyanjanitsa mtundu wa anthu.

> Masiku asanu ndi atatu atadutsa, mwana uja atadulidwa, anatchedwa Yesu, dzina lopatsidwa ndi mngelo kwa Iye asanalowe m'mimba mwa mayi wake. (Luka 2:21)





## Gawo la sewero 42

# Nkhani ya anzeru akum'mawa

Yesu atabadwira mu khola, Yosefe anapezera banja lake malo abwino ogona.

Tsiku lina anzeru akum'mawa anatulukira mu Yerusalemu. Anatsogoleredwa ndi nyenyezi yodabwitsa, anthuwa anachokera kutali ndipo amakayang'ana mfumu ya tsopanoyi.

Anthu anzeruwa anali ndi funso limodzi ndi cholinga chimodzi:


> "Kodi ali kuti amene wabadwa kukhala Mfumu ya Ayuda? Tawona nyenyezi yake ku m'mawa ndipo tabwera kudzamulambira Iye.
>
> Mfumu Herodi atamva izi anasokonezedwa ndi anthu onse mu Yerusalemu. Anayitana pamodzi aphunzitsi a malamulo nafunsa komwe khristuyo atabadwire.
>
> Mu Betelehemu ku Yudeya, anthuwo anayankha, pakuti izi ndi zomwe ulosi walemba.
>
> Kenako Herodi anayitana anzeru aja mwa chinsinsi, ndikunena pitani mukasake mwanayu. Mukamupeza mudzandiuze ine, kuti nane ndipite ndikukamulambira.
>
> Atamaliza kumva zomwe mfumuyo analankhula, iwo anapitiriza ulendo wawo ndipo nyenyezi ija anaiwona ku m'mawa inawatsogolera kufika pa malo pamene mwanayo anali. Atawona nyenyeziyo anasangalala.
>
> Akuyandikira nyumbayo, iwo anawona Mariya ndi mwanayo ndipo anawerama ndi kumulambira Iye. Atatero, anatsegula katundu wamtengo wapatali ndi kupereka mphatso zawo za golide ndi mafuta onunkhira.
>
> Atachenjezedwa mu maloto kuti asabwerere kwa Herodi, anzeruwa anabwerera kwawo kudzera njira ina.
>
> Iwo atapita, mngelo wa Mulungu anamuonekera Yosefe mu maloto, "dzuka" anati "tenga mwana wako ndi mayi ake ndipo muthawire ku Aigupto, mukakhale kumeneko mpaka ine ndidzakuuze pakuti Herodi adzafuna mwanayo kuti amuphe." (Mateyu 2:1-13)

Herodi anayesetsa kuti amuphe mwanayu, koma anthu a ku Yerusalemu sanamulabadire. Koma anzeru akum'mawa amene anadutsa m'chipululu chotentha kuti amupeze, anamulambira Iye, ndikumupatsa mphatso za ufumu: golide, lubani komanso mankwala odula oika thupi kuti lisawole.

Chifukwa chiyani mankhwala oika thupi kuti lisaole?

Kodi anzeruwa anadziwa kuti Yesu anabadwa kuti adzafe?





## Gawo la sewero 43

# Mwana wangwiro

Mngelo atapereka chenjezo, Yosefe anatenga Mariya ndi Yesu kupita ku Aigupto. Kumene anakhala mpaka imfa ya mfumu ya nkhanza Herodi.

> Herodi atamwalira mngelo wa Mulungu anamuonekera Yosefe ku maloto nanena "dzuka tenga mwanayu ndi mayi wake upite ku dziko la Israyeli chifukwa amene amafuna kutenga moyo wa mwanayu wamwalira." (Mateyu 2:19-20)

Izi zinakwaniritsa uneneri wakale wa Ambuye:

> kuchoka mu Aigupto ndiyitana mwana wanga. (Hoseya 11:1)

Choncho Yosefe ndi Mariya anatengera Yesu ku Nazareti, kumene anakula limodzi ndi abale ndi alongo ake.[15]

Mu njira zambiri Yesu mnyamata anali monga anyamata ena onse, anadya, kugona, kusewera, kuchita maphunziro ndi kuchita malonda. Koma mu njira zina anali osiyana ndi ana ena. Iye sanali odzikonda yekha, analemekeza makolo ake nthawi zonse, sananeneko bodza ndipo nthawi zonse anasangalatsa tate wake wa kumwamba.

> Anali woyera mtima, wopanda choyipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi ochimwa, wakukhala kupitirira miyamba. (Ahebri 7:26)

Yesu ndi mwana yekhayo wopanda cholakwika mu mbiri. Chosalakwika sikutanthauza kuti sanakhalepo ndi chilonda kapena kuti chiphuphu pa khungu, izi zikutanthauza kuti anali wa chibadwa cholungama. Anali woyera mu zonse ndi wabwino. Analinso wopambana mu mphamvu ndi mu nzeru. Koma asanalowe mu chiberekero cha Mariya anadzipatsa malire kuti akathe kukhala monga munthu pakati pa anthu.

> Yesu anakula mu nzeru ndi mu thupi, ndi mukukondera kwa Mulungu ndi anthu. (Luka 2:52)

Pamene Yesu anali ndi zaka khumi ndi ziwiri, anapita ulendo ochoka ku Nazareti kupita ku Yerusalemu ku msonkhano wa nsembe wa pa chaka otchedwa pasaka. Pamene anzake anali kuona zambiri za mzindawu, Yesu anakhala sabata yonse mu kachisi, kukhala pakati pa aphunzitsi kumvera iwo ndi kufunsa mafunso.

> Onse amene anamumva Iye anazizwa ndi kumvetsetsa komanso mayankho ake. (Luka 2:47)

Kachisi anali malo amene nkhosa zimawotchedwa, kuperekedwa nsembe mmalo mwa machimo awo. Yesu anali kumvetsetsa zomwe akulu sanathe kuzimvetsetsa.

Iye anabwera kudzapereka mwana wa nkhosa womaliza.





## Gawo la sewero 44

# Mwana wa nkhosa Wa Mulungu

Zaka makumi atatu zinali zitadutsa kuchokera nthawi yomwe Yesu anabadwa mu Betelehemu. Kaisala Augusto anali atamwalira; mwana wake womupeza wa mamuna Kaisala Tiberius anali atatenga ulamuliro wa ufumu wa chiRoma. Herode Antipas anali kulamulira mu Galileya. Pontio Pilato anatsogolera Yudeya. Ndipo mneneri watsopano amalalikira mu Palestina.

> Mumasiku amanewo Yohane m'batizi anabwera, kumalalikira mu chipululu cha Yudeya ndi kumati: "Lapani, poti ufumu wakumwamba wayandikira."
>
> Uyu ndi iye amene anayankhulidwa za Iye kudzera mwa mneneri Yesaya: "Mawu oyitanidwa kamodzi mu chipululu, 'Konzekerani njira ya Ambuye, pangani njira zowongoka za Iye."
>
> Ndipo Yohane yekhayo anali nacho chovala chake cha ubweya wa ngamira ndi lamba wa chikopa nchiuno mwake, ndichakudya chake chinali dzombe ndi uchi wa kuthengo. (Mateyu 3:1-4)

Pamene anthu ambiri amumasiku ake amavala nsalu yoterera yabwino ndi kudya zakudya zabwino, Yohane anakhala mosavuta. Anali munthu yemwe anali ndi cholinga.

Yohane anali wokonza njira ya Mfumu.

Zaka mazana mazana zoyambirira, aneneri awiri, Yesaya ndi Malaki, analemba za mneneri wa mtsogolo amene anakalengeza zakufika kwa mneneri Mesiya. Yohane anali mneneri ameneyu.

Pamene aneneri ambuyomu anali atanenera: *Panthawi imeneyi, mpulumutsi wolonjezedwa adzabwera padziko lapansi*, Yohane analalikira: *Nthawi imeneyi yafika. Mpulumutsi ali pano*!

Anthu ambiri anapita kuchipululu kuti akamumve Yohane. Amene amalapa zochimwa zawo ndikufuna mpulumutsi, anabatizidwa mu mtsinje wa Yolodani. Munjira imeneyi anasonyeza chikhulupiriro chawo mwa Mesiya, amene anakatsuka ngongole yawo yayikulu ya tchimo ndi kuwaveka iwo chilungamo chake.

Tsiku ndi tsiku, Sabata ndi Sabata, Yohane anayankhula ndi anthu za mpulumutsi wolonjezedwa wa kumwamba, "amene sindiyenera kunyamula nsapato zake. Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto." (Mateyu 3:11)

Kenaka tsiku lina, mpulumutsi anabwera—pamwamba pa phiri, kudzera mu chinamtindi cha anthu, ndikutsika pansi pomwe Yohane amapanga ubatizo.


Yohane anamuloza Yesu nati:

> "Onani, mwana wa nkhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko la pansi!" (Yohane 1:29)

Kodi ndi chifukwa chiyani Yohane anamutchula kuti Mwana wa Nkhosa wa Mulungu?

Ngati mukudziwa chifukwa chake, ndiye kuti mukudziwa cholinga cha Mfumu.





## Gawo la sewero 45

# Mwana wa mwamuna wangwiro

Yesu anamupempha Yohane kuti amubatize. Yohane anakana chifukwa Mesiya –Mfumu yomwe inachokera kumwamba inalibe tchimo kuti ilape.

> Koma Yesu anayankha nati kwa iye, balola tsopano: pakuti kuyenera ife kukwaniritsa chilungamo chonse motero." (Mateyu 3:15)

Ndiye Yohane anamubatiza Yesu. Pokhala obatizidwa, Yesu anawonetsa kuti anali wa banja la anthu lomwe anabwera kudzalipulumutsa.

> Ndipo Yesu, pamene anabatizidwa, pomwepo anatuluka m'madzi: ndipo onani, kumwamba kunamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye.  Ndipo onani mawu akuchokera ku mwamba akuti: 'Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa mwa iyeyu ndikondwera!" (Mateyu 3:16-17)

Pa tsiku loyamba lakulenga, tikuona mgwirizano waukulu wa Mulungu ukuwonetseredwa. Monga Mulungu Atate, Mzimu wake, ndi Mawu ake, akugwira ntchito pamodzi polenga dziko. Tsopano tikuonanso kuti ali pamodzi kugwira ntchito yoti apulumutse dziko.[17]

Tikuona *Mzimu wa Mulungu* (omwe pachiyambi ali pamwamba pamadzi) akutsikira pa Yesu. Tikuonanso *Mwana wa Mulungu* (Mawu omwe analenga dziko) akuyenda panyanja. Tikumvanso *Atate* akuyankhula kuchokera kumwamba.

Kwa zaka makumi atatu Yesu anakhala m'moyo wosadziulula chimene anali kwa anthu, koma Atate wa kumwamba amadziwa malingaliro ake, Mawu ake komanso zochita zake.

Kodi chikonzero  cha Mulungu pa Mwana wake chinali chotani?

> "Mwa Iye ndikondwera!"

Mu mbiri yonse ya munthu, Yesu ndi yekhayo yemwe anapanga zonse zomwe Mulungu amafuna. Chilichonse! Nthawi zonse! Moyenerera!

Yesu anapanga zomwe Adamu analephera kupanga: kuonetsera chithunzithunzi cha Mulungu.

Koma Yesu anapanga zoposa kuonetsera chinthunzicho. Iye anali Mulungu amene.


> Kale anayankhula ndi makolo mwa Aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana, koma pakutha pake pamasiku ano anayankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuyika wolowa mnyumba wa zonse, mwa iyenso analenga mayiko a m'mwamba omwe, ameneyu pokhala ali chinyezimiro cha ulemelero wake, ndi chizindikiro chenicheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mawu a mphamvu yake.... (Ahebri 1:1-3)

Palibe chodabwitsa kumva Yesu akunena:

> "Ine ndi Atate ndife amodzi." (Yohane 10:30)

Yesu ndi Mwana wangwiro.





## Gawo la sewero 46
# Munthu wachiwiri

Satana sanali osangalala kuti munthu wangwiroyu amakhala mu ufumu wake! Koma Satana anali ndi njira yogwirira ntchito. Ngati m'mene anamuyesera munthu oyambirira kuchita tchimo, ndiye tsopano anayesetsa kumuchititsa munthuyu uchimo.

Satana amafuna kumulamulira Yesu ngakhale kuti anamuika Adamu ku ulamuliro wake. Ngati Mwana wa Mulungu sangagonjetse tchimo, ndiye kuti sakanakhoza kupulumutsa anthu ake ku machimo.

> Kenaka Yesu anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera ku chipululu kuti akayesedwe ndi Satana. Atamaliza kusala kudya usana ndi usiku kwa masiku makumi anayi, anali ndi njala. Ndipo woyesayo anafika nanena kwa Iye, ngati muli Mwana wa Mulungu, tauzani miyala iyi isanduke mikate." (Mateyu 4:1-3)

Yesu anali ndi njala, koma sanamvere Satana. Sakanapanga zosiyana ndi chifuniro cha Atate wake. Sakanagwiritsa ntchito mphamvu zake zosatha kusangalatsa zokhumba za umunthu wake, kuti alimbane ndi Satana. Yesu ananena zomwe zinanendwa kale zochokera ku mabuku a Mose:

> "Kwalembedwa, munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mawu onse akutuluka mkamwa mwa Mulungu" (Mateyu 4:4; Deuteronomo 8:3)

Mu kupusa kwa kudzikuza kwake, Satana anayesanso kumuyesa Woyerayo.

> Pomweponso mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitali, namuonetsa mayiko onse a dziko lapansi, ndi ulemelero wawo, nati kwa Iye, zonse ndikupatsani Inu ngati mudzagwade pansi ndikundigwadira ine." (Mateyu 4:8-9)

Pamene Adamu anachimwa, munthu anataya mphamvu za ulamuliro wa dziko lapansi. Satana anali ataba ulamuliro wa dziko, kudzipanga yekha kukhala mfumu yake.

Tsopano mfumu ya ulemerero inali padziko lapansi kudzatenga ulamuliro, koma sadzapanga izi pomupembedza amene Iye anabwera kudzamuononga.

> Pomwepo Yesu ananena kwa iye, "choka Satana! pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekhayekha udzamlambira." (Mateyu 4:10)

Mapeto ake, Satana anamusiya Yesu. Satana anali asanamuyese aliyense ngati Iye, munthu amene analibe khumbo kapena kuthekera kochita tchimo. Yesu anali osiyana ndi Adamu ndi m'badwo wake.

> Munthu oyambayo ali wapansi, wamnthaka. Munthu wachiwiri ali wakumwamba. (1 Akorinto 15:47)

Adamu anali munthu wabwino oyambirira. Yesu anali munthu wabwino wachiwiri.

Pamene Satana anamuyesa Adamu kuti achimwe, Adamu analephera ndipo Satana anapambana. Pamene Satana anayesa kumupangitsa Yesu kuti achimwe, Satana analephera ndipo Yesu anapambana.

Munthu oyambirira anatitsogolera ife ku ufumu wa Satana wa tchimo ndi imfa. Munthu wachiwiri anabwera kudzatitsogolera ife kuti tichokemo.





# Gawo la sewero 47
## Mesiya-Mfumu

Satana atamaliza kumuyesa Yesu kuti achimwe, Yesu anabwerera ku Nazareti: kumene anakulira ndi kugwira ntchito ngati opala matabwa.

> Pa tsiku la sabata anapita ku sunagoge monga mwa mwambo wake. (Luka 4:16)

Sunagoge inali nyumba yolambiramo yomwe mawu a Mulungu amawerengedwa ndi kufotokozedwa tsiku la sabata lililonse. Patsiku la sabata lopatulikali Yesu anali ndi zoti alengeze.

> Anadzuka kuti awerenge.
>
> Zolembedwa za mneneri Yesaya zinaperekedwa kwa iye. Potambasula, anapeza malo omwe zinalembedwa:
>
> "Mzimu wa Ambuye ali pa Ine chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga wabwino, ananditumaIne kulalikira am'nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyenso …" (Luka 4:17-18)

Zomwe Yesu akuwerenga mu mawu a Mulungu ndi mbiri ya uneneri wa Mesiya-Mfumu yomwe inakawonetsa dziko lapansi m'mene Mulungu alili ndi kupulumutsa ochimwa kuchokera ku ufumu wa Satana, tchimo, imfa, ndi gahena.

> Kenaka Yesu anakulunga zolembedwa, anapereka kwa othandizira ndi kukhala pansi.
>
> Ndipo maso a anthu onse m'sunagogemo anamyang'anitsitsa Iye. Ndipo ananena kwa iwo; lero lembo ili lakwaniritsidwa m'makutu anu!" (Luka 4:20-21)

Kodi okhala naye pafupi anapangapo chiyani atatchula kuti Iye ndi Mesiya wochokera kumwamba kudzakwaniritsa zomwe aneneri analemba mu mawu a Mulungu?

> Anthu onse mu sunagoge anali okwiya atamva izi.
>
> Anadzuka, anamutulutsa mu mzindawu, ndi kumutengera pa mwamba pa phiri pomwe mzindawu unamangidwa, ndi cholinga chomuponya pansi pa phiri.
>
> Koma Iye anapitirira pakati pawo, nachokapo (Luka 4:28-30)

Yesu anali ndi ulamuliro. Angakhale kuti kuchimwa kwa Adamu kunakhudza ndi kudzetsa imfa ku mibadwo yotsatira koma Mesiya-Mfumu odzodzedwa[18] ndi Mulungu anali ndi mphamvu yothana zimenezi.

Palibe yemwe anakamukhudza pokhapokha Iye avomereze.

Koma Iye akanatha kuwakhudza.





## Gawo la sewero 48
# Ulamuliro pa Ziwanda ndi Matenda

Mu ma buku a aneneri, dzina lina la Mesiya ndi *Mkono wa Yehova.* (Yesaya 53:1) Zozizwitsa za Yesu zinaonetsa kuti Iye ndi Mkono wa Mulungu padziko. Ndikukhudza kwa dzanja lake kapena Mawu ochokera pakamwa pake, odwala ndi akufa nthawi yomweyo anapangidwa kukhala bwino.

> Anthu ambiri anadza kwa Iye, ali olumala, akhungu, osayankhula, ndi ena ambiri, nawakhazika pansi pamapazi Ake; ndipo Iye anawachiritsa. (Mateyu 15:30)

Mawu a aneneri anakwaniritsidwa.

> Akhungu alandira kuona kwawo, ndi olumala miyendo anayenda, akhate anachiritsidwa, ndi osamva anamva , ndi akufa anaukitsidwa, ndipo a umphawi analalikidwa Uthenga wabwino. (Mateyu 11:5 [Yesaya 35:4-6; 61:1])

Panalibe nthenda imene Yesu sanakachiritsa.

> Munthu wodwala khate anabwera kwa Iye, anamudandaulira ndi kumugwadira pansi Iye ndi kunena kuti: "ngati mukufuna, mukhoza kundiyeretsa."
>
> Kenaka Yesu, anasunthika ndi chifundo, anatambasula dzanja lake ndi kumukhudza iye, ndipo anati kwa iye, "Ndikufuna; khala oyeretsedwa."
>
> Ndipo pomwepo khate linachoka ndipo anachiritsidwa. (Marko 1:40-42)
>
> Pamene dzuwa limalowa, anthu anabweretsa kwa Yesu onse omwe anali ndi matenda, ndi kuika manja Ake pa wina aliyense, anawachiritsa. Ndipo, mizimu yoyipa inatuluka mwa anthu ambiri, ikufuula kuti "Ndinu mwana wa Mulungu."
>
> Ndipo Iye anadzudzula Mizimu yoyipa, osailola kuyankhula, chifukwa zinam'dziwa kuti Iye ndiye Khristu. (Luka 4:40-41)


Yesu samafuna kuti mizimu yoyipa iyikire umboni za Iye. Angelo oyipawa anali atayikira umboni za ulamuliro ndi mphamvu zake pamene anayika kumwamba ndi dziko lapansi m'malo mwake. Ananjenjemera pamene anakumbukira tsiku lomwe Iye anawaponya kuchoka kumwamba. Ndipo tsopano akukhala pa dziko lapansi ngati munthu! Ulamuliro wa Mfumu yawo unayamba kutha. Mfumu ya ulemerero Inali Italowerera ufumu wawo.

Kulikonse komwe Yesu ankapita, mphamvu za Satana zimachepetsedwa komanso themberero la tchimo limadulidwa.

Yesu analalikira Uthenga ndi kuchita zozizwa:

> "Nanena, nthawi yakwana, ndipo ufumu wa Mulungu wayandikira, tembenukani mtima khulupiriani uthenga wabwino!" (Marko 1:15)





## Gawo la sewero 49
# Ulamuliro pa Mphepo ndi Mafunde

Yesu anasankha amuna khumi ndi awiri kuti ayende nawo ndi kuphunzira kuchokera kwa Iye.

Komanso omutsatira Iye ambiri anali aakazi. Anathandiza Yesu ndi ophunzira ake powapatsa chakudya ndi ndalama.

Kwa omwe amakhulupirira mwa Iye, kuitana kwa Yesu kunali kosavuta:

> "Unditsate Ine." (Luka 5:27)

Koma kuitana kwakeko kunali ndi zovuta zake:

> "Iye wakukonda Atate wake, kapena amake kuposa Ine, sayenera Ine, ndipo Iye wakukonda mwana wake wa mwamuna, kapena wamkazi, koposa Ine sayenera Ine." (Mateyu 10:37)

Popeza ambiri mwa ophunzira ake anali asodzi, Yesu nthawi zambiri amakonda kukhala ku Nyanja yayikulu ya Galileya. Anthu amabwera kwa Iye kuchokera kutali.

> Nthawi zina amaphunzitsanso m'mbali mwa nyanja. Ndipo anthu ochuluka anamutsata Iye pamene Iye anali mungalawa. (Marko 4:1)

Litatha tsiku lophunzitsa, Yesu anati kwa ophuzira ake, "Tiyeni tipite mbali ina." Anali kale mu bwato ndiye ananyamuka, kusiya gulu la anthu M'mbuyo.

> Koma nthawi yomweyo mphepo ya mkuntho inafika. Chifukwa cha mafunde, bwato linayamba kudzadza madzi. Yesu anali akugona ataika mutu wake pa mtsamiro.
>
> Ophunzira anamudzutsa, akukuwa, "Aphunzitsi, kodi simukusamala kuti tikumira?"
>
> Pamene Yesu anadzuka, anadzudzula mphepo ndi kunena kwa mafunde,
>
> "Chete! khala bata!"
>
> Mwadzidzi mphepo inasiya, ndipo kunali bata.
>
> Kenaka anawafunsa, "Kodi muli ndi mantha chifukwa chiyani? Kodi mulibe chikhulupiriro?"
>
> Ndipo iwo anachita mantha akulu, nanena wina ndi mnzake, Kodi ndi ndani ameneyu, kuti ingakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye!" (Marko 4:37-41)

*Kodi munthu ameneyu ndi ndani?* Zaka zikwi zoyambirira, mneneri Davide anali atayankha kale funsoli:

> Adzandira napambanitsa miyendo ngati munthu oledzera, nathedwa nzeru konse. Pamenepo anafuwulira pa Yehova m'kusauka kwawo, ndipo awatulutsa mkuphinjika kwawo. Asanduliza namondwe akhale bata, kotero kuti mafunde ake atonthole. (Masalmo 107:27-29)

Kodi ndani amene angangoyankhula kwa mphepo ndi mafunde kuti zikhale bata?

Ndi Mawu omwewo amene anawalenga iwo.





## Gawo la sewero 50

# Ulamuliro pa tchimo

Tsiku lina, amuna anayi atanyamula munthu olumala pa machira anapita kunyumba komwe kunali Yesu.

Amunawa anayesa kupeza njira kuti akumane ndi Yesu koma m’chipindacho munali modzaza kwambiri. Ndiye anakwera padenga, kuchotsa denga, ndi kutsitsa mkeka m’chipindacho, kutsogolo kwenikweni kwa Yesu.

> Ndipo Yesu pakuona chikhulupiriro chawo ananena ndi odwala manjenje, mwana, machimo ako akhululukidwa.” (Marko 2:5)

Yesu anadziwa kuti munthu ameneyu chofuna chake chachikulu sichinali kufuna kuyenda ayi koma kukhululukidwa machimo ake.

> Koma ena mwa aphunzitsi achipembedzo amene anakhala pafupi anaganiza mwa iwo okha, “Kodi Iye akuti chiyani? Uwu ndi mwano! Ndi Mulungu yekha amene akhoza kukhululukira machimo!”
>
> Nthawi yomweyo Yesu anadziwa zomwe amaganiza, ndiye anawafunsa, “Kodi mukufunsiranji zimenezi mu mitima yanu? Kodi zophweka ndi ziti, kunena kwa munthu olumala kuti: ‘Machimo ako akhululukiridwa,’ kapena ‘Dzuka, tenga mkeka wako, ndi kuyenda’? Ndiye ndikuwonetsani kuti Mwana wa Munthu ali ndi ulamuliro pa dziko lapansi kuti akhululuke machimo.”
>
> Kenaka Yesu anamutembenukira munthu olumala, ndi kunena: “Dzuka, tenga mkeka wako, ndi kupita kunyumba!”
>
> Ndipo munthu anadumpha, kugwira mkeka wake mwa mphamvu,
>
> ndi kuyenda pakati pa woyang’anira osakhulupirira.
>
> Kotero kuti anadabwa onse, nalemekeza Mulungu, nanena kuti, zotere sitinaziwone ndi kale lonse!” (Marko 2:6-12)

Aphunzitsi a malamulo anali ophimbidwa m’maso ndi chipembedzo ndi kudzikuza kwawo. Maganizo awo anakhala ngati awa: *Yesu, ndiwe wamwano! Ukunyoza Mulungu chifukwa ukunama kuti umakhululukira machimo, koma ndi Mulungu amene angapange zimenezi!*


Anali olondola poganiza kuti ndi Mulungu yekha yemwe angakhululuke machimo,

koma, anali olephera pa kuganiza kwawo za kuti Yesu ndi ndani.

Kodi mukuganiza kuti Yesu ndi ndani? Kodi mukukumbukira tanthauzo la dzina lake? Limatanthauza kuti *AMBUYE Amapulumutsa*.

Mu mzinda wina waku Palestina kumene Yesu anaphunzitsa, anthu ananena motere:

> “Tsopanao sitikhulupirira chifukwa cha kuyankhula kwako; Pakuti tamva tokha ndipo tidziwa kuti Mpulumutsi wa dziko lapansi ndi Iyeyu ndithu.” (Yohane 4:42)





## Gawo la sewero 51
## Ulamuliro pa Imfa

Yesu anali ndi ulamuliro pa zolengedwa zonse. Koma sanayendeyende kumanena kuti: "Pembedzani Ine! Ndine Mulungu! Ndine Mulungu!" Iye amangochita zinthu zomwe Mulungu yekha akadatha kuchita ndikusiya anthu, kuganizira okha kuti Iyeyo ndi ndani.

Kuchokera pankhani ziwiri zakutsogoloku, Kodi mukuganiza kuti Yesu ndi ndani?

> Yesu anapita mu mzinda otchedwa Naini, ophunzira ake ndi khamu la anthu linapita naye limodzi. Pamene anafika pa chipata cha mzinda, munthu wakufa anali atanyamulidwa—mwana wa mamuna yekhayo wa mayi ake, ndipo anali mkazi wa masiye. Ndipo gulu lalikuru lochokera mu mzinda linali naye pamodzi.
>
> Pamene Ambuye anamuwona, mtima wawo unakhudzika ndipo anati: "Usalire."
>
> Kenaka anapita kukakhudza bokosi la maliro, ndipo amene analinyamula anakhala nalo chiyimire. Anati: "Mnyamata, ndi kunena kwa iwe, dzuka!"
>
> Munthu wakufa anauka nayamba kulankhula ndipo Yesu amampereka kwa amai ake. Onse anazizwa nalemekeza Mulungu. (Luka 7:11-16)

Tsiku lina Yesu anakumana ndi Maria ndi Marita ali a chisoni. Panali patapita masiku anayi mchimwene wao atamwalira.

> "Ambuye," Marita ananena kwa Yesu, "mukanakhalapo, m'chimwene wanga sakanafa …
>
> Yesu anati kwa iye, "Ndine kuuka ndi moyo. Amene akhulupirira mwa Ine adzakhala ndi moyo, ngakhale amwalira; ndipo amene akhala ndi moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa. Kodi mukukhulupirira izi?"
>
> "Inde, Ambuye," anamuwuza, "Ndikukhulupirira kuti ndinu Khristu, mwana wa Mulungu, amene amayenera kudzabwera padziko lapansi."
>
> Yesu … anapita ku manda. Linali mphanga lotsekedwa ndi mwala pakhomo lolowera. "Chotsani mwala," ananena.
>
> "Koma, Ambuye," ananena Marita, uyu anali mlongo wake wa Lazaro "panthawi imeneyi panali fungo loyipa, pakuti anali atakhalamo masiku anayi."
>
> Yesu anati "Kodi sindinakuuza iwe kuti ngati ukhulupirira udzaona ulemelero wa Mulungu?" zitatha izi anachotsa mwala. Yesu anafuula ndi mawu okweza "Lazaro Tuluka!" Wakufayo anatuluka ali womangidwa mmanja ndi mmiyendo. Yesu anati kwa iwo "Muvuleni zovala zakumanda ndi kumulora amuke." (Yohane 11:21,25-27,38-41,43-44)

Ambuye Yesu ndi yekhayo mu mbiri amene angathe kunena:

> "NDINE kuuka ndi moyo."

Ntchito zake zinatsimikizira kuti mawu ake anali oona.





## Gawo la sewero 52

# Wopereka

Khamu lalikulu la anthu linamuzungulira Yesu, nthawi zina kwa masiku. Nthawi zambiri amamupeza kumalo achipululu, kumene amatha kupita kukakhala pamodzi ndi akuphunzira ake. Nthawi zina gulu la anthu limakhala ndi njala.

Izi ndi zomwe zinachitika masana ena pamene zikwi zopitirira zisanu za anthu zinali zitasonkhana kuvuma kwa mbali ya phiri la nyanja ya Galileya. Ndiye Yesu anamufunsa Filipo, m'modzi mwa ophunzira ake,

> "Kodi tingagule kuti mkate odyetsa anthu onsewa?" Amamuyesa Filipo, poti Iye amadziwa kale chomwe akanachita.
>
> Filipo anayankha: "sizikhala zophweka kuti tiwadyetse!"
>
> Kenaka Andireya, Simoni m'chimwene wake wa Petro, anayankhapo.
>
> "Pali mnyamata wang'ono pano ali ndi mikate isanu yeniyeni ndi nsomba ziwiri. Koma kodi zili ndi ubwino wanji ndi gulu lalikululi?"
>
> "Uzani aliyense kuti akhale pansi," Yesu analamula. Ndiye onse—amuna okha amakwana zikwi zisanu—anakhala pansi malo otsetsereka a udzu.
>
> Kenaka Yesu anatenga mikate, ndikuthokoza kwa Mulungu, ndi kugawa kwa anthu. Kenaka anapanganso chimodzimodzi ndi nsombazo. Ndipo onse anadya mpaka anakhuta.
>
> "Tsopano sonkhanitsani zotsala," Yesu anawauza ophunzira ake,"kuti chilichonse chisaonongedwe."
>
> Panali mikate inayi yokha imene anthu amayenera kudya koma madengu khumi ndi iwiri inadzaza ndi mikate kufikira kuti anthu sakanatha kuimaliza kudya! (Yohane 6:5-13)


Tsiku lotsatira gulu la anthu linabwera kudzamuyang'ana Yesu. Amafuna kumpanga kukhala mfumu yawo, kuti awapulumutse ku khanza za ufumu wa Aroma ndi kuwapatsa chakudya chambiri. Yesu anawauza:

> "Simukuyenera kusamala za zinthu zakutha ngati chakudya. Gwiritsani ntchito mphamvu zanu kufunafuna mkate wa moyo omwe Ine, Mwana wa Mulungu,[19] ndi ngakupatseni. Poti Mulungu Atate wanditumiza Ine ndi cholinga chomwecho.
>
> "Ine Ndine Mkate Wamoyo. Yense wakudza kwa Ine sadzamva njala konse. Iwo wokhulupirira Ine sadzamva ludzu konse." (Yohane 6:27,35)

Chakudya chikhoza kusunga thupi lanu ndi moyo kwa ka nthawi, koma Ambuye Yesu yekhayo akhoza kukupatsani moyo wa choonadi, kwa nthawi yayitali ndi yosatha.

Yesu yekha akhoza kunena:

> "NDINE mkate wa moyo."





## Gawo la sewero 53

# Mphunzitsi

Yesu sanali ngati aphunzitsi azipembedzo omwe amanena zinthu ngati: "Pangani izi! Osapanga izi! Tsatirani malamulo awa! Iyi ndiye njira!" Yesu yekha amati:

> "Ine ndine njira, ndi choonadi ndi moyo." (Yohane 14:6)

Yesu analinso osiyana ndi aneneri omwe amapereka nsembe chifukwa cha machimo awo ndi kulemba za Mesiya amene akubwera. Yesu anati:

> "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: Sindinadza kupasula, koma kumwaniritsa" (Mateyu 5:17)

Nthawi zambiri amawaphunzitsa ophunzira ake m'mene nzika za ufumu wakumwamba ziyenera kukhalira kuti awunikire khalidwe ndi ulemerero wa Mfumu yawo.

> "Mwamva kuti zinanenedwa, 'Kondani mnasi wanu ndipo mudeni mdani wanu.' Koma ndikukuwuzani: Kondani adani anu ndi kuwapempherera amene amakusowetsani mtendere.
>
> "Pamene mukupemphera, musakhale ngati abodza, poti amakonda kupemphera … kuti adziwonedwa ndi anthu. Koma mukapemphera, pitani muchipinda chanu, tsekani chitseko chanu ndi kupemphera kwa Atate, amene sawoneka. Umu ndi m'mene muyenera kupempherera: 'Atate wathu wakumwamba, dzina lanu liyeretsedwe, Ufumu wanu udze, monga kumwamba chomwecho pansi pano. Mutipatse chakudya chathu chalero …'
>
> "Usadandaula," kunena: 'Kodi tidya chiyani?' kapena 'Kodi timwa chiyani?' kapena 'Kodi tivala chiyani?' Poti akunja amadera khawa za zinthu zonsezi, ndipo Atate wanu wakumwamba akudziwa kuti mukuzisowa. Koma funani kaye ufumu ndi chilungamo chake, ndipo zinthu zonse zidzaperekedwa kwa inunso.
>
> "Chenjerani ndi aneneri onama. Amabwera kwa inu muchovala cha nkhosa, koma mu mtima ndi nkhandwe zoopsa.
>
> "Aliyense amene amamva Mawu awa a Ine ndi kuwachita ali ngati munthu wanzeru amene anamanga nyumba yake pa mwala. Mvula inabwera, mitsinje inadzadza, ndipo mphepo zinawomba ndi kumenya nyumba; komabe sinagwe, chifukwa inali ndi maziko ake pa mwala.
>
> "Ndipo yense akamva mawu anga amenewa ndikusawachita, adzafanizidwa ndi munthu opusa, yemwe anamanga nyumba yake pa mchenga; ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinawomba mphepo, zinagunda panyumbayo; ndipo inagwa."
> (Mateyu 5:43-44; 6:5-6,9-11,31-33; 7:15,24-27)

Palibe anayankhulapo ngati Mphunzitsi ochokera kumwamba.





## Gawo la sewero 54

# Wolemekezeka

Aphunzitsi ndi a nsembe a chiYuda sanali okondwera kuona gulu la anthu likumumvera Yesu amafuna anthu adziwamvera iwo, osati Iye!

Tsiku lina wamkulu wa abusa anawatuma alonda amukachisi awo kuti amumange Yesu, koma sakanatha kumumanga Iye. Iwo atabwerera, abusa anawafunsa, “Kodi simunamubweretse chifukwa chiyani?” Alonda anayankha:

> “Nthawi yonse palibe munthu anayankhula ngati Iye.” (Yohane 7:46)

Ngakhale aneneri sanayankhule ngati Iye. Aneneri anali ngati nyali zongoonetsera kuwala mu dziko la m’dima, koma Mesiya anali ‘’Dzuwa la chilungamo.’’ (Malachi 4:2) Ndani angafunenso nyali dzuwa litawala?

Yesu anati:

> “Ine ndine kuwunika kwa dziko lapansi; Iye onditsata Ine sadzayenda mumdima, koma adzakhala nako kuwunika kwa moyo.” (Yohane 8:12)

Yesu ndi Liwu limene pachiyambi linati: “Lolani kuti kuwale.” Ndi chiyambi chenicheni cha kupezeka kwa kuwala kwa m’thupi ndi uzimu.

Pamene nthawi inakwana kuti Mesiya akwaniritse cholinga chake, anapita ndi ophunzira ake atatu, Petro, Yakobo, ndi Yohane ku phiri.


> Ndipo Iye anasandulika pamaso pawo; ndipo nkhope yake inawala monga dzuwa, ndizovala zake zinakhala zoyera mbu monga kuwala.
>
> Ndipo onani, Mose ndi Eliya anaonekera kwa iwo ali kulankhula ndi Iye… onani thambo wowala unawaphimba iwo; ndipo onani, mawu ali kunena mumtambo,
>
> “uyu ndi mwana wanga okondedwa mwa Iyeyu ndikondwera, mverani Iye!”
>
> Ndipo pamene ophunzira anamva, anagwa nkhope zawo pansi, nawopa kwakukulu. Ndipo Yesu anadza nati: “dzukani, musaopa.”
>
> Ndipo iwo, pokweza maso awo sanaona munthu, koma Yesu yekha. (Mateyu 17:1-3,5-8)

Ophunzira sanayiwale zimene anaona pa tsikulo. Patapita nthawi, Petro analemba, tinaona ndi maso ukulu wake (2 Petro 1:16) Ndipo Yohane analemba nati: “ndipo tinawona ulemelero wake, ulemelero wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi.” (Yohane 1:14)

Koma tsopano, ulemerero wa Mwana unakapitirira kubisika mu thupi la mnofu wake.

Inali nthawi ya Mfumu kukwaniritsa cholinga chake.





## Gawo la sewero 55
# Cholinga chake

Kwa zaka zitatu, Ambuye Yesu anali kuyenda mu Palestina "anachita zabwino, nachiritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi." (Machitidwe a atumwi 10:38) Anthu ambiri amamukonda, koma atsogoleri azipembedzo mu Yerusalemu amakonzekera kuti amuphe—ndipo Yesu anadziwa.

> Ndipo panali, pamene anayamba kukwanira masiku akuti alandiridwe Iye kumwamba, Yesu anali wa chisoni kuloza nkhope yake kunka ku Yerusalemu. (Luka 9:51)

Kodi munakadziwa kuti gulu la amuna oipa okhala mu mzinda amakonzekera zogwira, kuzunza ndi kupha inu kodi munakapitako?

Izi ndi zomwe Yesu anapanga.

> Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kuwalangiza ophunzira ake, kuti kuyenera Iye amuke ku Yerusalemu, kukazunzidwa kwambiri ndi akulu, ndi ansembe akulu, ndi alembi; ndi kukaphedwa, ndi tsiku la chitatu kuuka kwakufa. (Mateyu 16:21)

Uwu sunali mtundu wa mfumu yomwe ophunzira amayang'ana.
*Kodi Mesiya wake opachikidwa? Zoonadi Mulungu anakalola osankhidwa wake kuzunzika muzowawa ndi kuchititsidwa manyazi!* Ndiye Petro anati kwa Yesu:

> "Osatheka, Ambuye! Izi sizingachitike kwa Inu!"
>
> Koma Iye anatembenuka, nati kwa Petro, pita kumbuyo kwanga, Satana iwe!  Ndiwe chokhumudwitsa Ine, chifukwa sumasamalira za Mulungu, koma za anthu." (Mateyu 16:22-23)

Ophunzira amafuna Mesiya-Mfumu amene akanapasula Ufumu wa chiRoma ndi kupanga boma latsopano mu Yerusalemu. Ngakhale pamene amayenda, ophunzira amakangana za amene atenge ma udindo apamwamba mu Ufumu wa Mulungu. Ndiye Yesu anawauza ophunzira ake,

> "Koma amene aliyense afuna kukhala wamkulu mwa inu, akhale mtumiki wanu....Monga mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndikupereka moyo wake kwa anthu ambiri." (Mateyu 20:26,28)

Pakubwera kwake koyamba padziko lapansi, Mesiya sanabwere kudzagonjetsa ma ufumu andale ndi kulamulira mipando ya chifumu ya dziko lapansi; Anabwera kudzagonjetsa Satana ndi kulamulira mu mitima ya anthu. Ndi chifukwa chake Yesu anaphunzitsa,

> "Ufumu wa Mulungu uli mkati mwa Inu." (Luka 17:21)

Koma Mfumu ya kumwamba isanalamulire mu mitima yathu (ndipo kenaka kwa dziko lonse lapansi), ngongole ya tchimo la dziko lapansi imayenera kuperekedwa ndipo imfa imayenera kugonjetsedwa.

*Chimenecho* ndiye chinali cholinga chake.





## Gawo la sewero 56
# Mfumu Ilowa Mu Yerusalemu

Chilichonse chimayenda molingana ndi chikonzero chake. Pamene Ambuye anayandikira Yerusalemu,

Anatuma ophunzira ake awiri.

> "Pitani m'mudzi uwo," anawauza. "Pamene mukulowamo, muona bulu wang'ono omangidwa yemwe sanayambe wakweredwapo. Mumumasule ndipo mubwere naye kuno. Ngati wina aliyense afunsa, 'Kodi chifukwa chiyani mukumumasula mwana wa bulu?' mungonena kuti: "Ambuye akumufuna."
>
> Ndiye anapita ndi kukamupeza mwana wa bulu uja, ngati m'mene Yesu ananenera. Ndipo moonadi, pamene amamumasula, eni ake anawafunsa, "Kodi mukumumasuliranji mwana wa bulu?"
>
> Ndipo ophunzira anayankha, "Ambuye akumufuna." Ndiye anapititsa mwana wa bulu kwa Yesu ndi kuponya zovala zawo pamwamba pake kuti Iye akwere.
>
> Pamene anakwera, gulu la anthu linayala zovala zawo patsogolo pa Iye. Atafika pa malo pamene nsewu unatsikira ku Phiri la Azitona, omutsatira onse anayamba kufuula ndi kuyimba pamene amayenda nawo, kumutamanda Mulungu chifukwa cha zozizwitsa zabwino zonse zomwe anaona. "Madalitso kwa Mfumu imene akubwera mu dzina la Ambuye! Mtendere kwa onse, ndi ulemerero kumwamba!"
>
> Koma ena mwa Afarisi makumi awiri pakati pa gulu la anthu anati: "Aphunzitsi, dzudzulani otsatira anu ponena zinthu ngati zimenezo!"
>
> Ndipo anayankha nati: "ndinena ndi inu, ngati awa akhale chete, miyala idzafuwula!" (Luka 19:30-40)

Mfumu ya mtundu wina!

Mesiya-Mfumu sanabwere ndi kuimba kwa malipenga ndi asirikari amphamvu. Sanalowe ndi akhondo a akavalo ovala bwino.

Anakwera bulu wang'ono, yemwe anali asanagwiritsidwepo ntchito, ndipo buluyu ananyamula munthu wofunikira kwambiri, amene akanatha kukwaniritsa zomwe mneneri Zekariya anali atalemba zaka zikwi zisanu zoyambirira:

> Fuwula mwana wamkazi wa Yerusalemu; taona, Mfumu yako ikudza kwa iwe, ndiye wolungama, ndi mwini chipulumutso; wofatsa ndi wokwera pa bulu, ndi mwana wa mphongo wa bulu. (Zekariya 9:9)

Kodi ndi chifukwa chiyani Mesiya-Mfumu sanabwere ndi akavalo akhondo amphamvu? Chifukwa sanabwere kudzapulumutsa anthu ku nkhanza za Aroma.

Anali atabwera kudzapulumutsa anthu ku nkhanza za machimo awo.





# Gawo la sewero 57

## Mfumu ikufunsidwa mafunso

Kwa masiku ochepa otsogozana, Yesu anaphunzitsa anthu mu kachisi ali mnyamata, ndipo anadabwitsa wophunzira ndi mafunso ozama komanso mayankho a nzeru. Atsogoleri amukachisi anakhala ndi malingaliro aupandu nanena kuti:

> "Ife sitifuna munthuyu akhale mfumu yathu!" (Luka 19:14)

Ndipo anamuukira Yesu namufunsa mafunso ovuta ndi cholinga choti anthu ambiri amuukire Iye.

> Pofuna kupezerapo mwayi, atsogoleriwo anatumiza akazitape odzionetsera ngati anthu achilungamo. Anayesetsa kumukopa Yesu kunena zinthu zimene akanadzitengera kwa wamkulu wa Aroma ndi cholinga choti Yesu amangidwe.

> Mphunzitsi, ife tidziwa kuti munena ndi kuphunzitsa kolunjika, ndikusasamalira nkhope ya munthu, koma muphunzitsa njira ya Mulungu moonadi. Kodi kuloledwa kupereka msonkho kwa Kaisara kapena iai?" (Luka 20:20-22)

Kodi Yesu akanayankha bwanji? Akananena kuti: "Inde, perekani msokho kwa mfumu," Ayuda akanamuona ngati munthu wosakhudzika ndi mavuto awo. Komanso akanayankha kuti: "Ayi, osapereka msonkho," Mkulu wa Aroma anakamva zimenezi, akanamuweruza kuti akuukira.

> Ataona kuchenjera kwawo Iye anati: "Ndiwonetseni ndalama ya Aroma. Kodi pali nkhope ndi dzina la ndani?"

> "Kaisara," anayankha.

> Iye anati kwa iwo, "Chifukwa chake perekani kwa kaisara zake za kaisara, ndi kwa Mulungu zake za Mulungu."

> Ndipo analephera kumukola mu zonena zake pamaso pa anthu, mmalo mwake onse anadabwitsika ndi mayankhidwe ake, choncho onse anakhala kakasi. (Luka 20:23-26)

Kawirikawiri, magulu osiyanasiyana a aphunzitsi azipembedzo anayesa kuti amukole Yesu, koma nthawi iliyonse amawayankha mwanzeru.

> Zitatha izi, Ayuda sanafunenso kumufunsa mafunso. (Mateyu 22:46)

Chifukwa cha manyazi amunawa anachoka mozemba kukagwirizana ndi ansembe aakulu kuti amumange ndi kumupachika Yesu. Kusazindikira! Ansembewa, amene amapereka nsembe pa guwa samazindikira kuti nsembe zimene amapereka zinali chithunzithunzi cha Iye yemwe iwo amafuna kumupha.

Chinsinsi cha Mulungu chinali pafupi kukwaniritsidwa.





## Gawo la sewero 58

# Mfumu Imangidwa

Unali usiku woyandikira tsiku la phwando lapachaka lopereka nsembe, lotchedwa Paska. Tsiku lotsatiralo ana ankhosa ochuluka amaphedwa.

Ngakhale kuti Yesu amadziwa kuti nayenso amakaphedwa tsiku lotsatiralo, Iye anakhala limodzi ndi ophunzira ake, nagawana nawo chakudya cha madzulo chomaliza. Panthawi ya chakudya, Yesu anatenga mkate, ataudalitsa, anaunyema, ndikuwapatsa iwo kuti adye. Kenaka anayendetsa chikho cha vinyo. Anawauza kuti mkatewo uyenera kuwapanga iwo kuganiza za thupi lake ndipo vinyoyo kuganiza za mwazi wake omwe udzakhetsedwe kubweretsa chipangano chatsopano cha chikhululukiro cha machimo.

Pakati pa usiku, anatsogolera ophunzira ake ku munda wa Getsemane. Kumeneko, podziwa zoopsa zomwe zimamudikira, anapemphera kwa Atate wake.

Mwadzidzi atsogoleri achipembedzo anafika ndi gulu la anthu litanyamula zida. Yesu anati kwa iwo,


> "Kodi Ndine woukira owopsya, mpaka kubwera ndi malupanga ndi zibonga kuti mundimange? Kodi chifukwa chiyani simunandimangire mu kachisi? Ndinali m'menemo kuphunzitsa masiku onse. Koma izi zonse zikuchitika kukwaniritsa zonenedwa ndi aneneri monga analembera mu malemba oyera."
>
> Pomwepo ophunzira anathawa ndikumusiya Iye. (Mateyu 26:55-56)

Yesu anawalola anthuwo kumumanga ndi kupita naye kunyumba ya wa nsembe wamkulu, komwe olamulira a chiYuda anali atasonkhana. Anthu anamunenera Yesu za bodza.

> Kenaka wansembe wamkulu anaimilira ndi kumufunsa Yesu, "Kodi suyankha? Kodi ndi umboni wanji uwu omwe anthu akukubweretsera?" Koma Yesu anapitirirabe kukhala chete ndipo sanapereke yankho. Wansembe wamkulu anamufunsanso, "Kodi ndiwe Khristu, mwana wa odalitsikayo?"
>
> "Ndine," ananena Yesu. "Ndipo mudzawona mwana wa munthu atakhala kudzanja lamanja la Wolemekezekayo komanso akubwera m'mitambo."
>
> Wansembe wamkulu anang'amba zovala zake. "Kodi tifuniranji mboni zina?" anafunsa. "Mwamva mwano wake. Kodi mukuganiza bwanji?"
>
> Onse anamuweruza kuti amayenera kufa.
>
> Ndipo ena anayamba kumulavulira Iye, kumuphimba nkhope yake, kum'tosa, ndikum'funsa, Lota! Ndipo anyamatawo anam'menya Iye pama. (Marko 14:56,60-65)

Bwalo loweruza milandu la chiYuda linali litavomereza zoti aphedwe, koma analibe ulamuliro wokwaniritsa izi pa Iye. Bwalo loweruza milandu la chiRoma lokha ndi lomwe linayenera kupereka chigamulo cha imfa.





## Gawo la sewero 59

# Mfumu ipangidwa kukhala wolakwa

Unali m'mamawa kwambiri pamene olamulira achipembedzo ndi gulu la anthu linamutsogolera Yesu kuchoka ku nyumba ya wankulu wa achipembedzo kudzera mu mzinda wa Yerusalemu kupita ku nyumba ya chifumu kwa wamkulu wa chiRoma, Pontio Pilato.

Atsogoleri azipembedzo amafuna Pilato avomereze kuti Yesu aphedwe.

Anafotokozera mulandu motere, “Munthu uyu wakhala akutsogolera anthu powasokoneza kuti asamapereke msonkho kuboma la chiRoma ndi ponama kuti ndi Mesiya, Mfumu.”

Atamaliza kumufunsa mafunso Yesu, Pilato anatembenukira kwa wa nsembe otsogolera.

Ndi ku gulu la anthu ndi kunena: “Sindikupeza cholakwa chilichonse ndi munthu Uyu!” (Luka 23:2,4)

“Akanakhala kuti siolakwa, sitikanabwera naye kwa inu…” anayakha choncho anthuwo.

Pilato kenaka anabwerera mkati mwa nyumba ya chifumu kuzenga mlandu Yesu ndi kumufunsa:

“Kodi ndiwe mfumu ya Ayuda? … Kodi ndi chiyani chomwe wapanga?”

Yesu anati: “Ufumu wanga siwadziko lapansi lino. Ukanakhala kuti ndi wa padziko lapansi, a ntchito Anga akanapanga nkhondo kunditeteza kuti ndisamangidwe ndi Ayuda. Koma Ufumu Wanga ndi ochokera malo ena.”

“Ndiwe mfumu ndiye kuti!” Anatero Pilato.

Yesu anayankha, “Mwalondola ponena kuti Ndine Mfumu. Ndi chifukwa chake Ndinabadwa, ndi kubwera pa dziko lapansi, kudzachitira umboni choonadi. Aliyense amene ali mbali ya choonadi amamvera Ine.”

“Kodi choonadi ndi chiyani?” Pilato anafunsa.

Anatulukilanso kwa Ayudawo, nanena nawo, ine sindikupeza konse chifukwa mwa Iye.” (Yohane 18:30,33,35-38)

Koma gulu la anthu linapitirizabe kukuwa:

“Apachikidwe! Apachikidwe!”

Kwa nthawi yachitatu Pilato anayankhula nawo anthuwa: “Chifukwa chiyani? Kodi wapalamula mlandu otani? Ndamupeza kuti sakuyenera kulandira chilango chophedwa. Choncho angolangidwa ndipo kenaka mumumasule.”

Koma anthu anamkakamiza ndi mawu okweza, napempha kuti Iye apachikidwe, ndipo zofuna zawo zinavomelezedwa. (Luka 23:21-23)

Pilato amadziwa kuti Yesu anali osalakwa, koma chifukwa chochita mantha ndi atsogoleri azipembedzo pamodzi ndi gulu la anthu, anamuweluza Yesu kuti aphedwe.





## Gawo la sewero 60

# Mfumu Ibvekedwa Korona

Pilato anapereka chilango chachikulu kwambiri mu chilamulo cha chiRoma kwa Yesu: kumumenya mwa nkhaza kenaka ndikumupachika. Onse amene anapezeka olakwa anakwapulidwa ndi zida zachitsulo.

Zaka mazana asanu ndi awiri zambuyomo, Ambuye anamuuza mneneri Yesaya kuti alembe:

> "Ndinapereka msana wanga kwa omenya ndi masaya anga kwa iwo amene anakudzula tsitsi langa; sindinabisira nkhope yanga manyazi ndi kulavulilidwa." (Yesaya 50:6)

Uthenga wabwino umatiwuza ife zomwe zinatachitika Ambuye atakwapulidwa.

> Ena mwa asilikali anamutengera Yesu kulikulu lawo ndi kuitana gulu la asilikali onse.
>
> Anamuvula ndi kumuveka mkanjo wofiira.
>
> Ndipo anamulavulira namukwapula. Ndipo analuka chisoti cha minga, namuveka pamutu pake, namugwiritsa bango m'dzanja la manja lake, ndipo anagwada pansi pa maso pake, namuchitira chipongwe, nati, tikuoneni mfumu ya Ayuda. (Mateyu 27:27-30)

Asilikali samadziwa za tanthauzo la chisoti chaminga chomwe anamuveka m'mutu Mwake. Minga zinali mbali ya themberero lomwe linabwera chifukwa cha tchimo la Adamu. Mfumu yolungama ndi ya ulemerero inali itabwera kudzachotsa themberero la tchimo kwa ife.

> Ndipo pamene anatha kumchitira Iye chipongwe, anamuvula mwinjiro uja namuveka zovala zake, kenako anamtsogoza Iye kukampachika pa mtanda. (Mateyu 27:31)


Awiri olakwa pa mlandu anatengedwanso pamodzi ndi Yesu. Aliyense ananyamula mtanda wake kupita ku malo okaphedwa.

Pochoka mu pelete oopsa, asilikali AchiRoma anakakamiza mzibambo ochokera kumpoto kwa Africa kuti amunyamulire Yesu mtanda. Kenaka anapitirira, mu misewu yodzaza ndi anthu ya Yerusalemu, kunja kwa mizinda, kupita pamwamba pa phiri lotchedwa Gologota, mbali ya kumpoto kwa phiri la Moria, kwa zaka zikwi ndi mazana asanu ndi anayi oyambirira, mneneri Abrahamu ananena:

> "Mulungu adzadzifunira Yekha mwana wa Nkhosa wa nsembe yopsereza." (Genesis 22:8)

Inali nthawi yakuti mwana wa Nkhosa afe.





## Gawo la sewero 61

## Mfumu Ipachikidwa pamtanda

Imfa ya pa mtanda ndi yoopsa kwambiri –imene boma limagwiritsa ntchito pofuna kupha munthu amene walakwira malamulo. Powonjezera kumuchititsa manyazi pa gulu la anthu, asilikali AchiRoma anamuvula zovala, akufuna kumubaya misomali m'manja ndi m'miyendo yake pamtanda.

> Pamene anafika kumalo otchedwa Bade, anamupachika pamtanda, pamodzi ndi zigawenga—chimodzi chinali ku manja kwake, chinacho chinali kumanzere kwake. Yesu anati: "Atate, akhululukireni, poti sakudziwa zomwe akuchita."
>
> Ndipo anagawana zovala zake nachita maere. Anthu anaima ndi kumawonera, ndipo ngakhale olamulira anamunyogodola. Anati:
>
> "Anapulumutsa ena; muloleni adzipulumutse yekha ngati ali Khristu wa Mulungu." (Luka 23:33-35)

Akanakhala kuti Yesu anadzipulumutsa yekha, sakanatipulumutsa ife. Chinamtindi cha anthu sichimadziwa kuti chimakwaniritsa zomwe Ambuye anali atayankhula kwa mneneri Davide:

> "Abaya manja anga ndi miyendo yanga. … Anthu anayang'ana ndi kundiyang'ana mondinyogodola ine. Anagawana zovala zanga ndi kupanga maere za Malaya anga ambiri. … Onse omwe akundiona ine ndi kusereulidwa; kutukwanidwa, kugwedeza mitu: '… Adzampulumutsa. Amulanditse tsopano popeza akondwera naye!" (Masalmo 22:16-18,6-8)

Dongosolo lakupulumutsa la Mulungu linakwaniritsidwa mwatsatanetsatane.

Pa phiri pomwepo[11] pamene m'neneri Abrahamu anati, Mulungu yekha adzapereka mwana wa nkhosa, ndi, Yehova-Yireh" (Genesis 22:8,14), Mulungu anali atapereka mwana wake wa nkhosa—Yesu.

Mukukumbukira m'mene mwana wankhosa osalakwa kanthu amene anaperekedwa nsembe pa guwa la Abrahamu m'malo mwa mwana wake? Tsopano mwana osalakwa kanthu wa Mulungu anaperekedwa pa mtanda m'malo mwa mtundu wochimwa wa Adamu. Iye amene sanatimana mwana wake wa Iye yekha, koma anam'pereka chifukwa cha ife tonse." (Aroma 8:32)

> Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha. (Yohane 3:16)
>
> Podziwa kuti simunawomboledwa ndi zovunda, golide ndi siliva kusiyana nawo makhalidwe anu achabe ochokera kwa makolo anu. Koma ndi mwazi wake wa mtengo wapatali monga wa mwana wa nkhosa opanda chilema, ndiwopanda banga, ndiwo mwazi wa Khristu. (1 Peter 1:18-19)

Ndi m'mene mtengo wanu ulili kwa Mulungu.





## GAWO LA SEWERO 62
# MPULUMUTSI-MFUMU

Pokwaniritsa dongosolo la chipulumutso cha Mulungu, Ambuye Yesu anachititsidwa manyazi ndi zomwe tchimo limabweretsa.

Anatembereredwa m'malo mwa ife. Anatenga chilango chomwe chimatiyenera ife.

Tsiku lina Adamu anaphwanya malamulo a Mulungu, Mulungu anadzipanga kuti zidziwike kuti Mesiya tsiku lina adzamuphwanya Satana. Mulungu anali atamuuza Satana:

> "Ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chitende chake." (Genesis 3:15)

Uneneri wa kale, wodabwitsa okamba za momwe Satana adzalalira chitende cha mpulumutsi unakamba za manyazi ndi ululu wa mwana wa nkhosa ya Mulungu amene adzazunzike pamtanda pamene "adzalasidwa chifukwa cha zolakwa zathu." (Yesaya 53:5)

Anthu amene anamupachika Yesu pa mtanda sankadziwa za dongosolo la chinsinsi cha Mulungu.

> Palibe ngakhale mmodzi wa olamulira a nthawi imeneyo anazimvetsetsa, popeza akanakhala kuti ankadziwa, sakanakamupachika Ambuye wa ulemerero pa mtanda.
>
> Pakuti mawu a mtanda ndi chinthu chopusa kwa iwo akutayika koma kwa ife amene tili kupulumutsidwa ali ndi mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:8; 1:18)

Mtanda wa Yesu unaikidwa pakati pa zigawenga ziwiri.

> M'modzi wa zigawengazo amene anapachikidwa pamenepo anayankhula chipongwe kwa Iye: "Kodi si Iwe Khristu? Dzipulumutse Wekha ndi ife tomwe!"
>
> Koma chigawenga china chinamudzudzula. "Kodi suopa Mulungu," anatero, "poti mwalandira chilango chofanana? Tikulangidwa mwachilungamo, pakuti tilandira chilango chogwirizana ndi ntchito zathu. Koma munthu uyu sanapanga chilichonse cholakwa." Kenaka anati: "Yesu, mukandikumbukire mukapita mu ufumu Wanu."
>
> Ndipo Iye ananena naye, indetu Ndinena ndi iwe, lero lino udzakhala ndi Ine m'Paradizo." (Luka 23:39-43)

Chigawenga choyamba chimangofuna kupulumutsidwa ku zowawa za kuthupi. Sananganizire kuti amafunika Mpulumutsi kufa m'malo mwa iye.

Chigawenga chachiwiri chinalinso chitamunyoza Yesu. Koma pamene amakumana ndi imfa, anali atatembenuka mtima. Amafuna Ambuye amupulumutse ku ufumu wa Satana. Amafuna kukhala nzika ya ufumu wa Mulungu, ngati Mfumu ikanakhala naye. Yankho la Yesu lasiyidwa opanda chikaiko:

> "Lero lino uzakhala ndi ine m'Paradizo" (Luka 23:43)

Patapita nthawi madzulo, zigawenga zonse zinafa. China chinapita kugahena. China chinapita ku paradizo. Kodi chinapangitsa kusiyana ndi Chiyani?

M'modzi sanaike chikhulupiriro chake mwa Mpulumutsi-Mfumu. Wina anaika.





## Gawo la sewero 63

# Kupereka nsembe komaliza

Ndi masana. Yesu wakhala kale pa mtanda kwa maola atatu. Mitambo yakuda yagwa. Usana wakhala usiku. Anthu owonerera anamwazikana ndi mantha.
M'phiri munali bata lochititsa mantha. Maola atatu atadutsa, Yesu analira:

> "Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji?" (Mateyu 27:46)

Paguwa la mtanda, Mwana yekhayo wa Mulungu anamva kuwawa kosiyanitsidwa ndi Mulungu kumwamba. Pa nthawi ya mdima umenewo, maso a anthu anabisika, Mulungu anatenga machimo athu onse ndi kuwaika mwa mwana wake woyera. Yesu anakhala chopereka chomaliza cha tchimo.

Machimo onse akale, a tsopano ndi amtsogolo a dziko lapansi anayikidwa pa Yesu, Mulungu anayenera kuyang'ana kumbali chifukwa chakuti "maso ake sapenya choyipa." (Habakuku 1:13) Kwa maola atatu, mkwiyo wa Mulungu pa tchimo unaotcha chopereka chake chomwe. Ngati mwana wa nkhosa kuperekedwa nsembe pa guwa, mwana wa nkhosa wa Mulungu anakhomeredwa pa mtanda pakati pa kumwamba ndi padziko lapansi, pakati pa Mulungu ndi munthu. Wamuyayayo anapirira ku zowawa za machimo athu mu nthawi yake kuti ife tisalipire zowawa kwa nthawi zonse.

Kenaka zinachitika.

Podziwa kuti anali atalandila chilango chomwe chimayenera anthu ochimwa ndi kuti anali atakwaniritsa mauneneri a chipangano chakale, Yesu anati:

"Kwatha!"

> Ndipo anawerama mutu napereka Mzimu. (Yohane 19:30)

> Ndipo onani chinsalu chotchinga cha m'kachisi chinang'ambika pakati, kuchokera kumwamba kufikira pansi; Ndipo dziko linagwedezeka, ndi miyala inang'ambika. (Mateyu 27:51)

Kwa zaka mazana mazana, ana ankhosa anakhala akuphedwa ndi kuotchedwa pa guwa la kachisi. Pamene Yesu anafa, Mulungu anang'amba chinsalu chomwe chimabisa chipinda chopatulika kumene magazi amawazidwa chaka chilichonse kuti aphimbe tchimo. Pong'amba chinsalu, Mulungu amalamula:

*Kwatha! Ngongole ya tchimo yaperekedwa mokwanira! Mwana wanga wa nkhosa wakhetsa mwazi wake woyera chifukwa cha tchimo la dziko lapansi. Sindidzavomeranso magazi achinyama chifukwa cha tchimo. Mwana wanga okondedwa ndi nsembe yomaliza kwa onse amene akhulupirira mwa iye, nkhomo la kumwamba ndi lotsegula!* (Onani buku la Aheberi mu chipangano chatsopano.)

Seven hundred years earlier, the Mneneri Yesaya wrote,

> Koma Iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango chotitengera ife mtendere chinamgwera iye; ndipo ndi mikwingwirima yake ife tinachirisidwa. Tonse tasochera ngati nkhosa; tonse tayenda yense njira ya mwini yekha ndipo Yehova anayika pa iye mphulupulu ya ife tonse. (Yesaya 53:5-6)

Kwatha!





## Gawo la sewero 64

# Mfumu Iyikidwa m'manda

Yesu waku Nazareti anali atafa. Pofuna kutsimikiza, msilikali anamubaya ndi mkondo mu nthiti mwake. Magazi ndi madzi anatuluka.

Ophunzira analibenso chiyembekezo. Poganiza kuti Yesu akanangowononga Aroma ndi kupanga ufumu wake padziko lapansi, ophunzira anali asanamvetsetsebe za lonjezo lake kuti azauka tsiku lachitatu.

Matupi akufa a anthu opachikidwa pa mtanda nthawi zambiri amatayidwa ngati zinyalala kunja kwa mzinda. Kapena kuikidwa ku manda a unyinji. Koma osati ndi thupi la Yesu. Zaka zikwi zisanu ndi ziwiri zoyambirira, mneneri Yesaya anali atalemba:

> "Ndipo anayiika pamodzi ndi oyipa, ndi pamodzi ndi olemera mu imfa yake …." (Yesaya 53:9)

Mulungu anapanga ganizo loti mwana wake aikidwe m'manda mwa ulemu.

> Ndipo pamene panali madzulo, anadza munthu wa chuma waku Arimateya, dzina lake Yosefe amene analinso ophunzira wa Yesu. Yemweyu anapita kwa Pilato, napempha mtembo wa Yesu, pomwepo Pilato analamula kuti mtembo uperekedwe. (Mateyu 27:57-58)

Imfa ya Yesu isanachitike, Yosefe waku Arimateya ndi mnzake Nicodemo anali omutsatira Yesu Mesiya mwa chinsinsi. Amaopa atsogoleri a zipembedzo. Koma atamuona Yesu akuvutika pa mtanda, sanaopenso ayi. Ndiye anatenga thupi la Yesu, kulitsuka, ndi kulikulunga mu milezi milezi ya nsalu zoyera pamodzi ndi mure wapafupifupi makilogamu 35, mtundu omwewo wa mafuta onunkhiritsa okwera mtengo omwe Anzeru akumawa anamupatsapo Yesu ali wamng'ono. Kenaka anaika thupi lake mu manda atsopano a Yosefe. Atamaliza kugubuduza chimwala chachikulu kutseka pakhomo lolowera ndipo anapita kunyumba.

Kunali kuikidwa m'manda kwa chifumu, kokwanira mfumu.

M'mamawa atsogoleri azipembedzo anapita kwa Pilato.

> Nanena: "tikukumbukira kuti pamene anali ndi moyo wosokoneza uja anati: 'Pakadutsa masiku atatu ndidzadzukanso.' Ndiye mupereke malamulo a manda kuti atetezedwe kufikira tsiku lachitatu. Mwina, ophunzira ake akhoza kubwera ndi kuba thupi lake ndi kuwauza anthu kuti waukitsidwa kwa kufa. Chinyengo ichi chomalizira chidzafika poyipa kuposa choyambirira"
>
> Pilato anati kwa iwo: "Tengani alonda, mukani, kasungeni monga mudziwa. Ndipo iwo anamuka nasunga manda, nasindikizapo chizindikiro pa mwalapo, iwo pamodzi ndi alondawo." (Mateyu 27:63-66)

Pakadali pano, m'kati mwa manda, kodi chikuchitika ndi chiyani ku thupi la Yesu?

Palibe.





## Gawo la sewero 65

# M'manda mopanda kanthu

Kuyambira tsiku lomwe Adamu anachimwa, imfa inalamulira ngati mfumu yankhanza pa mtundu wa anthu. Yesu akanachimwapo, imfa inakapanganso thupi lake kuyamba kuola, kununkha. Koma zaka zana limodzi loyambirira, mneneri Davide anali atalemba:

> "Simudzalola wokondedwa wanu aone chibvundi." (Masalmo 16:9-10)

Imfa ndi manda zinalibe mphamvu pa amene sanachimwepo.

Pa tsiku lachitatu Yesu anaphedwa ndi kuikidwa m'manda, m'mamawa kwambiri wa lamulungu, amayi ambiri anabwera kumanda kuti adzapereke ulemu wawo. Mwadzidzidzi, kunali chivomerezi chachikulu pamene mngelo anabwera pansi kuchokera kumwamba, kukankhira mwala pambali, ndi kukhalapo. Asilikali anakomoka, koma mngelo anawauza amayi:

> "Musaope!" ananena. "Ndikudziwa mukufuna Yesu, amene anapachikidwa pamtanda. Sali muno! Wauka kwa akufa, ngati m'mene ananenera kuti zidzachitika. Bwerani, onani pamene thupi lake linagona. Ndipo tsopano, pitani fulumirani ndipo mukawauze ophunzira ake kuti wauka kwa akufa …"
>
> Amayi anathamanga mofulumira kuchoka m'mandamo. Anali ndi mantha kwambiri komanso kudzazidwa ndi chimwemwe, ndipo anathamanga kuti akawapeze ophunzira kuti awapatse uthenga wa mngelo.
>
> Pamene anali kubwerera Yesu anakumana nawo nanena; "Moni"! Anthu anam'thamangira nagwa pamapazi ake kumulambira. (Mateyu 28:5-9)

Nthawi yomweyo, asilikali anabwera mu mzinda ndi kuwauza atsogoleri azipembedzo zomwe zinachitika. Ndiye atsogoleri ananyengerera ndi ndalama zambiri, kuwauza:

> "nati: "muzinena kuti ophunzira ake anabwera usiku, namba Uja m'mene ife tinali m'tulo." (Mateyu 28:13)

Koma bodza lawo silikanabisa chilungamo. *M'manda munalibe kanthu!*

Yesu analipira ngongole ya machimo athu ndi imfa yake. Ndi kuikidwa m'manda kwake, Yesu anapita pansi pa dzenje la imfa ndi kuola. Ndi kuuka kwake kwa akufa, Yesu anagonjetsa imfa, ndipo tsopano akunena:

> "Usaope, Ine ndine woyamba ndi wotsiriza, ndi Wamoyoyo; ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi ndipo ndili nazo zofungulira za imfa ndi gahena." (Chibvumbulutso 1:17-18)

Kwa onse amene amakhulupirira uthenga wabwinowu, imfa ndi khomo limene limangotseguka kuti akafike pamaso pa Mfumu amene ananena kuti:

> "Popeza Ine ndili ndi moyo inunso mudzakhala ndi moyo." (Yohane 14:19)





## Gawo la sewero 66
# Uthenga wa Aneneri

Pa tsiku limene Yesu anauka kwa akufa, Iye anaonekera kwa ambiri a ophunzira ake:

> Koyambirira kwa amayi, kenaka kwa Petro, ndi kwa anthu awiri a paulendo…
>
> Tsiku lomwelo awiri a otsatira a Yesu amapita ku mudzi wa Emau, mitunda isanu ndi iwiri kuchokera ku Yerusalemu.
>
> Mwadzidzidzi Yesu mwini wake anabwera ndi kuyamba kuyenda nawo. Koma Mulungu anapanga kuti iwo asamuzindikire Iye. Anawafunsa, "Kodi mukukambirana chiyani mwa chidwi kwambiri pamene tikuyendapa?"
>
> Anayima kwa kanthawi kochepa, kukhumudwa kunaoneka pa nkhope zawo. Kenaka m'modzi mwa iwo, Kleopa, anayankha, "mukuyenera kukhala munthu yekhayo mu Yerusalemu amene sanamve za zinthu zonse zomwe zachitika kumeneko kwa masiku ochepa apitawo."
>
> Ndipo anati kwa iwo, zinthu zanji? (Luka 24:13,15-19)

Anthu a paulendo ananena m'mene amamuyembekezera Yesu waku Nazareti kuti akanakhala. Mesiya pogonjetsa adani awo. Koma anapachikidwa pamtanda! Ndipo tsopano m'mandamo mulibe kalikonse. *Sizinapereke nzeru!*


> Kenaka Yesu anati kwa iwo, "Anthu opusa inu! Mukuziona zovuta kukhulupirira zonse zomwe aneneri analemba mu malembo oyera. Kodi sizinaloseredwe momveka bwino kuti Mesiya ayenera kuvutika mu zinthu zonsezi asanalowe mu ulemerero wake?"
>
> Kenaka Yesu anawaonetsa zolemba za Mose ndi aneneri onse, nawafotokozera iwo kuchokera mu zolembedwa zonse zinthu zonse zokhudza Iye mwini.
>
> Panthawi yomwe amayandikira ku Emau ndipo kumathero kwa ulendo wawo. Yesu anaonetsera ngati akupitirira, koma anamupempha kuti a bwerere, "mukhale nafe usiku uno, poti kukuda." Ndiye anapita nawo limodzi kunyumba.
>
> Pamene anakhala pansi kuti adye, anatenga mkate ndi kuudalitsa. Kenaka anaunyemwa ndi kuwapatsa. Nthawi yomweyo, maso awo anatseguka, ndipo anamuzindikira Iye. Kenako posakhalitsa anasowa!
>
> Ndipo anati wina kwa mnzake, mtima wathu sunali wotentha m'kati mwathu nanga m'mene anayankhula nafe m'njira, m'mene anatsegulira malembo?" (Luka 24:25-32)

Anathamanga ndi kubwerera ku Yerusalemu kukawauza ophunzira: *Ambuye ali moyo! Ndi Mpulumutsi olonjezedwa mu malembo oyera! Ndi Mwana wa Nkhosa amene akuoneka mukupereka nsembe! Iye ndiye AMBUYE*

Pomaliza uthenga wa aneneri ukumveka bwino.

Kumveka bwino ndithu.





## Gawo la sewero 67
# Thupi Losandulika

Linali tsiku lamulungu madzulo. Ophunzira anali pamodzi, ndi zitseko zotseka. Mwadzidzidzi Yesu anaonekera mu chipinda ndi kunena:

> "Mtendere ukhale ndi inu!"
>
> Ndipo pamene ananena izi, anawawonetsa iwo manja Ake ndi nthiti Zake. Pamenepo akuphunzira anakondwera pakuona Ambuye. (Yohane 20:19-20)

Tomasi, m'modzi wa ophunzira khumi ndi awiri a Yesu, sanali nawo pamodzi madzulo amenewo. Kenaka, ophunzira anamuuza, "Tamuona Ambuye!"


> Koma Tomasi anati kwa iwo, "Ndikapanda kuona m'manja ake chizindikiro cha misomaliyo, ndi kuika chala changa m'chizindikiro cha misomaliyo, ndi kuika dzanja langa ku nthiti yake; sindidzakhulupirira."
>
> Patatha sabata limodzi ophunzira ake analinso m'nyumba, ndipo Tomasi anali nawo limodzi. Ngakhale kuti zitseko zinali zotseka, Yesu anabwera ndi kuima pamaso pawo ndi kunena: "Mtendere ukhale ndi inu!"
>
> Kenaka ananena kwa Tomasi, "Bwera nacho chala chako kuno, nuone manja anga; ndipo bwera nalo dzanja lako, nuliyike ku nthiti yanga, ndipo usakhale wosakhulupirira, koma wokhulupirira."
>
> Tomasi anayankha nati kwa Iye: "Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga!"
>
> Yesu ananena kwa iye, "chifukwa wandiona Ine, wakhulupirira; odala iwo akhulupirira, angakhale sanaona." (Yohane 20:24-29)

Kwa masiku makumi anayi otsatira, Ambuye anakhala akuonekera kwa omutsatira ake ndi kuyankhula nawo, akatero amangosowa. Thupi loukitsidwa la Yesu Khristu limatha kudutsa angakhale makoma a nyumba komanso kuyenda mwachangu kwambiri. Ngakhale anali oyamba kukhala ndi thupi lotero, sadzakhala omaliza.

> Monga tavala fanizizo la wa m'nthakayo, tidzavalanso fanizo la wakumwambayo.
>
> Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso mwa munthu. Pakuti monga mwa Adamu onse amwalira, choteronso mwa Khristu onse akhalitsidwa ndi moyo. (1 Akorinto 15:49,21-22)

Kodi mumamvetsetsa kuti ndinu ochimwa, osowa chochita, opanda njira kuti mupeze zoyenera kuti mukhale mu ufumu wa Mulungu? Kodi mumakhulupirira kuti Ambuye Yesu Khristu anafa m'malo mwanu, chifukwa cha machimo anu ndi kubwerera ku moyo, kugonjetsa imfa chifukwa cha inu? Ngati zinali choncho, Mulungu akunena, sulinso mwa Adamu. Mulungu amakuonani inu ngati olungama mwa Khristu. Tsiku lina inunso mudzalandila thupi losandulika—ngati lake.

Koma lopanda zipsera za misomali.





## Gawo la sewero 68

## Kunyamuka

Ulamuliro umene Adamu anaulanditsa kwa Satana, Yesu anautenganso. Yesu anaonetsa kuti ulamuliro wonse uli m'manja mwake pa mdierekezi, ziwanda, mphepo, mafunde, matenda, njala, tchimo ndi imfa. Pamene atsogoleri azipembedzo ndi asilikali anamumanga, kumuzunza, ndi kumupachika pa mtanda, Iye anawalola kupanga zimenezi.

Ndi chifukwa chake, asanabwerere kunyumba kwa Atate wake, Ambuye Yesu anati kwa ophunzira ake:

> "Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi pa dziko lapansi, chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndikuwabatiza iwo M'dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera; ndikuwaphunzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani Ine ndilipamodzi ndi inu masiku onse kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano"(Mateyu 28:18-20)

Yesu anauzanso omutsatira ake kuti:

> "Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mnzake; monga ndakonda inu, kuti inunso mukondane wina ndi mnzake. Mwa ichi adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondano wina ndi mnzake." (Yohane 13:34-35)


Masiku makumi anayi Iye atauka kwa akufa, Yesu anasonkhanitsa ophunzira Ake Pa phiri la azitona kunja kwa Yerusalemu. Ophunzira amafuna kudziwa kuti Iye adzabweranso liti.

Yesu anawayankha kuti:

> "Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene Atate anaziyika mu ulamuliro wake wa Iye yekha. Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu oyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya lonse ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko."
>
> "Ndipo mmene adanena izi, ali chipenyerere iwo, ananyamulidwa; ndipo mtambo unamulandira Iye kum'chotsa kumaso kwao."
>
> Pamenepo anabwera ku Yerusalemu …. (Acts 1:7-12)

Mu nthawi imeneyo kumwamba, Mfumu imavekedwa "korona wa ulemerero ndi ulemu."
(Masalmo 8:5; Ahebri 2:9)





## Gawo la sewero 69
# Chikondwerero Chakupambana

Tangoganizirani kukongola. Mitundu. Nyimbo. Kusangalala. Angelo osawerengeka kuyankhulana okhaokha: *Mfumu ikubwera kunyumba! Koma idzaoneka mosiyana. Amene anamulenga munthu mu chifanizo cha Mulungu, adzakhala mu chifanizo cha munthu nthawi zonse!*

kumwamba kunakhala bata.

Mwadzidzidzi bata linatha ndi nyimbo za mphamvu za malipenga, zotsogozedwa ndi kufalitsa uthenga mwa mphamvu:

> Weramutsani mitu yanu zipata inu; ndipo kwezani inu, zitseko zosatha: Kuti Mfumu ya ulemelero ilowe. Mfumu ya ulemelero ndani? Yehova wa mphamvu ndi wolimba, Yehova wolimba ku nkhondo. Weramutsani mitu yanu zipata inu; Inde weramutsani, zitseko zosatha inu, kuti Mfumu ya ulemerero ilowe. Mfumu imene ya ulemerero ndani? Yehova wamakamu makamu ndiye Mfumu ya Ulemelero! (Masalmo 24:7-8,10)

Zipata zinatsegulidwa ndi kusangalala kwakukulu kumwamba. Anadza katswiri, Mwana wa nkhosa, Mwana wa munthu ogonjetsa nkhondo—Yesu! Iye anayenda kudutsa khwimbi la anthu omupembedza, mpaka kufika ku mpando wa chifumu wa atate wake. Potembenuka, anayang'ana pa dipo limene Adamu ankalifunafuna amene ali Yesu, ndikukhala pansi.

Cholinga chinakwaniritsidwa.

Zitatha izi mbadwa za kumwamba zinayimba nyimbo yatsopano kwa Mfumu yao yokondedwa:

> "Muyenera kulandira bukulo,... chifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu amafuko onse, ndimanenedwe onse ndi mitundu yonse." (Chibvumbulutso 5:9)


Kenako angelo anazungulira mpando wa chifumu, kulemekeza Mulungu, nanena kuti:

> "Ayenera mwana wa nkhosa, wophedwayo, kulandira chilimbiko, ndi chuma, ndi nzeru ndi mphamvu ndi ulemu ndi ulemerero, ndi chiyamiko!" (Chibvumbulutso 5:12)

Lero anthu ambiri padziko lapansi a m'badwo wa Adamu akanali mu goli loweruzidwa mu ufumu wa Satana wa tchimo ndi imfa. Koma ufulu ulipo. Chifukwa cha imfa yake, kuikidwa m'manda, ndi kuuka kwa akufa, Ambuye Yesu anapambana nkhondo yofunikira. Kwa onse amene amakhulupirira iye, akuti:

> "Mtima wanu usavutike. Mukhulupirira Mulungu, khulupirirani inenso. Mnyumba mwa Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri...ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha."
>
> "Ine ndine njira, ndi chowonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine." (Yohane 14:1-3,6)





## Gawo la sewero 70

# Mfumu ikubweranso

Tsiku lina, pamene dziko latanganidwa ndi kufunafuna zinthu zosafunikira ndi zipembedzo zabodza, Mfumu ya ulemerero idzabwerera padziko lapansi, koma osati pa bulu, osatinso ali wonyozeka ndi kubvekedwa chisoti cha minga.

Mfumu youka kwa akufa inamupatsa Yohane chithunzithunzi cha mtsogolo za tsikuli:

> Ndipo ndinaona mutatseguka m'Mwamba; ndipo taonani, kavalo woyera, ndi Iye wakumkwera wotchedwa Wokhulupirika ndi Woona; ndipo aweruza, nachita nkhondo molungama. Ndipo maso ake ali lawi la moto, ndipamutu pake pali nduwira zachifumu zambiri ndipo atchedwa dzina lake Mawu a Mulungu. Ndipo magulu ankhondo okhala m'Mwamba anamtsata Iye, okwera pa kavalo oyera, wovala bafuta woyera woti mbuu! Ndipo ali nalo pachovala chake ndi pa ntchafu yake dzina lolemba, MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE. (Chibvumbulutso 19:11-14,16)

Pamene Mfumu izidzabwerera, mawu adzagwedeza kuchokera kumwamba:

> "Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Khristu wake, ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi ndi nthawi!" (Chibvumbulutso 11:15)

Adani a Mfumu adzanyenyeka pa maso pake. Kenaka adzamumanga Satana. ndikuliwonetsa dziko lofooka m'mene boma lolungama limaonekera. Idzakhala nthawi yamtengo wapatali ya dziko lapansi.

> Ndipo Yehova adzakhala Mfumu ya mu dziko lonse. Tsiku lomwelo Yehova adzakhala Iye yekha, ndi dzina lake ilo lokha. (Mneneri Zechariah 14:9)

Patsiku la chiweruzo, AMBUYE Yesu adzakhala woweruza.

> Anakhala pa mpando wachifumu. Mpandowu unali Malawi amoto ndi njinga zake moto woyaka. Mtsinje wamoto unayenda wotuluka pa maso pake, zikwizikwi anamtumikira, ndi unyinji wosawerengeka unayima pamaso pake, woweruza mlandu anakhalapo, ndi mabuku anatsegulidwa. (Mneneri Daniel 7:9-10)

Satana ndi ufumu wake adatayidwa m'nyanja yamoto." (Chibvumbulutso 20:10) Patsiku lomaliza, mutu wa Satana udzaphwanyidwa mpaka kalekale.

Kwa anthu amene adzakhale mu Ufumu Woyera, Mulungu adzawapangira "Kumwamba kwa tsopano ndi dziko lapansi latsopano...ndi iwo adzakhala anthu Ake, ndi Mulungu yekha adzakhala nawo, Mulungu wao; ndipo adzawapukutira misozi yonse pa maso pawo; ndipo sipadzakhalanso imfa, ndipo sipadzakhalanso maliro kapena kulira." (Chibvumbulutso 21:1,3-4)

Patsiku lomaliza, pemphero la onse omwe amakonda Mfumu yawo lidzamveredwa mpaka kalekale:

> "Kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba chomwecho pansi pano!" (Mateyu 6:10)

Kodi ili ndi pemphero lanu? Kodi mwaigwadira Mfumu ya ulemerero?

Kodi ndi Mfumu yanu?



# Matero

Indetu, indetu, Ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mawu Anga, ndi kukhulupirira Iye Amene ananditumа Ine, ali nawo moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wachokera ku imfa, nalowa m'moyo.

— Yesu, Mfumu ya Ulemerero (Yohane 5:24)

Anali m'dziko lapansi, ndi dziko linalengedwa ndi Iye, koma dziko silinamzindikira Iye. … Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina Lake.

— Uthenga wabwino (Yohane 1:10,12)

## Uthenga Munkhani • 1

# Kusangalala kwa muyaya?

Anthu amibadwo yonse amakonda nthano za chikondi ndi zopulumutsa, nkhani zamathero osangalatsa. Anthu amanena nthano za mtundu oterewu chifukwa choti Mulungu m'modzi wa chilungamo wamanga mu mtima mwa munthu kufunitsitsa koti kuperekedwe kuchoka kwa oyipa ndi kukhala osangalala kwa muyaya. Koma nkhani ya Mfumu ya ulemerero sinthano yopeka.




Nkhani yokhulupirira yongopanga simalembedwa ndi aneneri makumi anayi kwa zaka mazana mazana zopitirira khumi ndi zisanu, koma buku Mulungu linalembedwa. Nkhani yopeka simatsimikizidwa ndi ndi mazana mazana a uneneri ndi kafukufuku wa mbiri, koma nkhani ya Mulungu inatsimikizidwa.



Katswiri womukhulupirira wopangidwa samakhala mbali yogawa mbiri, koma Yesu anagawa. Kuyerekeza sikungathe kuchotsa tchimo lathu ndi manyazi athu, kutibweretsa ife kwa Mulungu, ndi kutipatsa ife mtima watsopano odzadza ndi chikondi chake, chisangalalo chake, ndi mtendere wake, koma Yesu angthe.


Pokwaniritsa malembo abwino a aneneri, Yesu Mesiya wazipanga kukhala zotheka kwa mibadwo ya Adamu kukhala kwa muyaya ndi Mfumu yawo mlengi. Koma onse sadzakhala mu ufumu wake.

Ngati m'mene Mulungu anapangira lamulo lake limodzi momveka bwino kwa Adamu bwino la kakhalidwe ka m'munda wa dziko lapansi, ndiye Mulungu wapanga lamulo lake limodzi momveka bwino kwa mibadwo ya Adamu la kakhalidwe ka mumzinda wa kumwamba:



Ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakuchita chonyasa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa m'buku la moyo la mwana wankhosa. (Chivumbulutso 21:27)

Buku la moyo la mwana wankhosa ndi kalembera wakumwamba ndi dzina la munthu aliyense amene, kuchokera nthawi ya Adamu, wakhulupirira njira ya Mulungu ya chipulumutso. Mfumu ya ulemerero sidzakakamiza inu kapena banja lanu kukhulupirira iye ndi zomwe wapanga pokupulumutsani inu kwa Satana, tchimo, imfa, ndi gehena.



Sikudzakhala nzika zosafuna mu ufumu wake. Koma chifukwa mfumu sikufuna aliyense kuti adzathe kwatunthu, anatseka buku lake ndi kuitana, kuchenjeza, ndi lonjezo:

"Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, idzani. Ndipo wakumva ludzu adze; iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere. Ndichita umboni kwa munthu aliyense wakumva mawu a chinenero cha buku ili, munthu akaonjeza pa awa, adzamuonjezera Mulungu miliri yolembedwa m'bukumu, ndipo aliyense akachotsako pa mawu a buku achinenero ichi, Mulungu dzamuchotsera gawo lache pa mtengo wa moyo, ndi mzinda woyerawo, ndi pa izi zilembedwa m'bukumu. Iye wakuchitira umboni izi, anena indetu, ndiza msanga. Amen Idzani, Ambuye Yesu!" (Chibvumbulutso 22:17-20)

Adamu atachimwa, kodi anati chiyani kwa Mulungu pamene Mulungu anabwera m'munda ndi kumamuitana? Adamu mwa manyazi anayankha,

> "Ndipo anati, ndinamva mawu anu m'mundamu, ndipo ndinaopa" (Genesis 3:10)

Koma tsopano, kodi ena mwa mibadwo ya Adamu amachitapo chiyani pa lonjezo la Ambuye lobwera padziko lapansi chifukwa cha iwo? Mwasangala amayankha,


> "Amen. Idzani, Ambuye Yesu!" (Chibvumbulutso 22:20)

Kodi ndi chiyani chinabweretsa kusintha kwa mtundu umenewu? Kodi ndi chifukwa chiyani anthu ena sakuopanso kuima pamaso pa oweruza wa dziko lapansi? Kodi ali osangalala chifukwa chiyani kumuona Mfumu mason di maso?


Ndi chifukwa choti amakhulupirira nkhani ndi uthenga wake.

Mneneri Yesaya analemba,

> Ndani wamvera uthenga wathu? Ndi mkono wa Yehova wavumbukira yani? … Tonse tasochera ngati nkhosa, tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa iye mphulupulu ya ife tonse. (Yesaya 53:1,6)




Yesaya anaphatikiza nkhani ndi uthenga wa Mfumu mu kalongosololedwe ka nkhani zitatu:



**1. Tili ndi vuto.**
"Tasiya njira za Mulungu ndi kutsatira njira zathu."

**2. Mulungu ali ndi yankho.**
"AMBUYE anaika pa [mwana wake] machimo a ife tonse."



**3. Tili ndi mwayi osankha.**
"Kodi ndi ndani wakhulupirira uthenga wathu?"

Kodi mumakhulupirira Mfumu?

> Tikuvomereza umboni wa munthu, koma umboni wa Mulungu ndi opambana chifukwa ndi umboni umene Mulungu wapereka wokhudzana ndi Mwana wake.…
>
> Aliyense amene samakhulupirira Mulungu wamupanga Iye kukhala wonama, chifukwa sanakhulupirire umboni umene Mulungu wapereka wokhudza mwana wake. Ndipo umboniwu ndi uwu: Mulungu watipatsa ife moyo osatha, ndipo moyo umenewu uli mwa mwana wake. Amene ali ndi mwana ali ndi moyo; amene alibe mwana wa Mulungu alibe moyo.
>
> Ngati tilandira umboni wa anthu, umboni wa Mulungu ndi oposa; chifukwa umboni wa Mulungu ndi uwu, kuti anachita umboni za mwana wake. Iye amene amakhulupirira mwana wa Mulungu ali nawo umboni mwa Iye; amene sakhulupirira anamuyesa Iye wonama; chifukwa sanakhulupirira umboni wa Mulungu wonena za mwana wake. Ndipo uwu ndi umboniwo, kuti Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa mwana wake. Iye wakukhala ndi mwana ali nawo moyo; wosakhala ndi mwana wa Mulungu alibe moyo. Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la mwana wa Mulungu. (1 Yohane 5:9-13)

Inde, mukhoza kudziwa. Mfumu simangokusungani mukulota.

Kodi mwatembenuka m'mbuyo pa chipembedzo cha munthu ndi kukhulupiririra umboni wa Mulungu? Ngati ziri choncho, ndiye kuti muzakhala kwa muyaya ndi Mfumu …

… kusangalala kwa muyaya

## Uthenga munkhani • 2

# Uthenga Woipa

Pamene tikuwerenga kumayambiriro kwa buku lake, Mfumu yakumwamba ndi dziko lapansi Inamulenga munthu muchifaniziro ndi kufanana kwake. Anapanga anthu chifukwa cha ulemerero wake. Anthu anakakhala chuma chake chapadera cha mtengo wapatali, abwenzi ake okondedwa, ndi nzika zoyera mu ufumu Wake owala. Koma poyamba payenera kukhala nthawi yoyesera.

AMBUYE Mulungu anamupatsa Adamu mayeso ochepa ndi zotsatira zazikulu. Mulungu anamuwuza kuti anali omasuka kudya zochokera mumitengo yonse ya m'munda kupatulapo mtengo umodzi. Kodi Mulungu ananena kuti chimuchitikire Adamu ndi chiyani akaphwanya lamulo limodzili?





Kodi Mulungu anamuwuza Adamu kuti ayambe kulakatula mapemphero, kusala kudya, ndi kuchita ntchito za bwino kuti afanane ndi machitidwe ake woyipa? Ayi! Mulungu anati: "Koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoyipa usadye umenewo; chifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu." (Genesis 2:17)

Tikudziwa chomwe chinachitika. Munthu anasankha kusamvera Mlengi-Mfumu yake. Adamu ndi Hava anachimwa. Koma kodi anagwa ndi kufa tsiku lomwelo? Ayi. Ndiye kodi Mulungu amatanthauza chiyani pamene ananena: "pamene udzadye umenewo udzafa ndithu"?



Kodi, malingana ndi malembo woyera, tanthauzo la imfa ndi chiyani?


Onani pa chithunzi. Kodi ndi chiyani chomwe chikuchitika ndi nthambi? Kodi chichitike ndi chiyani kunthambi ikathyoledwa ku mtengo? Kodi ikhala moyo? Kapena ifa?

Nthambi ikhoza kumaonekabe ngati ili moyo, koma ikhala kuti yafa chifukwa yalekanitsidwa ndi gwero lake la moyo.

Imfa imatanthauza kulekana. Iyi ndi nkhani yosakhala bwino.

Pamene Adamu ndi Hava anasankha kupita njira yawo m'malo mwa njira ya Mulungu anataya mgwirizano wawo ndi Mulungu, ngati nthambi yodulidwa pa mtengo. Ubale wawo ndi Mulungu unafa. Samafunanso kukhala naye. Anayesa kubisira. Adamu ndi Hava anafa mu uzimu.

Koma zoyipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu, ndipo machimo abisa nkhope yache kwa inu, kuti iye sakumva. (Yesaya 59:2)



Adamu ndi Hava anayambanso kufa kuthupi. Ngakhale kuti masamba apa nthambi yothyoka samauma nthawi yomweyo, chimodzimodzi matupi awo sanabwerere kufumbi tsiku lomwe anachimwa. Koma njira ya kukalamba inali itayamba. Imfa anali mdani amene sanakatha kumuthawa.

Pomwepo iye adzanena kwa iwo aku dzanja lamanzere, chokani kwa ine otemberereredwa inu, ku moto wanthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ache." (Mateyu 25:41)

Anthu ena amanyoza ganizo la gehena—Nyanja ya moto kumene mizimu yoonongeka ndi tchimo iyikidwe kwa muyaya. Koma kodi ndi koyenera kunyoza chomwe sitikumvetsetsa? Ngati anthu,



sitingamvetsere ganizo la muyaya. Ndi muyeso wa chinthu china.[8] Anthu amamunyozanso mneneri Nowa pamene amamanga chombo chake ndi kuwachenjeza za kusekufikira kwa madzi komwe kumabwera, koma pamene chitseko cha chombo chinatsekedwa ndi kusefukira kwa madzi kunabwera, anamvetsetsa chilungamo chomwe anachinyoza. Munjira yomweyo, nthawi yomweyo imene anthu adzalowe ku gehena, adzamvetsetsa chitsimikizo chake cha zifukwa zomveka.


Amene adzamva chilango, ndicho chionengeko chosatha chowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerero wa mphamvu yache. (2 Atesalonika 1:9)

Mfumu sidzalola tchimo kuipitsa dziko lake kwa muyaya.


Tchimo ndi mphamvu yowononga kwambiri ndi ngozi yofikira kutali kwa dziko lathu.

Tcimo ndi chobweretsa cha zoyipa zonse.

Ngati matenda opatsirana, tchimo la Adamu latigwira ife tonse.




Chimodzimodzi ngati nthambi ndi tsamba lililonse pa nthambi yothyoka ndi yakufa, ndiye aliyense wa ife ndi okhudzidwa ndi tchimo la Adamu. Tonse ndi ife mbali ya nthambi ya Adamu.




chifukwa chake, monga uchimu unalowa m'dziko la pansi mwa munthu modzi, ndi imfa mwa uchimo: chotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa. (Aroma 5:12)

Munthawi ya Mose, anthu anali ndi ganizo lolakwika lomwelo limene anthu ali nalo lero. Amayembekezera



kuti akapanga zambiri zabwino koposa zoyipa, Mulungu anakatha kuwaonetsa chifundo pa Tsiku la chiweruzo. Pokonza kuganiza kwawo kolakwika, Mulungu anabwera pansi pa Phiri la Sinai mwa moto waukulu ndi kuwapatsa anthu malamulo



khumi oti adzimvera. Aliyense amene sanasunge malamulo khumi onse moyenerera analamulidwa kukhala olakwa ndi kuyenera kufa.

Malamulo khumi ali ngati galasi. Ngati nkhope yanu yada, galasi limakuthandizani kuona pakudapo, koma silingachotse pakudapo.




Munjira yomweyo, malamulo sanaperekedwe kuti atipange ife oyenera ndi Mulungu. M'malo mwake, amationetsa ife kuti ndife olakwa ochimwa pamaso pa Mulungu woyera. Si ife okwanira kukhala mu ufumu wake olungama. Ndife ochimwa opanda thandizo amene tikufuna Mpulumutsi wabwino

Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu. (Aroma 3:23)

Uthenga woipa ndiyakuti sitimafika pa muyeso oyenera wabwino wa Mulungu. Uthenga wabwino ndiyakuti pali munthu m'modzi mu mbiri amane anazichita.

Dzina lake ndi Yesus.


# Uthenga munkhani • 3

## Uthenga wabwino

AMBUYE ndi wabwino kwambiri pa chilungamo ndi chifundo. Chilungamo chimatanthauza kuti chilango chokwanira cha malamulo cha chotsedwa pa tchimo langa. Chifundo chimatanthauza kuti chilango chalamulo sichinachotsedwe pa ine.

Kodi Mulungu angalange bwanji tchimo lathu popanda kulanga ife?


Yankho likupezeka mwa Ambuye Yesu Khristu, amene anabwera kuchipulumutso chathu.



Munthawi ya Chipangano cha kale, Yesu asanabwere, Mulungu anapanga lamamulo lopereka nsembe la tchimo kuti lipulumutse ochimwa ku lamulo la imfa. Mulungu anavomera mwazi wa zinyama zosalakwa ngati malipiro a tchimo. Umu ndi m'mene amalangira tchimo popanda kulanga ochimwa.


Koma kodi mwana wa nkhosa ndi malonda a chilungamo a munthu? Ayi. Mwazi wa chinyama ukhoza kungowonetsa zomwe chilungamo chimafuna.

Kodi ndi mtundu uti wamagazi umene ukhoza kuepereka ngongole ya tchimo la dziko lapansi? Ndi mwazi okhawo wa munthu olungama ndi okhala muyaya. Mlengi-wa dziko mwiniwake anakhala munthu.



"Pachiyambi panali mawu, ndipo mawu anali kwa Mulungu, ndipo mawu ndiye Mulungu… Ndipo mawu anasandulika thupi nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wache, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi." (Yohane 1:1,14)






M'mawa mwache anaona Yesu alinkudza kwa iye, nanena, onani mwana wankhosa wa Mulungu amene achotsa chimo lache ndi dziko lapansi!" (Yohane 1:29)






Mukumbukira Abele? Mulungu anaika machimo a Abele pa mwana wankhosa. Mwana wankhosa anali onyamala-tchimo la Abele mongoyembekezera. Yesu ndi onyamaula-tchimo lathu kwa muyaya. Mulungu anaika matchimo athu onse mwa iye.










Pamene Yesu tsono adalandira vinyo wosasayo anati, kwatha; ndipo anawerama mutu, napereka mzimu!" (Yohane 19:30)


Chilungamo ndi chosangalatsidwa.
Chifundo ndi chopezeka.




Umenenso mupulumutsidwa nawo ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikira kwa inu; ngati simunakhulupira chabe. Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, chimenenso ndinalandira, kuti Khristu anafera zoyipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu, monga mwa malembo..(1 Akorinto 15:2-4)

Ganizirani za Abrahamu ndi mwana wake. Kodi Mulungu anawatumiza ku phiri lakutali kukapereka nsembe chifukwa chiyani?





Mulungu amakonza malo amene Mwana wake anakapita kukafa chifukwa cha machimo a dziko lapansi.

Kodi ndi chifukwa chiyani Abrahamu analitcha Phiri kuti "AMBUYE apereka"? Chifukwa panali pa phiri pamene Mulungu anapereka nsembe yokwanira ndi yomaliza .

Kodi Mulungu anapereka chiyani kwa mwana wa Abrahamu? Nkhosa yaimuna. Kodi Mulungu wapereka chiyani kuti akupulumutseni inu kuchiwerezo? Yesu, Mwana wankhosa wa Mulungu.






Kodi mumaopa imfa ndi chiweruzo? Ngati muika chikhulupiriro chanu chonse mwa Yesu kukhala mpulumutsi wanu mukuyenera osaopa, chifukwa Mulungu walandira malipiro onse kuchokera kwa Iye amachimo anu ndi kumudzutsa Iye kubwerera kumoyo.

Tsopano ganizirani m'mbuyo za Adamu ndi Hava. Tchimo ndi manyazi awo zinawapangitsa iwo kuzibisa ndi masamba a nkhuyu ndipo amafuna kubisira kwa Mulungu. Mwachilungamo ndi chifundo chake, Mulungu anaika poyera tchimo lawo ndi kuwaveka mu zikopa za nyama zoperekedwa nsembe. Mwazi okhetsedwa wa nyama onawonetsa zomwe zinali zoyenera kubisa tchimo lawo, ndipo zikopa za nyama zinaonetsa zomwe zinali zoyenera kubisa manyazi awo.

Tonse timagawana tchimo ndi manyazi a mzimu wa makolo athu. Tonse timaperewera mukulungama kwa Mulungu. Tonse sitili ife oyenera kukhala naye. Nkhani yabwino ndiyakuti pamtanda Yesu Khristu anatenga tchimo ndi manyazi athu. Mumaola amdima amenewo, Anazindikira kulekena ndi Mulungu komwe ife tikuyenera. Ndipo keneko anafa. Koma popeza analimbe tchimo la iye mwini, manda sanakatha kumusunga iye.

Chifukwa cha imfa ndi kuuka kwa Yesu, Mulungu amapereka mwayi oyeretsa ndi kumveka inu: posinthanitsa machimo anu ndi chilungamo chaketo exchange.

> Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndizolungama zathu zonse ziri ngati zovala chovala chodetsedwa; ndipo ife tonse tifota ngati tsamba, ndi zoyipa zathu zitiuluza monga mphepo. (Yesaya 64:6)




> Ndidzakondwa kwambiri mwa Yehova, moyo wanga udakondwerera mwa Mulungu wanga; pakuti iye wandiveka ine ndi zovala za chipuumutso, nandifunda chofunda cha chilungamo, monga mkwati avala nduwira, ndi monga mkwatibwi adzikometsa yekha ndi miyala ya mtengo. (Yesaya 61:10)

> Ameneyo sanadziwa uchimo anamyesera uchimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa iye. (2 Akorinto 5:21)

Patsiku la chiwerezo, kodi mudzaima pamaso pa Mulungu munsanza zanu za kulimbikira mu chipembedzo?


Kapena mudzaima mumwinjiro mu chilungamo choyera cha Khristu?

UTHENGA MUNKHANI • 4

## YANKHO LANU KWA MFUMU

Taziyerekezeni nokha mukuyenda mukhalango yayokha. Kodi mungakonde kukumana ndi chiyani—mwana wankhosa kapena mkango?





Pakubwera kwake koyamba, Mfumu ya ulemerero imatchedwaMwana wa nkhosa. Inabwera modzichepetsa kudzapulumutsa ochimwa. Mfumu ikadzabweranso, idzatchedwaMkango. Idzabwera mwa ulemerero kudzaweruza ochimwa osatembenuka mtima.

Kodi Yesu akadzabweranso, mudzasangalala pamaso pa Mpulumutsi-Mfumu kapena mudzanjenjemera pamaso pa Oweruza-Mfumu? Zonse zikutengera pa yankho lanu ku uthenga wa Mulungu.

Pamene Yesu anayamba kuyenda ndi kuphunzitsa, ena mwa mawu ake oyambirira anali,

> "nanena nthawi yakwanira, ndipo ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino!" (Marko 1:15)

"Kutembenuka mtima" kumatanthauzakusintha maganizo anu okhudzana ndi zimene mukukhulupirira zoyenera kuti mukhale mu ufumu wa Mulungu. Kumatanthauza kusiya kukhulupirira njira yanu ndi kuyamba kukhulupirira ndi kutsatira njira ya Mulungu.

"Kukhulupirira uthenga wabwino" kumatanthauza kuika chikhulupiriro chanu mwa Mpulumutsiamene anafa chifukwa cha machimo athu ndi kuukanso kukupatsani inu moyo watsopano. Koma kodi zimatanthauza chiyani kuika chikhulupiriro chako mwa wina wake?

Ndipereke chitsanzo chofanana ndi nkhani yatsopano yakuzambwe kwa Africa. Ikukamba za akazi awiri, Fatu ndi Bintu.

Onse anali ndi matenda opatsirana m'maso awo. Fatu anapita ku chipatala. Dokotala anamupatsa mankhwala othira m'maso. Maso ake anachira. Bintu anapita kwa asing'anga. Anapaka "mankwala  ake" m'maso mwa mkaziyo. Maso ake anasanduka oyera ndikukhala osawona.

Fatu ndi Bintu onse anali ndi chikhulupiriro. Akazi onse anachitapo kathu pa chikhulupiriro chawo popita kwa ochiritsa amene amamukhulupirira—koma zotsatira zinali zosiyana.

Kukamba za moyo wosatha, aliyense amakhulupirira mwa china chake kapena mwa wina wake.

Ambiri amaika chiyembekezo chawo pa chipembedzo cha makolo awo. Ena amavomerezana ndi amene amanena kuti moyo umathera ku manda. Ena amabwera ndi maganizo awo okhudzana ndi moyo, imfa, ndi nthawi yosatha. Pamapeto pake, funso lokha ndi lomwe lidzafunikire: Kodi munasankha chilungamo?


> "Ine ndapanga chisankho, ndikhulupirira Mfumu, amene anati: yense wakukhala mwa choonadi amva mawu anga" (Yohane 18:37)

> "Iye ndi amene anandikonda ine napereka moyo Wake chifukwa cha ine." (Galatians 2:20)

Si mfumu chabe. Ndi Mfumu yanga!



Munthu woyambirira anapangidwa kuti awunikire fanizo la Mulungu. Fanizo limenelo linaonongedwa ndi tchimo. Yesu Khristu, “amene ali fanizo la Mulungu wosaonekayo, wobadwa woyamba wa chilengedwe chonse” (Akolose 1:15), anabwera kudzakupatsani inu moyo watsopano ndi kubwezeretsa fanizo la Mulungu mwa inu.



Ngati mwaika chikhulupiriro chanu mwa Yesu Khristu, ndiye kuti, pamaso pa Mulungu, simulinso mwa Adamu. Muli mwa Khristu. Ndinu nzika yokonderedwa ya kumwamba ndi mwana wokondedwa wa Mulungu. Ndinu chuma cha mwini wake Mulungu, chomwe anachiombola ndi mwazi wa mwana wake.

Ngati membala wobadwa mwatsopano mu banja la Mulungu mukhoza tsopano kumuitana Mulungu Atate.

Koma ndi mwayi opambana kumabwera udindo opambana.

> Monga ana omvera osadzifanizitsanso ndi zilakolako zakale, pokhala osadziwa inu; komatu monga iye wakuitana inu ali woyera mtima, khalani inunso oyera mtima m'makhalidwe anu onse. (1 Peter 1:14-15)

Ngati otsatira wa Khristu, mukuyenera kukhululuka, kukonda, ndi kupempherera anthu onse, ngakhalenso adani anu. Yesu akunena:

> “Mwa ichi adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondano wina ndi mnzache.” (Yohane 13:35)

Pamene mukudzipereka kwa Iye, Mzimu wa Ambuye Yesu, amene anabwera mu mtima mwanu pamene munakhulupirira uthenga wabwino, ukuthandizani inu kulipambana tchimo ndi kuunikira khalidwe lake loyera. .

> Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima chikhulupiriro, chifatso, chiletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Galatians 5:22-23)


Ngati mwana wa Mfumu, muli ndi cholinga chatsopano m'moyo: kumulemekeza Iye.

> Ndinu nthumwi Yake ku dziko lotaika. Muimirireni bwino. Tsiku lina mudzamuona maso ndi maso, ndipo kenaka “okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu ndipo sichioneka chimene tidzakhala. Tidziwa kuti, pa kuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, pakuti tidzamuona Iye monga ali.” (1 Yohane 3:2) Mpakana,

muyankhule Naye nthawi ina iliyonse. Mutamandeni mu nyengo iliyonse. Mulambireni ndi kumutumikira ndi ena amene amamukonda Iye ndi mawu Ake. Werengani malembo oyera tsiku ndi tsiku.

(muyambe ndi Luka, Yohane, Machitidwe atumwi, ndi Aroma.) Mzimu Woyera ndi mphunzitsi wanu.

Baibulo ndi chakudya chanu cha uzimu ndi chida pa Satana, ndani samafuna kuti inu muziganiza, kuyankhula, ndi kuchita ngati Yesu. Mukalingalira kwambiri za malembo oyera mukhalanso amphamvu kwambiri mu uzimu.



Ndimakonda mawu awa ochokera ku Masalmo:

> Monga nswala ipuma wefuwefu kukhumba mitsinje; motero moyo wanga upuma wefuwefu kukhumba inu, Mulungu. (Masalmo 42:1)

Kodi mukhoza kunena kuti?

Chisankho ndi chanu.

*Paul D. Bramsen*
resources@rockintl.org

# Zowonjezera

Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu; chiri mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense. Pakuti ife ndife chipangano chache, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo.

Popeza tsopano tayesedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khristu; amene ife tikhoza kulowa Naye ndi chikhulupiriro m'chisomo ichi m'mene tirikuimamo, ndipo tikondwera m'chiyembekezo cha ulemerero wa Mulungu.

— Kuchokera ku Chipangano Chatsopano
(Aefeso 2:8-10; Aroma 5:1-2)

## Mafunso • Gawo 1 • Chipangano Chakale

Mndandanda uwu ukupereka funso limodzi kapena awiri pa magawo 70 a sewero. Mayankho amafunsowa alumikizika ku ndime ya gawo lasewero limene liri pafupi ndi sewero lina. Khalani omasuka kutenga izi ndikukagwiritsa ntchito mmagulu okambirana za mawu. Mukafuna zambiri pitani ku: **www.one-god-one-message.com**

*Gawo la sewero • Mafunso*

1 • Mfumu ya ulemerero inakatha kutenga zaka mazana ochuluka kuti Ipange madongosolo ake. Kodi izi zikukuwuzani chiyani zokhudzana ndi Mfumu?

2 • Tchulani magawo ofunikira awiri a Baibulo. Kodi amasiyana bwanji?

3 • Kodi mumakhulupirira mawu oyambirira a malembo oyera (Genesis 1:1)? Kodi Chifukwa chiyani kapena sichifukwa chiyani?

4 • Ngakhale pamene Mulungu yekha analipo, sanali yekha. Kodi mukumvezetsatsapo chiyani pa ndemanga imeneyi?

5 • Kodi tingaphunzirepo chiyani kwa Mulungu pa zinthu zomwe wapanga?

6 • Tchulani zina zomwe Mulungu anapanga mwa anthu zosiyana ndi nyama.

7 • Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu sanamufunse Adamu ngati amafuna kukhala mu Edeni?

8 • Kodi tchimo ndi chiyani? Kodi Mulungu ananena kuti chingachitike ndi chiyani ngati Adamu samvera lamulo la Mulungu? Kodi liwu lina a imfa ndi chiyani?

9 • Ngati Adamu ndi Hava analengedwa muchifanizo cha Mulungu.

Kodi izi zikutanthauza chiyani?

10 • Kodi chochititsa chidwi chabwino kumwamba ndi chiyani?

11 • Kodi tchimo linalowa bwanji mudziko?

12 • Kodi AMBUYE anati chinakachitika ndi chiyani ngati munthu anakadya chipatso cha mtengo odziwitsa zabwino ndi zoyipa? Kodi Satana anati chinakachitika ndi chiyani?

13 • Kodi tchimo linalowa bwanji m’banja la munthu?

14 • Kodi chotsatira choyambirira cha tchimo chinali chiyani? Kodi ndi munjira iti imene tchimo la Adamu ndi Hava linabwezeretsa ulemu wawo ndi manyazi?

15 • Kodi ndi munjira iti imene Adamu ndi Hava anafa tsiku lomwero limene anachimwa? Kodi anali ngati nthambi yothyoka bwanji? (onaninso patsamba 160.)

16 • Tchulani njira zina za themberero la tchimo zimene zaononga chilengedwe chenicheni.

17 • Mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani dongosolo la chinsinsi cha Mulungu likuphatikiza Mpulumutsi amene anakakhala mwana wa mzimayi (kukhala ndi mayi wakuthupi, koma osakhala ndi bambo wakuthupi)?

18 • Kodi Mulungu anapanga chiyani kuti aphimbe tchimo ndi manyazi a Adamu ndi Hava? Kodi Mulungu anawaonetsa bwanji kuti iye ndi Mulungu wachilungamo, chifundo, ndi chisomo?

19 • Kodi Mulungu anamuchotsa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni chifukwa chiyani?

20 • Kodi tchimo la Adamu ndi Hava linakhudza bwanji ana awo? Kodi limakhudza ife bwanji ndi mabanja athu? (Onaninsoni patsamba 161.)

21 • Kodi ndi mtundu wanji wankhosa umene Mulungu anakavomera kufa m'malo mwa ochimwa?

22 • Kodi dipo limatanthuza chiyani? Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu amafuna malipiro a imfa?

23 • Kodi Mulungu anapanga chiyani ndi tchimo la Abele? Kodi chinavuta ndi chiyani ndi chopereka cha Kaini?

24 • Kodi kutembenuka mtima kumatanthauza chiyani? Kodi Mulungu amafuna Kaini kuti achite chiyani?

Kodi Kaini anachita chiyani?

25 • Kodi kusefukira kwa madzi padziko lonse lapansi munthawi ya Nowa kumatiphunzitsa ife bwanji zakuleza mtima ndi chigamulo cha Mulungu?

26 • Kodi ndi chithu choyambirira chiti chomwe Nowa ndi banja lake anachita atatuluka mungalawa?

27 • Kodi ndi munjira iti imene Babele akuonetsa chipembedzo chabodza?

28 • Kodi ndi malonjezo akulu awiri ati amene AMBUYE anapanga kwa Abrahamu, ngati anakakhulupirira ndi kutsatira AMBUYE?

29 • Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anakhululukira Abrahamu ndi Sara machimo awo ndi kuwalamula kukhala olungama?

30 • Kodi ndi funso lanji limene mwana wa Abrahamu anafunsa bambo ake pamene amapita ku phiri lokapereka nsembe?

31 • Mulungu anali atalonjeza kumupanga Isaki kukhala tate wa fuko latsopano. Popeza Abrahamu amadziwa kuti Mulungu sanganame, kodi Abrahamu anaganiza kuti Mulungu anakapanga chiyani akamaliza kupereka Isaki ngati nsembe pa guwa?

32 • Kodi ndi chifukwa chiyani Abrahamu analitchula phiri kuti AMBUYE apereka? Kodi mwana wankhosa anafa m'malo mwa mwana wa Abrahamu tsiku limenelo?

33 • Kodi AMBUYE anakwanilitsa bwanji malonjezano awo akulu awiri amene anali atamupangira Abrahamu?

34 • Tikayesetsa kwambiri kumvera malamulo a Mulungu, kodi tikhoza kukhala abwino kwambiri woyenera kukhala ndi Mulungu kumwamba? Kodi malamulo khumi amakhala bwanji ngati galasi? Kodi ndi munjira iti imene malamulo amationetsa ife kuti tikufuna Mpulumutsi?

35 • Kodi ndi chifukwa chiyani kupereka nsembe kwa nyama sikumachotsa ngongole ya tchimo la dziko lapansi?

36 • Sankhani uneneri umodzi pa zolembapo ndi kunena m'mene ukulozera kwa mpulumutsi akubwerayo.

# MAFUNSO • GAWO 2 • CHIPANGANO CHATSOPANO

37 • Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anagwiritsa ntchito anthu anayi m'malo mwa munthu m'modzi kuti alembe nkhani ya uthenga wabwino wa Yesu?

38 • Kodi ndi chifukwa chiyani mngelo Gabriel amamutchula Yesu Mwana wa Mulungu?

39 • Kodi dzina loti Yesu limatanthauza chiyani?

40 • Kodi mumakonda Chiyani kwambiri pa nkhani ya kubadwa kwa Yesu?

41 • Mngelo anawauza abusa ang'ombe, "Mpulumutsi wakubadwirani; ndi Khristu Ambuye." Kodi abusa ango'mbe anali osangalala kumva nkhaniyi chifukwa chiyani?

42 • Kodi zinali zoyenera kwa anzeru aku m'mawa kumulambira mwana Yesu? Chifukwa chiyani kapena sichifukwa chiyani?

43 • Kodi ndi munjira iti imene Yesu anali osiyana ndi ana ena?

44 • Kodi uthenga wa mneneri Yohane unali osiyana bwanji ndi uthenga wa aneneri onse ambuyomu? Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani Yohane analozera kwa Yesu ndi kunena: "wonani, Mwana wa nkhosa wa Mulungu, amene amachotsa tchimo la dziko lapansi"?

45 • Wonaninso gawo la sewero ili ndi kunena china chake chomwe mukudziwa chochokera mu Baibulo chokamba za mzimu wa Mulungu, Mwana wa Mulungu, ndi Atate wakumwamba.

46 • Kodi ndi chifukwa chiyani Satana amkafuna kumuchimwitsa Yesu?

47 •Yesu atamaliza kuwerenga zolemba za mneneri Yesaya, anati: "Lero malembo oyerawa akwaniritsidwa mukumva kwanu!" Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani izi zinawapangitsa anasi ake kukwiya?

48 • Kodi Yesu anali chida cha Mulungu chotani pa dziko lapansi?

Kodi ndi chifukwa chiyani ziwanda zimaopa Yesu?

49 • Yesu atamaliza kulamula mphepo ya mkutho, "Chete! Khala bata!" ophunzira anati: "Kodi munthu ameneyu ndi ndani? Ngakhale kuti mphepo ndi mafunde zikumumvera Iye!" Kodi mukuganiza kuti Yesu ndi ndani?

50 • Kodi ndi chifukwa chiyani atsogoleri azipembedzo anamunamizira Yesu zonyoza Mulungu?

51 • Yesu anati: "Ndine kuuka ndi moyo. Amene akhulupirira mwa Ine adzakhala ndi moyo, ngakhale kuti atamwalira." Kodi timadziwa bwanji kuti anayankhula zoona?

52 • Kodi Yesu ananena chiyani kwa anthu amene anabweranso tsiku lotsatira kudzayang'ana chakudya china?

53 • Wonaninso gawo la sewero ili ndi kunena chithu chimodzi chimene Yesu ananena chimene chinakudabwitsani.

54 • Aneneri anamutcha Mesiya "dzuwa la chilungamo. "Yesu mwini anadzitcha Mwini wake "kuwala kwa dziko lapansi." Kodi Yesu Mesiya ndi osiyana bwanji ndi aneneri?

55 • Kodi ophunzira amaganiza kuti Mesiya apange chiyani?

Kodi Mesiya anabwera kuzapanga chiyani?

56 • Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anakwera bulu wonyozeka kwambiri m'malo mwa kavalo –wankhondo opambana?

57 • Kodi chifukwa chiyani atsogoleri azipembezo sanamupusitse Yesu kunena china chake cholakwika?

58 • Kodi chifukwa chiyani m'busa wamkulu ndi olamulira AchiYuda ananena kuti Yesu aphedwe?

59 • Kodi ndi chifukwa chiyani Pilato anasutsa kuti Yesu aphedwe?

60 • Asilikali anasindikizira chisoti chaminga m'mutu mwa Yesu.

Kodi minga zimatikumbutsa chiyani?

61 • Kodi mauneneri a Abrahamu anakwaniritsidwa bwanji ndi Yesu?

Kodi ndinu oyenera bwanji kwa Mulungu?

62 • Mbava ziwiri zinapachikidwa pa mtanda pafupi ndi Yesu. Lerolino imodzi ili ku gehena (kusiyana ndi Ambuye kwa muyaya) ndipo imodzi ili kumwamba (kwamuyaya ndi Ambuye) Kodi ndi chiyani chimene chinapangitsa kusiyana?

63 • Pamene Ambuye Yesu anali pamtanda mu mdima,

Kodi Atate kumwamba anaika Chiyani pa Iye?

Kodi Yesu anati chiyani, "kwatha"?

Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anang'amba chinsalu cha mukachisi?

64 • Kodi ophunzira amakumbukira za lonjezo kuti adzaukanso?

Kodi atsogoleri azipembedzo oyipa anakumbukira za lonjezo lake?

65 • Kodi azimayi anapeza chiyani pamene anapita kumanda m'mamawa wa tsiku la Mulungu? Kodi atsogoleri azipembedzo anapanga chiyani ndi manda opanda kathu? Ngati ndimakhulupirira kwanthunthu mwa Yesu Mwana wa nkhosa wa Mulungu amene anafa chifukwa cha machimo anga ndi kuukanso, kodi sindikuyenera kuopa imfa chifukwa chiyani?

66 • Kodi ndi chifukwa chiyani Ambuye Yesu anawauza awiri apaulendo pa nsewu opita ku Emmaus kuti anali opusa?

67 • Pamene Mpulumutsi wa kuuka kwa akufa anaonekera mu chipinda, Tomasi anati kwa Iye,

"Ambuye wanga ndi Mulungu wanga!" Kodi Tomasi anakhoza kapena analakwitsa kumuitana Yesu Ambuye wake ndi Mulungu wake? Chifukwa chiyani?

68 • Kodi Yesu anawauza ophunzira ake kuti apange chiyani Iye akabwerera kumwamba?

69 • Kodi Mfumu ya ulemerero ndi ndani? Kodi mumaganiza chiyani za Iye?

70 • Kodi Mfumu ikadzabweranso, mudzakhala osangalala kapena amantha? Chifukwa chiyani?

## Zolemba zomaliza

**Gawo la sewero:** [1]*Buku la 'Alice in Wonderland'* linatanthauzilidwa mu zinenero pafupifupi 200, Koma Buku Lopatulika linatanthauziridwa mu zinenero zopitirira 2,500.

[2]Baibulo limatsimikizidwa ndi akatswiri a zakafukufuku, komanso mbiri ya dziko, kukwanilitsidwa kwa uneneri komanso kufanana kwa nkhani zolembedwe motsatirana kwa zaka zambiri zapitazo.

**Gawo la sewero 2:** [3]Mfumu siyolenga ndi kusamalira dziko kokha, komanso ndi Mlembi ndi Woteteza wa Buku lake. Zolembedwa zopezeka m'nyanja ya mchere zimatsimikiza kuti Malembo a Chipangano chakale a nthawi ino ndi chimodzimodzi ndi amene amapezeka Yesu asanafike. Malembo Chipangano Chatsopano amavomerezedwa ndi zolembedwa zochuluka za nthawi ya kale, zambirir za mmasiku oyambirira Yesu atabwera. Mphekesera yodziwiwka kwambiri yakuti malembo Oyamba anaonongedwa ndi kuchitidwa chinyengo ndi anthu ambiri zilibe umboni wotsimikizira. Onani *One God One Message*, chapter 3. www.one-god-one-message.com

**Gawo la sewero 5:** [4]FKuti mumvetse bwino za makhalidwe a Mulungu monga zimaonekera mu masiku asanu ndi limodzi ndi limodzi akulenga. Onani *One God One Message*, chapter 8.

**Gawo la sewero 6:** [5]SPopeza Mulungu ndi mmodzi, Ndichifukwa chifukwa chiyani amanena kuti "Tiyeni Tipange munthu mu Chifanizo chathu…."? Yankho lake lalumikizika ku umodzi wa Mulungu. Mu mawu a Mulungu, Dzina la Mulungu mu chi Heberi limatanthauza kuti Elohim lomwe ndi dzina lamagawo angapo. Liwu lakuti Mulungu ndi mmodzi ndi Echad kuwonetsera umodzi wa Mulungu. Mu Muyaya Mulungu asanalenge Angelo ndi Anthu Mulungu anakondwera mwa Iye yekha pamodzi ndi Mawu ake / Mwana ndi Mzimu Woyera. "Taonani Mulungu ndiye Wamkuru ndipo sitimdziwa, chiwerengo cha zaka zake nchosasanthulika!" (Mneneri Yobu 36:26)

**Gawo la sewero 7:** [6]Dothi lomwelo limene linalengedwera Munthu lomwelonso ndi Pfumbi komanso nthaka ya dziko. Zinthu izi sizinavomerezedwe ndi nzeru zapansi pano mpaka lero lino. Pamene ambiri mwa akatswiri a za maphunziro amatsatira zinthu pofufuza ndi kuyesera (Nzeru za Munthu), Kudziwa kwa iwo amene amakhulupirira Baibulo kumachokera pa chidziwitso ndi bvumbulutso. (Mawu a Mulungu)

**Gawo la sewero 11:** [7]Kuti mudziwe zambiri za chiyambi cha Satana onani *One God One Message*, chapter 11.

**Gawo la sewero 16:** [8]Ngati Nyanja ya Moto ndi malo a chilango chosatha, ziwoneka zopanda chilungamo ku mitima yathu, Ndiye kuti sitinamvetse za chiyero cha Mulungu, Umuyaya wa Munthu, mphamvu ya tchimo ndi chithunzithunzi cha moyo wosatha. Mawu akuti Muyaya amapitirira kumvetsetsa kwathu, popeza kuti umboni wa kumvetsetsa kwathu ndi nthawi. Moyo Wosatha ulibe nthawi ya malire. Mulungu amaene analenga nthawi salamulilidwa ndi nthawi. (2 Peter 3:8-9) Moyo wa Muyaya siuli mu Zaka. Ganizira kuti tsopano ndi Muyaya. Nthawi imene ochimwa alowa mu malo osathawika, adzamvetsetsa dongosolo lake loyenera.

**Gawo la sewero 17:** [9]Kuombora (kapena kupulumutsa) kumatanthauza kuti kugulanso chinthu popereka mtengo wake wofunikira. Mu Ndime 18 ya One God One Message wolemba anawonetsera izi ndi nkhani yochokera mu ubwana wake: Ngati mwana wokulira ku Califonia, ndinali ndi Galu wa mng`ono. Ndimamudyetsa kumusamalira komanso kusewera naye. Amanditsatira ndi kundisangalalira pobwerera ku Sukulu. Koma anali ndi Bvuto. Nthawi zina amayendayenda mmudzi woyandikana nawo, ngakhale amabwerera kufikira tsiku lina. Nditabwera kuchokera ku Sukulu Galu wanga panalibe kuti andilandire ine. Nthawi yokagona sanawonekenso. Tsiku lotsatira Bambo anga anandiuza kuti ndiyimbe lamya kwa Oyang`anira Ziweto a Mdera lathu. Amene amasunga a Pusi, Agalu ndi ziweto zina zimene zasowa kwa kanthawi. Ziweto zimene eni ake sanalondole amazipha.

Ndinayimba kwa adindowo. Ndipo anali ndi Galu wamng`ono amene ndinkamufunafuna. Amene amasunga a Galu anampeza Galu wangayu. Galu wanga analephera kudzipulumutsa yekha, Pakanapanda wina wompulumutsa akanaphedwa. Ndinapita kumsasa kokatenga Galu koma ndisanamunyamule Adindo anandiuza kuti ndilipire chindapusa ndisanamutenge. Zinali zosephana ndi malamulo kuti Galu aziyenda yekha panseu.

Ndidalipira Mtengo wa ndalama ndipo anandipatsa Galu wanga. Iye anali wokondwa kutulutsidwa mu khola losasangalatsa ndikukhala mmanja mwa amene amamusamalira iye. Anawomboledwa.

Zimene zinandichitikira mu ubwana wanga powombola galu zikupereka chithunzi thunzi cha nyengo yomwe tili. Monga oukira, ochimwa oweluzidwa, tilibe njira yodzipulumutsira ku chilango cha uchimo, komanso chilamuro cha tchimo ndi imfa.

Tikusowekera Mpulumutsi Yemwe akhoza kutipelekera dipo lotiombola.

**Gawo la sewero 23:** [10]It 10Ndizotheka Mulungu kubvomeleza nsembe ya Abeli ngati mmene anachitira ndi Mneneri Mose, Solomo di Eliya: "Moto wochokera pamaso pa Mulungu unayaka ndi kunyeketsa Nsembe zonyeketsa ndi mafuta pa Guwa." (Levitiko 9:24; 2 Mbiri 7:1; 1 Mafumu 18:38)

**Gawo la sewero 30 & 61:** [11]Mawu akuti Moriah amatanthauza kuti Wosankhidwa wa Mulungu. Ndi dera limene Yerusalemu anamangidwa. Lero Phiri la Moria ndi malo amene padamangidwa Kachisi wa Solomo kale. (2 Mbiri 3:1) Pafupi ndi phirili pali malo otchedwa bade." (Luka 23:33)

**Gawo la sewero 36:** [12]FKukwaniritsidwa kwa Uneneri kumapangitsa Baibulo kukhala Buku lopatulika kuposa mabuku onse pa dziko lapansi. Kulosera kwa Aneneri pa za Mtsogolo, kutsatirana ndi kukwaniritsidwa kwake mu Mbiri, ndi njira imodzi imene Mulungu wabvomelezera uthenga wake. Mulungu yekha angathe kudziwitsa mapeto ake a zinthu pachiyambi kuchokera nthawi za kale ndi chimene chikubwera. (Yesaya 46:10) Yesu Mesiya anati: "Ndikuuzani tsopano zisanachitike, kuti zikadzachitika mudzakhulupirire kuti INE ndine IYE." (Yohane 13:19) See *One God One Message*, chapter 5.

**Gawo la sewero 41:** [13]Khristu ndi dzina lachi Helene lochokera mu chi Heberi lakuti Mesiya kutanthauza kuti Wosankhidwa.

[14]Masiku a zochitika mu mbiri amatsatiridwa molingana ndi chaka chimene Yesu Christu anabadwa. For example, the prophet Abraham was born around 2000 BC Mwachitsanzo Mneneri Abraham anabadwa mu nyengo ya (Zaka2,000 Yesu asanabadwe) Buku ili (Mfumu ya Ulemelero) Linalembedwa mu chaka cha AD 2011 (kupitirira zaka 2,000 Yesu atabadwa) AD amaimira -Anno Domini, mawu amu latini kutathauzira kuti mu chaka cha Ambuye wathu. Anthu ambiri lero amagwiritsa BCE (Before Common Era) and CE (Common Era) Pongofuna kuchotsa Yesu mu mbiri, koma umboni wa kugawika kwa mbiri umatsimikizika ndi kubadwa kwa Yesu.

**Gawo la sewero 43:** [15]"'Kodi uyu si mpala matabwa? Uyu si mwana wa Mariya komanso m'bale wa Yakobo, Yosefe, Yudasi ndi Simon? Kodi alongo ake sitili nawo pano?' Ndipo anamupaka mulandu Iye." (Mariko 6:3) Pokhala Yosefe sanali bambo womubereka Yesu, Iye' analumukizana ndi achimwene ake komanso achemwali ake kuchokera ku banja la mayi ake. Yesu anali mwana wa Mulungu komanso munthu. Onanai zolemba zomalizila 19 (Gawo la sewero 52)

**Gawo la seweros 43 & 58:** [16]Mu chaka chilichonse pa mphwando la pasaka, a Yuda amakumbukira zomwe zinachitika mu thawi ya Mose pomwe iwo anali mu ukapolo ku Egipito. Makolo awo anapha ana a khosa ndikupaka magazi ake pa zitseko monga ananenera Mulungu, "Ndikadzaona magazi, ndidzapitirira inu" (Eksodo 12:13) Pakati pa usiku Mulungu anapha mwana wa mwamuna oyamba wa m'nyumba iliyonse yomwe inalibe magazi a mwana wa nkhosa pa khomo. Mulungu anagwiritsa tchito njira iyi populumutsa anthu ake omwe anali akapolo kwa zaka 400.

## Zolemba zomaliza

**Gawo la sewero 45:** [17]Tingamvetse bwino za utatu wa Mulungu pa ife tokha. Chodziwikiratu ndi chakuti Iye ndi Mulungu Dziko lathu la dzala ndi zithu mu magawo atatu: Nthawi: Imafotokozeredwa kale, tsopano, ndi mtsogolo. Mulengalenga: Kutalika, kuchepa, kuya. Munthu: mzimu, moyo, thupi. Dzuwa limakhalanso ndi magawo atatu. Timatchula dzuwa lowooneka, kuwala kwake dzuwa, kutetha kwake dzuwa, koma dzuwa ndi limodzi Chimodzimodzi ndi Ambuye amene ali mwana wosatha, Mzimu Woyera wosatha ndi Atatenso wosatha. Monga kuwala ndi kutetha kuchokera ku dzuwa, chonchonso mwana(Mawu) a Mulungu ndi Mzimu wa Mulungu achokera kwa Mulungu", Mulungu ndi M'modzi (Deuteronomy 6:4) Onaninso Gawo 4 ndi zolemba zomaliza 5 (Gawo 6) For more on God's complex unity and Jesus' human and divine nature Kuti mudziwe zambiri za umodzi wa Mulungu komanso ummunthu wa Yesu ndi u'Mulungu wake, Werengani 'One God One Message', ndime 9 ndi 17. Werengani Uthenga wa Yohane.

**Gawo la sewero 47:** [18]Mesiya amatanthauza wosakhidwa kapena odzodzedwa. Kalekale ku mvuma, pamene mfumu yatsopano imavekedwa ufumu, Wansembe kapena mneneri amadzodza mafuta pa mutu pa mfumu kusonyeza kuti tsogoleri wa tsopano mu dziko. Yesu sanadzozedwe ndi munthu koma Mzimu Woyera (Onani Gawo la sewero 45)

**Gawo la sewero 52:** [19]Yesu kawirikawiri amazitchula kuti mwana wa munthu 19. Iye adali mwana wa Mulungu nthawi zonse, koma anakhala mwana wa munthu. Monga mwana wa Mulungu Iye ndi mawu amene anali pa chiyambi ndi Mulungu (Yohane 1:2; Genesis 1:3), koma ngati mwana wa munthu Iye ndi mawu amene anasandulika thupi, osakhidwa ndi Mulungu kudzakhala Mpulumutsi-Oweluza-Mfumu ya dziko lonse (Yohane 1:14; Daniel 7:13-14)

**Gawo la sewero 56:** [20]Afarisi anali gulu la achipembedzo cha chiYuda. Ena a iwo amapephera kasanu ndi kamodzi patsiku, kusala kudya miyezi itatu pa chaka, komanso kupereka chakhumi cha chuma chawo kwa a umphawi (Luka 18:9-14) Koma izi zinali mwambo chabe. Anali achipembedzo koma osadziwa ndi kukonda Mulungu.


**Gawo la sewero 68:** [21]Kwa okhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu, ubatizo umangokhala umboni wotsimikizira chisakho chawo chomutsatira Iye. Kumizidwa mu madzi sikuchotsa machimo. IZi zimatsimikizira kuti munthu akuvomereza kufa, komanso kuuka pamodzi ndi Yesu. Ubatizo wa m'madzi umaimilira kusiya moyo wakale ndi kuyamba moyo watsopano.

[22]Patangotha masiku ochepa mwana wa Mulungu atapita ku mwamba, the Mzimu wa Mulungu unapatsidwa kukhala mu mtima mwa bambo aliyense, mzimayi, komanso mwana okhulupirira Uthenga Wabwino. Buku la Machitidwe mu chipangano chatsopano limaonetsera khani yosangalatsa ya momwe Mzimu Woyera anawapatsira mphamvu ophunzira kuti aonetsere chikhalidwe cha Yesu komanso kufalitsa uthenga ku dziko lonse. Njira ya chipulumutso cha Mulungu sinasithe. Ngati ungapange chisakho chokhulupira uthenga Wake— kuti ndiwe ochimwa olekanitsidwa ndi Mulungu, osakwanitsa kuzipulumutsa Yekha kuchilango cha tchimo, ndikuti Yesu Khristu anatenga chilango chako pa mtanda, ndikuikidwa m'manda, ndikuuka kwa akufa—Kenako nanunso mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Izi zikutathauza kuti Mfumu ya dziko lonse idzabwera yokha ndikukhala mu mtima mwanu.. Adzakhala Mbuye wanu, tate, komanso bwenzi. Malemba ak, munasindikizidwa ndi chizindikiro ndi Mzimu Woyera wa lonjezano, Ndiye chikole cha cholowa chathu, kuti ake ake akawomboledwe, ndikuti ulemelero wake uyamikike, Mwa Iyeyo inunso, mutamva mawu a coonadi, uthenga wabwino wa chipulumutso chanu, ndikukhulupirira Iye. Ziposa kuganiza chabe kuti ife timulemekeze Mulungu wathu wa ulemelero" (Aefeso1:13-14) Mulungu ndi wamkulu, Mfumu yodabwitsa ndipo Iye adzakhala ndipo adzakhala ndi banja la likulu, lodabwitsa kwa thawi yosatha. Kodi mudzakhalako?

# Mabuku ena a Mthenga Wabwino

Mthenga Wabwino ndi okondwa kwambiri kukupatsirani inu mabuku ena. Mu zaka zapitazi takonza ndi kumasulira mabuku mu zilankhulo za ku Malawi:

Buku loyamba limene tikulimbikitsa kuti muwerenge ndi ***"Thandizani Asilamu".***




Zaka zapitazo tinagawa mabuku okwanira 10,000 ku Malawi.

Buku ili likupezekanso muchilankhulo cha chiTumbuka.

Buku lina lomwe tikulimbikitsa kuti muwerenge ndi *"Kufalitsa Uthenga Wabwino."*




**Mabuku ena omwe akonzedwa ndi Mthenga Wabwino mu chiChewa ndi:**

- *Uthenga wa Nabi Isa - ndi Gerhard Nehls*
- *Kufikira aSilamu ndi Uthenga Wabwino wa Chipulumutso - ndi Steven Paas*
- *Zikhulupiriro ndi zichitochito za aKhristu - ndi William McElwee Miller*
- *Ndinalimba Mtima kumutchula iye Atate - ndi Bilquish Sheikh & Richard Schneider*
- *Chophimba chong'ambika - ndi Gulshan Esther*

**Mu chiYao tili ndi mabuku awa:**

- *Kwanga kwakulupichika*
- *Mwenye jwa Lumbili - ndi Paul D. Bramsen*
  *(Kanema opangidwa kuchokera ku buku ili muthakumupeza pa www.rockintl.org)*

Mabuku onsewa atithandiza kumvetsa chikhulupiriro cha abale athu achisilamu.



ROCK International Ikupatsirani

# Mfumu ya Ulemelero

## Kanema

Mawu ndi mawu ofotokozera za Mfumu Ya Ulemerero

*"Kanema ofotokozera zinthu munjira yomwe ndingamvetse."* — Eli, zaka 7

*"Ndinakhudzika ndi nkhani mu moyo wanga onse."* — Lydia, zaka 21

*"Kanema ofotokozera mavumbulutsa akuya munjira yophweka!"* — Dick, zaka 74

Oonetsedwa m'nyumba m'sukulu, magulu ndi malo ena osokhanira anthu.

### Nkhani 1 mu magawo 2 ~ 70
### Gawo la sewero mu ndime 15


**Gawo 1: Chipangano Chakale: Mfumu iyankhula dongosolo lake** ***1 Ora 47 Mphindi***

| | | |
|---|---|---|
| 1. Chiyambi | *Gawo 1-3* | ~ 10:40 |
| 2. Mlengi ndi chilengedwe chake | *Gawo 4-9* | ~ 19:04 |
| 3. Kulowa kwa Zoipa | *Gawo 10-15* | ~ 15:10 |
| 4. Temberero la tchimo ndi lonjezo la Mulungu | *Gawo 16-19* | ~ 11:57 |
| 5. Njira ya nsembe | *Gawo 20-24* | ~ 14:58 |
| 6. Kuukira kwa munthu & kukhulupirika kwa Mulungu | *Gawo 25-27* | ~ 9:05 |
| 7. Ndongosolo la Mulungu lipambana | *Gawo 28-32* | ~ 14:04 |
| 8. Lamulo ndi Aneneri | *Gawo 33-36* | ~ 12:20 |

**Gawo 2: Chpangano chatsopano: Mfumu ikwaniritsa chikonzero** ***1 Ora 55 Mphindi***

| | | |
|---|---|---|
| 9. Kulowa kwa Mfumu | *Gawo 37-42* | ~ 20:16 |
| 10. Khalidwe la Mfumu | *Gawo 43-47* | ~ 15:32 |
| 11. Ulamuliro wa Mfumu | *Gawo 48-51* | ~ 14:02 |
| 12. Cholinga cha Mfumu | *Gawo 52-56* | ~ 15:24 |
| 13. Kuzipereka kwa Mfumu | *Gawo 57-61* | ~ 14:50 |
| 14. Nsembe ndi chipambano cha Mfumu | *Gawo 62-65* | ~ 13:53 |
| 15. Uthenga ndi Ulemero wa Mfumu | *Gawo 66-70* | ~ 18:26 |
| *Mulungu wathu wopambana* (Yoyimbidwa mu Arabic) | *Credits* | ~ 2:45 |


www.king-of-glory.com